2026

APR - JUN



# Zofunikira za Ulosi

Kusanthura Utumiki wa
Uneneri wa Danieli ndi Yohane

# Zirimkatimu


1. Chiyambi cha Ulosi ........ 5
2. Mtumiki wa Mulungu kwa Mafumu ........ 10
3. Maufumu Amtsogolo Avumbulutsidwa ........ 15
4. Masomphenya Oyamba a Danieli ........ 20
5. Mndandanda wa Maufumu ........ 26
6. Masomphenya Afotokozedwa ........ 31
7. Buku Losindikizidwa Litsegulidwanso ........ 36
8. Mneneri Wa Ku Patimosi ........ 41
9. Chinjoka, Nkazi, ndi  Otsala ........ 46
10. Chilombo ndi Chizindikilo ........ 52
11. Angelo Atatu ........ 57
12. Kuyitana Komaliza ........ 62
13. Chimaliziro Chanenedweratu ........ 67


Maphunziro a Baibulo apa Sabata, maphunziro a tsiku ndi tsiku, ndi ochokera mu Baibulo ndi Mzimu wa Chinenero okha basi opanda ndemanga zoonjezera. Mawu a ndemanga za m'baibulo ndi mu Mzimu wa Chinenero ndi achidule oti apeleke mangaliro lofunikira lachidule ndi lachindunji. Zikutiro [ ] zimapelekedwa mu nthawi zina kuti zitsimikize kumveka bwino, nkhani yoyenera, ndi kuwelenga kosalala. Kuphunzira kopitilira kupyolera mu mene mwachokera ndemanga kumalimbikitsidwa kwambiri.

**Zithunzi ndi Chikutiro:** Honduran Union, Rwandan Union Mission, AMAPI, H. Cibalde

Copyright © 2025 by the Seventh Day Adventist Reform General Conference, Chigawo cha Sabata Sukulu, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019, USA. Telefoni: 1-540-362-1800 • Webusaiti: www.sdarm.org • Imelo: info@sdarm.org Kumalawi: SDARM Malawi Mission P.O. Box 200069 Lilongwe 2. Foni: +265 999 701 423, +265 884 288 535

Maphunziro a Baibulo pa Sabata (USPS 005-118), Vol. 101, No. 2, Apulo – Juni 2025. Lofalitsidwa pa kotala ndi Seventh Day Adventist Reform General Conference, chigawo cha Sabata Sukulu Kusindikizidwa, ndi kugawidwa ndi Reformation Herald Publishing Association, 5240 Hollins Road, Roanoke, Virginia 24019–5048, U.S.A. Malipiro anthawi ndi nthawi ku Roanoke, Virginia 24022- 9993.

**U.S.A. ndi Canada**

Lumikizanani: Telefoni 1-540-366-9400 • Webusaiti: www.reformationherald. com • Imelo: info@reformationherald.org Kulembetsa pachaka ku U.S.A.: U.S. $22.00. Kusindikiza kwakukulu $33.00. Mayiko $21.00 kuphatikiza kutumiza. Kusindikiza kwakukulu kwapadziko lonse $31.00 kuphatikiza kutumiza. Kope limodzi $6.00. Kusindikiza kwakukulu $9.00. Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira (mu ndalama zaku U.S. zokha) pa keyala ali pansipa. Mitengo zitha kusintha popanda chidziwitso. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata,

**South Africa**

Lumikizanani: Telefoni & Fax 27-011-336-7064 • Webusaiti: www.sdarm sa.org. za •Imelo: admin@sdarm sa.org.za Kulembetsa kwapachaka mu South Africa: R120-00 (kope limodzi R35-00). Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 7950, Johannesburg 2000, South Africa

**Malawi**

Lumikizanani: Telefoni +26 999 701 423, +265 884 288 535 za•Imelo: sdarmmalawi@yahoo.com Kulembetsa kwapachaka Malawi: MK 2000 (kope limodzi MK 500). Chonde tumizani zopempha zolembetsa ndi zolipira ku adilesi ili pansipa. POSTMASTER, chonde tumizani kusintha maadiresi ku: Maphunziro a Baibulo a Sabata, P. O. Box 20069, Lilongwe 2, Malawi

# Mawu Otsogolera

Baibulo linalembedwa ndipo linasungidwa ndi Mulungu ngati buku louziridwa lotsogolera ife. Nkhani zomwe zili m'bukuli zimapereka maphunziro osawerengeka okhudza miyoyo yathu komanso nthawi yomwe tikukhala. Buku ili la mmene Mulungu amagwirira ntchito kudzera mumbiri ya mitundu ndi ya anthu Ake imatilimbikitsa ndi kutitsimikizira za chikondi Chake. Ndipo umboni wake wamtengo wapatali—mbiri ya moyo ndi uthenga wa Yesu—imadzutsa chikondi cha Mulungu mwa ife, "chifukwa Iye anayamba kutikonda ife" (1 Yohane 4:19).

Chimodzi mwa zinthu zopatsa chidwi za Mulungu wathu zomwe zili m'Baibulo ndi kudziwa zinthu zisadachitike—Iye amatha kuona "chimaliziro kuyambira pachiyambi" (Yesaya 46:10). Izi zimamuthandiza kugwiritsa ntchito mphamvu zake zopanda malire kuchita "zinthu zonse . . . pamodzi kuti zikhale zabwino kwa iwo okonda Mulungu" (Aroma 8:28). Sikuti izi zokha ayi, koma nthawi ndi nthawi amasankha kuulula kwa anthu ake "zinthu zomwe ziyenera kuchitika posachedwa" (Chivumbulutso 1:1). Izi zimatipatsa chidaliro mu chikondi Chake ndi chisamaliro Chake, ndipo ndi chimodzi mwa umboni wa kuuzira kwa Mulungu kwa Baibulo. Chowonadi chakuti ulosi umakwaniritsidwa nthawi zonse m'mbiri ndi zochitika zomwe zikuchitika masiku ano zikusonyeza kuti mawu a Mulungu ndi oposa chipango cha anthu.

Ulosi ndi wofunika kwambiri kwa ana a Mulungu. Madalitso ake aperekedwa kwa "amene awerenga, ndi iwo amene amva mawu a ulosi uwu, nasunga zolembedwa mmenemo" (Chivumbulutso 1:3).

Pakati pa zolemba za aneneri, ziwiri zimaonekera kwambiri ngati zili ndi maulosi atsatanetsatane komanso am'ndanda a mbiri yakale. Danieli ndi Yohane anapatsidwa mauthenga apaderawa, ndipo mabuku awo, Danieli ndi Chivumbulutso, ndiwo nkhani yaikulu ya kotala ino ya *Maphunziro a Baibulo apa Sabata.*

Kwa miyezi itatu ikubwerayi, ophunzira a sukulu ya Sabata adzaphunzira nkhani za Danieli ndi Yohane, ndi zina mwa zigawo zofunika kwambiri za maulosi omwe adalemba. Izi zimayika maziko omvetsetsa uthenga wa Advent ndi magulu auzimu ndi andale akale komanso amakono.

Ngakhale kuti palibe malo okwanira oti afotokozere gawo lililonse la mabuku onse awiri kotala lino, ophunzira akulimbikitsidwa kuphunzira mozama zonse zomwe zili m'mabuku awo, pamodzi ndi kulumikizana kwawo ndi Baibulo lonse.

Chimodzi mwa zinthu zabwino kwambiri zomwe ophunzira ndi aphunzitsi a sukulu ya Sabata angapeze pofuna kumvetsetsa tsatanetsatane wa maulosi awa ndi buku lodziwika bwino lolembedwa ndi Uria Smith, *Thoughts on Daniel and the Revelation.* Tikulimbikitsa kwambiri kuti likhale lokuthandizani pophunzira kotala ino.

Ndi pemphero lathu kuti mudalitsidwe ndi kuphunzira kwanu maulosi awa, pakuti zoonadi "nthawi yayandikira" (Chivumbulutso 1:3).

Department ya Sabata School ya General Conference

# Zopereka za Sabata Loyamba

**Epulo 4, 2026**



**Likulu la Filudi la ku Italy**

Italy, dziko lokongola lomwe lili pakati pa Nyanja ya Mediterranean, ndi lodziwika padziko lonse lapansi chifukwa cha mbiri yake yakale, zaluso zosayerekezeka, zakudya zokongola, ndi malo okongola. Kuwonjezera pa kukhala limodzi mwa malo oyendera alendo padziko lonse lapansi, ndi dziko lofunika kwambiri lopanga mafakitale ndi zaulimi. Ndi anthu oposa 60 miliyoni, Italy imatsimikizira ufulu wachipembedzo kudzera mu Malamulo ake. Komabe, Chikatolika chikadali chipembedzo chofala ndi 74% ya anthu, kutsatiridwa ndi Akristu osakhala Akatolika omwe ali ndi 9.3%, ndi—chifukwa cha kuchuluka kwa anthu osamukira m'dziko muno posachedwapa—Kupezeka kwa Asilamu komwe kukukukulirakulira pakali pano pa 3.6%. Izi zikutsatiridwa ndi zipembedzo zina zazing'ono, komanso kusakhulupirira Mulungu ndi kusakhulupirira kuti kuli Mulungu zikuchulukirachulukira.

Uthenga wa SDA Reform Movement unalalikidwa koyamba ku Italy mu 1926, koma magulu oyamba a Okonzanso zinthu sanakhazikitsidwe mpaka mu 1939/40. Kuyambira m'ma 1990, ndi kufika kwa amishonale ena ochokera ku South America, Portugal kenako Romania, ntchitoyo inakula ndi kukhazikitsidwa kwa magulu ena m'madera osiyanasiyana a dzikolo. Kuyambira nthawi imeneyo, uthengawu walengezedwa mopirira ndipo wakhazikitsidwa m'malo osiyanasiyana m'derali; lerolino tili ndi mamembala oposa 130 omwe agawidwa m'matchalitchi 6, magulu awiri, ndi mamembala apokha.

Pakadali pano tili ndi nyumba imodzi yokha ya tchalitchi, yomwe ili kumpoto chakum'mawa kwa dzikolo, mumzinda wa Trieste. Komabe, tikuwona kufunika kwachangu kwa malo abwino ogwirira ntchito ngati mzati wa mphamvu ndi kukula kwauzimu kwa anthu athu.

Malo awa adzakhala likulu la Filudi - ndipo malo ake ozungulira adzalola abale ambiri kutenga nawo mbali pazochitika zomwe zakonzedwa, monga kuphunzitsa achinyamata amishonale kudzera m'misonkhano, mapulogalamu a nyimbo, mapulojekiti a umishonale ozikika pa misonkhano yazaumoyo, ndi makalasi ophika zakudya kuchekera ku zomera. Tikukhulupirira kuti malowa adzakhala ofunikira kwambiri pakupititsa patsogolo ntchito ya Ambuye ku Italy, kotero tikupempha abale athu, alongo athu, ndi abwenzi athu ochokera padziko lonse lapansi kuti athandizire mowolowa manja ntchitoyi kudzera mu zopereka zawo.

Mwa chisomo cha Yesu komanso ndi mgwirizano wanu, tidzakwaniritsa cholinga ichi, tilimbikitse kulalikira uthenga wabwino m'dziko lino, ndikubweretsa uthenga wa chipulumutso kwa miyoyo yambiri. Ambuye akudalitseni ndikukupatsani mphotho zambiri!

*Abale anu ochokera ku Italy*

LASABATA, EPULO 4, 2026

PHUNZIRO 1

# Chiyambi cha Ulosi

**VERSE LOLOWEZA:** Ndipo tili nawo mawu a chinenero okhazikika koposa;amene muchita bwino powasamalira, monga nyali younikira m'malo a mdima, kufikira kukaca, nikauka nthanda pa mtima yanu''[2 petulo 1:19].

**Zowelenga Zoonjezera:** The Great controversy, pp. 593-602.

'Mbiri ndi ulosi zimaikila umboni kuti Mulungu, mwini wa dziko lonse amavumbulutsa zinsinsi kudzela mwa osakhidwa ake omwe anyamula kuunika ku dziko lonse lapansi.'_ Bible Training School, December 1, 1912.

## 1. MAGANIZO OPANDA MALIRE

**Loyamba, Malitchi, 29**

**a. Ndichani chimene Mulungu yekha amatha kuona? Yesaya 46:9,10**

___

___

___

'INE NDILI, kumatanthauza kukhalapo kwamuyaya; zakale, zapano ndi zamtsogolo zili chimodzimodzi kwa Mulungu. Iye amaona zimene zinachitika kale ndizatsogolo lakutali lomwe ndi masomphenya ooneka bwino ngati momwe tikuonera zinthu zomwe zikuchitika tsiku ndi tsiku.'_ The SDA Bible Commentary [E.G. White Comments], vol. 1, p. 1099.

**b. Kodi Mulungu wathu amatani ndi chidziwitso ichi? Danieli 2:20-22.**

___

___

'Pamwamba pa zisokonezo zonse za padziko lapansi, Mulungu wakhala pa mpando wachifumu; zinthu zonse zili poyera pamaso pake pa Mulungu ndikuchokera ku umuyaya wake waukulu ndi wodekha. Amalamula zomwe uphungu wake ukuona bwino.'_ The Ministry of Healing, p. 417.

'Mzolemba za mbiri ya anthu, kukula kwa mitundu, kukwera ndi kugwa kwa maufumu, zikuoneka ngat zidalira chifuniro ndi mphamvu za munthu. Kuumbika kwa zochitika zikuoneka pamlingo waukulu kuti kumatsimikiziridwa ndi mphamvu zake, chikhumbo chake kapena kusakhazikika kwa maganizo ake. Koma m'mwawu ake a Mulungu, chinsalu chimapatulidwa ndipo tiona pamwamba, kumbuyo ndi kupyola masewelo onse ndi kusithana kwa zokonda za anthu ndi mphamvu ndi zilakolako, ntchito za wachifundo chonse, akugwira nchito mwakachetechete, ,oleza mtima kukwaniritsa malangizo za chifuniro chake.'_ Prphets and Kings, pp. 449,500.

**a. Kodi Mulungu amachita chiyani akafuna kukwaniritsa chifuniro Chake pa dziko lapansi? Amosi 3:7; Chivumbulutso 1:1.**

______________________________________________

______________________________________________

‘Ambuye Yehova sachita kanthu kopanda kuulula chinsinsi chake kwa atumiki ake, aneneri.’ Pamene ‘zinthu zobisika nza Yehova Mulungu wathu,’ ‘koma zinthu zowululidwa nza ife ndi ana athu mpaka kalekale.’ Amosi 3:7; Deuteronomo 29:29. Mulungu watipatsa zinthu izi, ndipo dalitso lake lidzatsagana ndi kuphunzira mwaulemu ndi mwa pemphero Malemba a uneneri.” — The Desire of Ages, p. 234.

**b. N’chifukwa chiyani Mulungu amatitumizira mauthenga otere? 1 Yohane 3:1; Yohane 1:12; Akolose 1:25–28.**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

“Baibulo ndi buku lodabwitsa. Ndi mbiri yomwe imatitsegulira zaka zakale. Popanda Baibulo, tikadangosiyidwa ndi malingaliro ndi nthano zokhudza zimene zinachitika m’nthawi zakale. Ndi uneneri womwe umavumbulutsa tsogolo. Ndi mawu a Mulungu omwe amatsegula kwa ife dongosolo la chipulumutso, kusonyeza njira imene tingapulumukire imfa yosatha ndi kulandira moyo wosatha. Ngakhale pali mabuku ambiri padziko lapansi, ngakhale ena ali ofunika, Baibulo ndi buku la mabuku, loyenera kwambiri kuphunziridwa ndi kuyamikiridwa. Limatipatsa osati mbiri ya dziko lino kokha, komanso kufotokoza za dziko lomwe likudza. Lili ndi malangizo okhudza zodabwitsa za chilengedwe, ndipo limavumbulutsa kwa ife khalidwe la Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi. M’menemo muli vumbulutso la Mulungu kwa munthu.” — The Signs of the Times, Januwale 30, 1893.

**c. Ndi chidziwitso chofunika kwambiri chiti chimene tiyenera kufunafuna? Yeremiya 9:23, 24; Yohane 17:3; Aefeso 3:17–19.**

______________________________________________

______________________________________________

“M’mawu a Mulungu, maganizo amapeza nkhani zokomera kuganiza mozama kwambiri ndi zolinga zapamwamba kwambiri. Pano tingakhale ndi ubwenzi ndi makolo ndi aneneri, ndikumva mawu a Wamuyaya akulankhula ndi anthu. Pano timaona Ulemerero wa kumwamba pamene Iye anadzichepetsa kukhala M’malo mwathu ndi Chitsimikizo chathu kuti alimbane yekhayekha ndi mphamvu za mdima ndi kupambana m’malo mwathu. Kugonera mwaulemu pa mitu yotere sikungalephere kufewetsa, kuyeretsa, ndi kukweza mtima, komanso kulimbikitsa maganizo ndi mphamvu zatsopano.” — Testimonies for the Church, vol. 5, p. 25.

**a. Kodi tikufunika chithandizo chotani kuti timvetse Malemba, kuphatikizapo uneneri? Yohane 16:7–13.**

___

"Mulungu akufuna kuti, ngakhale m'moyo uno, choonadi chizipitiriza kuvumbulutsidwa kwa anthu Ake. Pali njira imodzi yokha imene chidziwitsochi chingapezeke. Tingathe kumvetsa mawu a Mulungu kudzera mu kuunikira kwa Mzimu amene mawuwo anaperekedwa kudzera mwa Iye." — Testimonies for the Church, vol. 5, P 703.

"Baibulo siliyenera kuphunziridwa popanda pemphero. Tisanatsegule masamba ake, tiyenera kupempha kuunikira kwa Mzimu Woyera, ndipo kudzaperekedwa. Pamene Nataniyeli anabwera kwa Yesu, Mpulumutsi anati, 'Onani, Mwisrayeli weniweni, mwa iye mulibe chinyengo!' Nataniyeli anati, 'Munandidziwa bwanji?' Yesu anayankha, 'Filipo asanakuitane, uli pansi pa mtengo wa mkuyu, ndinakuona.' Yohane 1:47, 48. Ndipo Yesu adzationanso m'malo obisika a pemphero ngati tifuna kuwala kuti tidziwe choonadi. Angelo ochokera kudziko la kuwala adzakhala pamodzi ndi iwo amene, mwa kudzichepetsa kwa mtima, akufuna chitsogozo chaumulungu." — Steps to Christ, P 91.

**b. N'chifukwa chiyani n'kofunika kuti tisamangotsatira maganizo athu okha pamene tikuphunzira uneneri? 2 Petro 1:19–21.**

___

___

"Pamene mukuphunzira mawu a Mulungu, siyani kunja maganizo anu amene munakonzeratu komanso malingaliro amene munalandira kuchokera ku makolo kapena amene munazolowera. Simudzafika pa choonadi ngati mukuphunzira Malemba kuti mutsimikizire maganizo anu. Asiyeni kunja, ndipo ndi mtima wolapa lowani kuti mumve zimene Ambuye akunena kwa inu. Pamene wofufuza choonadi mwa kudzichepetsa akukhala pa mapazi a Khristu ndi kuphunzira kwa Iye, mawu amapereka kumvetsa. Kwa iwo amene amadziona anzeru kwambiri moti safuna kuphunzira Baibulo, Khristu akuti, Muyenera kukhala ofatsa ndi odzichepetsa mumtima ngati mukufuna kukhala anzeru za chipulumutso.

Musawerenge mawu a Mulungu m'kuwala kwa maganizo anu akale; koma, ndi maganizo opanda tsankho, mufufuze mosamala ndi mwa pemphero. Ngati, pamene mukuwerenga, mukumva kutsutsidwa ndipo muona kuti maganizo anu okondedwa sakugwirizana ndi mawu a Mulungu, musayese kusintha mawu kuti agwirizane ndi maganizo anu. Sinthani maganizo anu kuti agwirizane ndi mawu. Musalole zimene munakhulupirira kapena kuchita kale zitsogolere kumvetsa kwanu. Tsegulani maso a maganizo anu kuti muone zodabwitsa m'chilamulo. Pezani chimene chalembedwa, kenaka limbikitsani mapazi anu pa Thanthwe losatha."-Messages to young people,p.260.

**a. Kodi Mulungu amapereka bwanji mawu Ake, ndipo tiyenera kuwaphunzira motani? Yesaya 28:9, 10.**

"Umboni wa choonadi cha mawu a Mulungu uli m'mawuwo enieni. Malemba ndi kiyi wotsegula Malemba. Tanthauzo lozama la choonadi cha mawu a Mulungu limavumbulutsidwa m'mitima yathu kudzera mwa Mzimu Wake." — 8 T, p. 157.

"Palibe amene ali ndi mtima woyamikira chiphunzitso chake angawerenge gawo limodzi la Baibulo osapeza lingaliro lothandiza. Koma chiphunzitso chamtengo wapatali kwambiri cha Baibulo sichipezeka mwa kuphunzira mwachisawawa kapena mosalumikizana. Dongosolo lake lalikulu la choonadi silinaperekedwe moti lingamveke kwa wowerenga mwachangu kapena wosasamala. Chuma chake chochuluka chili pansi pa pamwamba, ndipo chimapezeka kokha mwa kufufuza mosamala ndi kulimbikira kosalekeza. Choonadi chimene chimapanga chithunzithunzi chachikulu chiyenera kufufuzidwa ndi kusonkhanitsidwa, 'pano pang'ono, aposo pang'ono.' Yesaya 28:10.

Choonadi chikafufuzidwa motere ndi kusonkhanitsidwa pamodzi, chimapezeka kuti chikugwirizana bwino kwambiri. Uthenga uliwonse wa Uthenga Wabwino umawonjezera pa wina, uneneri uliwonse ukufotokoza wina, choonadi chilichonse chimakulitsa china. Zizindikiro za dongosolo la Ayuda zimamveka bwino kudzera mu Uthenga Wabwino. Mfundo iliyonse m'mawu a Mulungu ili ndi malo ake, ndipo chochitika chilichonse chili ndi tanthauzo lake. Ndipo dongosolo lonse, m'kapangidwe ndi m'kuchitidwa kwake, limachitira umboni Mlengi wake. Dongosolo lotere silikanatheka kuganiziridwa kapena kupangidwa ndi maganizo ena kupatula a Wosatha." — Education, pp. 123, 124.

**b. N'chifukwa chiyani gawo lililonse la Baibulo n'lofunika? Mateyu 4:4; Luka 24:27.**

Sitingatenge umboni wa munthu aliyense pa zimene Malemba amaphunzitsa, koma tiyenera kuphunzira mawu a Mulungu tokha. . . . Maganizo adzakula ngati agwiritsidwa ntchito kufufuza ubale wa mitu ya m'Baibulo, kuyerekezera malemba ndi malemba ndi zinthu zauzimu ndi zauzimu. . . .

Sitingapeze nzeru popanda khama ndi kuphunzira mwa pemphero. Zigawo zina za Malemba n'zosavuta kumvetsa, koma zina tanthauzo lake silioneka pamwamba kuti liwoneke mwamsanga. Malemba ayenera kuyerekezera ndi Malemba. Payenera kukhala kufufuza mosamala ndi kuganiza mwa pemphero. Kuphunzira kotere kudzabwezera mopambana. Monga mmene wofukula miyala amapezera mitsempha ya chitsulo chamtengo wapatali yobisika pansi pa nthaka, momwemonso amene amafufuza mawu a Mulungu mosaleka ngati chuma chobisika adzapeza choonadi chamtengo wapatali kwambiri, chimene chabisika kwa wofufuza wosasamala. Mawu a kudzozedwa, akaganiziridwa m'mtima, adzakhala ngati mitsinje yochokera ku Kasupe wa moyo." — Steps to Christ, pp. 89–91.

## 5. KUPHUNZIRA NDI NZERU

**Lachisanu, Epulo 2**

**a. Kodi maganizo athu ndi zosankha zathu zimakhudza bwanji luso lathu lozindikira tanthauzo la mauneneri? Danieli 12:10; 2 Timoteyo 3:1–8.**

“Mzimu umene mumabwera nawo pofufuza Malemba udzatsimikizira khalidwe la mthandizi amene adzakhala pambali panu. Angelo ochokera kudziko la kuwala adzakhala pamodzi ndi iwo amene, mwa kudzichepetsa kwa mtima, amafuna chitsogozo chaumulungu. Koma ngati Baibulo litsegulidwa mopanda ulemu, ndi mtima wodzidalira, ndipo mtima uli wodzaza ndi tsankho, Satana amakhala pambali panu, ndipo adzaika mawu omveka bwino a Mulungu m’kuwala kosokoneza.” — TM, p. 108.

“Satana wapangitsa ambiri kukhulupirira kuti zigawo za uneneri m’zimene analemba Danieli ndi Yohane Muvumbulutsi sizingamveke. Koma lonjezo liri lomveka bwino kuti dalitso lapadera lidzatsagana ndi kuphunzira kwa mauneneri amenewa — Prophets and Kings, p. 547.

**b. Fotokozani kufunika kogwiritsa ntchito choonadi payekha. Chivumbulutso 22:7; Mateyu 7:24–27; Yohane 7:17.**

---

“Ofatsa amatsogoleredwa ndi Ambuye, chifukwa ndi ophunzitsika, ofunitsitsa kuphunzitsidwa. Ali ndi chilakolako chenicheni chodziwa ndi kuchita chifuniro cha Mulungu. Lonjezo la Mpulumutsi ndi ili, ‘Ngati munthu afuna kuchita chifuniro Chake, adzadziwa za chiphunzitsocho.’ Yohane 7:17. Ndipo kudzera mwa mtumwi Yakobo Iye akuti, ‘Ngati wina mwa inu asowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene amapatsa onse mowolowa manja, osanyoza; ndipo adzamupatsa.’ Yakobo 1:5. Koma lonjezo Lake ndi la iwo okha amene ali ofunitsitsa kutsatira Ambuye mokwanira.” — Patriarchs and Prophets, p. 384.

“Ngati mukufuna kudziwa chinsinsi cha chipembedzo, muyenera kutsatira mawu omveka bwino a choonadi — mukhale ndi kumva kapena opanda kumva, ndi chisangalalo kapena opanda chisangalalo. Kumvera kuyenera kuchitidwa chifukwa cha mfundo, ndipo choyenera chiyenera kutsatiridwa m’mikhalidwe yonse.” — Fundamentals of Christian Education,p. 125.

## MAFUNSO OYANKHA PAWEKHA

**Lachisanu n’chimodzi, Epulo 3**

1. Pankhani ya chidziwitso, kodi Mulungu amadzipatula bwanji ndi zolengedwa zina zonse?
2. Kodi Mulungu amativumbulutsira chani m’zolemba za aneneri, n’chifukwa chani?
3. Tikamatsegula Mawu a Mulungu, kodi tiyenera kupempherera chithandizo chotani?
4. Ndi khama lotani limene ndiyenera kukhala wokonzeka kuyika mu kuphunzira Baibulo?
5. Kodi ndili wokonzeka kugwiritsa ntchito zimene ndapeza m’mawu a Mulungu?

# Mtumiki wa Mulungu kwa Mafumu

**VESI LOLOWEZA:** “Koma anyamata amene anai, Mulungu anawapatsa chidziwitso ndi luntha la m’mabuku monse ali onse, ndinzeru; koma Danieli anali nalo luntha la masomphenya ndi maloto onse” (Danieli 1:17).

**Zowelenga Zoonjezera:** Prophets and Kings, pp. 479–490.

“Moyo wa Danieli ndi anzake aja ndi chisonyezo cha zimene Iye adzachitira iwo amene adzipereka kwa Iye ndipo ndi mtima wonse amayesetsa kukwaniritsa cholinga Chake.”—Prophets and Kings, p. 490.

## 1. ANDENDE MU BABULONI — Loyamba, Epulo 5

**a. Kodi Danieli anafika bwanji ku Babulo? Danieli 1:1–7.**

________________________________________

________________________________________

**b. Kodi chinatsatira ndi chiyani ku chisankho cha Daniel chokhudza kudya pa gome la mfumu? Danieli 1:8–16.**

________________________________________

________________________________________

“Gawo litaperekedwa ku mafano, chakudya chochokera pagome la mfumu chimapatulidwa ku kulambira mafano; ndipo munthu wodya nawo anayenerakuonedwa ngati akupereka ulemu kwa milungu ya ku Babulo. Pa kulambira koteroko, kukhulupirika kwa Yehova kunaletsa Danieli ndi anzake kuti asatenge nawo gawo. . . .

“Ndipo sanayerekeze kuika pachiwopsezo zotsatira za moyo wapamwamba ndi kusadziletsa pa chitukuko chakuthupi, chamaganizo, ndi chauzimu.”—Prophets and Kings, pp. 481, 482.

“Pamene Danieli ndi anzake anayesedwa, anadziika okha kumbali ya chilungamo ndi choonadi. Sanayende modzidzimutsa, koma mwanzeru. Iwo anaganiza kuti popeza nyama ya nyama sinali chakudya chawo m'mbuyomu, komanso sichiyenera kulowa mu chakudya chawo mtsogolo. Ndipo popeza kugwiritsa ntchito vinyo kunali koletsedwa kwa onse omwe ayenera kuchita utumiki wa Mulungu, anatsimikiza mtima kuti sadzadya nawo.”—In Heavenly Places, p. 261.

**c. Fotokozani kuyesera ndi kufufuza kwa mfumu. Danieli 1:17–21.**

________________________________________

________________________________________

**a. Pansi pa chiopsyezo cha imfa, kodi Ahebri anayesedwa bwanji pankhani ya kukhulupirika ku lamulo lachiwiri? Danieli 3:1–15.**

---

"Si onse amene anagwadira chizindikiro cha mafano cha mphamvu ya umunthu. Pakati pa khamu la anthu olambira panali amuna atatu omwe anali otsimikiza mtima kuti asanyoze Mulungu wakumwamba. Mulungu wawo anali Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye; sakanagwadira wina aliyense kapena chinachilichonse."— Prophets and Kings, p. 506.

**b. Kodi iwo anakwanitsa bwanji kusunga chikhulupiriro chawo ndi kumvera kwawo? Danieli 3:16–18; Yesaya 43:1, 2.**

---

"Ziwopsezo za mfumu zinali zopanda pake. Sanathe kutembenuza anthu kuchoka pa kukhulupirika kwawo kwa Wolamulira wa chilengedwe chonse. Kuchokera m'mbiri ya makolo awo anaphunzira kuti kusamvera Mulungu kumabweretsa manyazi, tsoka, ndi imfa; ndi kuti kuopa Ambuye ndiye chiyambi cha nzeru, maziko a chitukuko chenicheni. Atayang'ana ng'anjo modekha, anati, 'O Nebukadinezara, sitikusamala kuyankha pankhaniyi. Ngati zili choncho [ngati ichi ndi chisankho chanu], Mulungu wathu amene timamutumikira akhoza kutipulumutsa ku ng'anjo yotentha yamoto, ndipo Iye adzatipulumutsa m'dzanja lanu, inu mfumu.' Chikhulupiriro chawo chinalimba pamene analengeza kuti Mulungu adzalemekezedwa mwa kuwapulumutsa, ndipo ndi chitsimikizo chopambana chochokera ku chidaliro chonse mwa Mulungu, anawonjezera kuti, 'Koma ngati sichoncho, dziwani, inu mfumu, kuti sitidzatumikira milungu yanu, kapena kulambira fano lagolide limene mudaliimika.' "— Ibid., pp. 507, 508

**c. Kodi Mulungu analemekezedwa bwanji mu chipulumutso chawo? Danieli 3:19, 20, 24–28.**

---

---

"Mfumu inayang'ana kuchokera pampando wake wachifumu, ikuyembekezera kuona anthu amene anatsutsa mfumuyo akuwonongedwa kotheratu. Koma malingaliro ake a chipambano anasintha mwadzidzidzi. . . Mumawonekedwe a munthu wachinayi pakati pa moto, mfumuyo inazindikira Mwana wa Mulungu. . . .

"Ndipo tsopano, ukulu ndi ulemu wake zitayiwalika, Nebukadinezara anatsika pampando wake wachifumu. . . .

"Kenako Sadrake, Mesake, ndi Abedinego anatuluka naima pamaso pa khamu lalikulu, kudzionetsera okha osavulazidwa. . . . Choiwalika chinali chifaniziro chachikulu chagolide, choyikidwa ndi mwano waukulu, chinaiwalika. Pamaso pa Mulungu wamoyo, anthu anachita mantha ndi kunjenjemera.—Ibid., pp. 509, 510.

**a. Kodi Mulungu analankhula bwanji ndi mfumu Nebukadinezara? Danieli 4:4–7**

___

"N'zosadabwitsa kuti mfumu yopambanayi, yodzikuza komanso yodzimva kwambiri, iyenera kuyesedwa kuti ipatuke panjira ya kudzichepetsa, yomwe yokhayo ndiyo imatsogolera ku ukulu weniweni. . . . Mulungu mwachifundo anapatsa mfumu loto lina, kuti amuchenjeze za choopsa chake ndi za msampha umene unayikidwa kuti chiononongeko chake."— Prophets and Kings, p. 515.

**b. Pamene Danieli anaitanidwa kuti amasulire loto, kodi uphungu wake unali wotani kwa mfumu? Danieli 4:20–27**

___

"Kwa Danieli tanthauzo la lotolo linali lachindunji, ndipo tanthauzo lake linamudabwitsa. . . . Mneneriyo anazindikira kuti Mulungu anaika pa iye udindo waukulu wovumbulutsira Nebukadinezara chiweruzo chomwe chinali pafupi kumugwera chifukwa cha kunyada kwake ndi kudzikuza kwake."— Ibid., p. 517.

"Atamasulira lotolo mokhulupirika, Danieli analimbikitsa mfumu yodzikuzayo kuti ilape ndi kutembenukira kwa Mulungu, kuti mwa kuchita zabwino athe kupewa tsoka lomwe linkaopsezedwa pa Iye."—Ibid., p. 518.

**c. Pokakamizidwa kuphunzira kudzera mu chokumana nacho chovuta komanso chamanyazi, kodi mfumuyo inatsogoleredwa bwanji kulemekeza Mulungu kudzera mu utumiki wa Danieli? Danieli 4:34–37.**

___

"Kwa zaka zisanu ndi ziwiri Nebukadinezara anali wodabwitsa kwa anthu ake onse; kwa zaka zisanu ndi ziwiri iye anachepetsedwa pamaso pa dziko lonse lapansi. Kenako nzeru zake zinabwezeretsedwa ndipo, poyang'ana mmwamba modzichepetsa kwa Mulungu wakumwamba, anazindikira dzanja la Mulungu m'kulangidwa kwake. Mu chilengezo cha poyera, Iye anavomereza kulakwa kwake ndi chifundo chachikulu cha Mulungu m'kubwezeretsedwa kwake. . . .

"Mfumu yomwe kale inali yodzikuza inakhala mwana wodzichepetsa wa Mulungu; wolamulira wankhanza, wopondereza, anakhala mfumu yanzeru komanso yachifundo. Iye amene atsutsa ndi kunyoza Mulungu wakumwamba, tsopano anavomereza mphamvu ya Wam'mwambamwamba ndipo anayesetsa mwakhama kulimbikitsa kuopa Yehova ndi chisangalalo cha anthu ake. . . .

"Cholinga cha Mulungu chakuti ufumu waukulu kwambiri padziko lonse lapansi upereke chitamando Chake tsopano chakwaniritsidwa. Chilengezo ichi cha poyera, chomwe Nebukadinezara anavomereza chifundo ndi ubwino ndi ulamuliro wa Mulungu, chinali chochita chomaliza cha moyo wake cholembedwa m'mbiri yopatulika."—Ibid., pp. 520, 521.

**a. Ndi chochitika chotani chonga sewero chomwe chinaimitsa mwadzidzidzi Belisazara, mbadwa ya Nebukadinezara, mukunyoza Mulungu wakumwamba? Danieli 5:1-6.**

---

---

"Ataloledwa ali mnyamata kukhala ndi ulamuliro waufumu, Belisazara anadzitamandira ndi mphamvu zake ndipo anadzikweza mumtima wake motsutsana ndi Mulungu wakumwamba. Iye anali ndi mipataya yambiri yodziwa chifuniro cha Mulungu ndi kumvetsetsa udindo wake womvera Mulungu. Iye anali atadziwa za kuchotsedwa kwa agogo ake aamuna, mwa lamulo la Mulungu, kuchokera pakati pa anthu; ndipo ankadziwa za kutembenuka kwa Nebukadinezara ndi kubwezeretsedwa kozizwitsa. Koma Belisazara analola chikondi cha chisangalalo ndi kudzilemekeza kuti zichotse maphunziro omwe sanayenera kuwaiwala."—Prophets and Kings, pp. 522, 523.

**b. Kodi Danieli anabweretsedwanso bwanji kuti akapereke uthenga wa Mulungu kwa mfumu yachikunjayi? Danieli 5:8–16.**

---

"Choyamba mneneriyo anakumbutsa Belisazara za nkhani zomwe ankazidziwa bwino, koma zomwe sizinamuphunzitse phunziro la kudzichepetsa lomwe likanamupulumutsa iye. Iye analankhula za uchimo wa Nebukadinezara ndi kugwa kwake, ndi za machitidwe a Mulungu kwa iye—ulamuliro ndi ulemerero zomwe zinapelekedwa kwa iye, chiweruzo cha Mulungu chifukwa cha kunyada kwake, ndi kuvomereza kwake mphamvu ndi chifundo cha Mulungu wa Israyeli; kenako m'mawu olimba mtima komanso otsimikiza anadzudzula Belisazara chifukwa cha kuipa kwake kwakukulu."— Ibid., p. 529

**c. Kodi kutanthauzira kwa Danieli kunakwaniritsidwa bwanji usiku umenewo? Danieli 5:17, 25–31.**

---

---

"Adakali m'nyumba yachikondwerero, atazunguliridwa ndi anthu omwe tsoka lawo latsimikizika, mfumu inauzidwa ndi mthenga kuti 'mzinda wake wagwidwa' ndi mdani amene ankadzimva kuti ku ziwembu za mdaniyi iye anali otetezeka kwambiri. . . . Ngakhale pamene iye ndi akuluakulu ake anali kumwa kuchokera m'ziwiya zopatulika za Yehova, ndi kutamanda milungu yawo yasiliva ndi yagolide, Amedi ndi Aperisi, atatulutsa Mtsinje wa Firate m'ngalande yake, anali kuyenda kupita pakati pa mzinda wosatetezedwawu. Gulu lankhondo la Koresi tsopano linaima pansi pa makoma a nyumba yachifumu; mzindawu unali wodzaza ndi asilikali a adani, 'ngati mbozi' (vesi 14); ndipo kufuula kwawo kopambana kunamveka pamwamba pa kulira komvetsa chisoni kwa osangalala odabwa."—Ibid., p. 531.

## 5. MU DZENJE LA MIKANGO

**Lachisanu, Epulo 9**

a. **N'chifukwa chiyani kukhulupirika kwa Danieli kwa Mulungu kunabweretsa chizunzo? Danieli 6:1–5.**

"Ulemu umene Danieli anapatsidwa unayambitsa nsanje kwa akuluakulu a ufumuwo, ndipo iwo anafunafuna chifukwa chomudandaula. . . . "Khalidwe la Danieli lopanda chilema linawonjezera nsanje ya adani ake. . . . "Pamenepo apulezidenti ndi akalonga, akupangana uphungu, nakonza chiwembu chomwe ankayembekezera kukwaniritsa kuwononga mneneriyo."—Prophets and Kings, pp. 539, 540

b. **N'chiyani chinachitika chifukwa cha kukana kwa Danieli kugwedezeka? Danieli 6:11–17.**

"Ngakhale ankadziwa bwino zotsatira za kukhulupirika kwake kwa Mulungu, mzimu wake sunagwedezeke. Pamaso pa omwe ankakonza chiwembu chake chomuwononga, sanalole kuti ziwoneke ngati kuti ubale wake ndi Kumwamba watha. Nthawi zonse pamene mfumu inali ndi ufulu wolamula, Danieli ankamvera; koma mfumu kapena lamulo lake silikanamupangitsa kusiya kumvera Mfumu ya mafumu."—Ibid., p. 542.

c. **Kodi Mulungu analemekezedwanso bwanji kudzera mwa mtumiki wake? Danieli 6:19–23, 27.**

"Mulungu sanaletse adani a Danieli kuti asamuponye m'dzenje la mikango; Iye analola angelo oipa ndi anthu oipa kufikira pamenepo kuti akwaniritse cholinga chawo; koma chinali chakuti apangitse chipulumutso cha mtumiki wake kukhala chodziwika bwino, ndi kugonjetsedwa kwa adani a choonadi ndi chilungamo kukhala kodzadza. 'Ndithudi mkwiyo wa munthu udzakutamandani' (Masalmo 76:10), woimba masalmo wachitira umboni. Kudzera mu kulimba mtima kwa munthu mmodzi uyu amene anasankha kutsatira zoyenera m'malo mwa Mfundo zokhazikitsidwa, Satana anayenera kugonjetsedwa, ndipo dzina la Mulungu linayenera kukwezedwa ndi kulemekezedwa."—Ibid., pp. 543, 544.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu n'chimodzi, Epulo 10**

1. Kodi tingatsanzire bwanji zisankho zanzeru za Ahebri anayi masiku ano?
2. Kodi kukumana ndi mayesero kungatipangitse bwanji kukhala olimba ndikutsegula chitseko cha umboni ku dziko lapansi?
3. Kodi ndi maphunziro ati omwe Mfumu Nebukadinezara adaphunzira omwe adamupangitsa kuti atembenuke?
4. Kodi atsogoleri a masiku ano angaphunzire chiyani kuchokera ku usiku womaliza wa Belisazara ku Babulo?
5. Kodi nkhani ya Danieli ingalimbikitse bwanji anthu a Mulungu omwe akukumana ndi chizunzo?

# Maufumu Amtsogolo Avumbulutsidwa

**VESI LOLOWEZA:** "Pakuti amasanduliza nthawi ndi nyengo, achotsa mafumu, nalonga mafumu, apatsa anzeru nzeru, ndi chidziwitso kwa iwo okhoza kuzindikira." (Danieli 2:21).

**Zowerenga Zoonjezera:** Prophets and Kings, pp. 491–502.

"Mphamvu za mayiko, monga za dziko lililonse palokha, siipezeka mu mwayi kapena zinthu zomwe zimaoneka kuti zimawapangitsa kukhala osagonjetseka; siipezeka mu kudzitamandira mu ukulu. Zimayesedwa kudzera mu kukhulupirika komwe amakwaniritsa nako cholinga cha Mulungu."—Prophets and Kings, p. 502.

## 1. LOTO LOPATSA CHIDWI — Loyamba, Epulo 12

**a. Kodi mfumu Nebukadinezara analamula chiyani atadzuka ku loto losautsa? Danieli 2:1, 2.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

**b. Kodi aphungu a mfumu anayankha bwanji pempho lake lachilendo? Danieli 2:3–7.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

"Mfumu inadziwa kuti ngati iwo akanatha kufotokoza tanthauzo la loto lake, iwo akanathanso kufotokoza lotolo. Mulungu, mwa mu chisamaliro Chake, anapatsa Nebukadinezara lotoli, ndipo anachititsa kuti lotoli liiwalike, pamene chikoka chake chopatsa mantha chinatsalabe m'maganizo mwake, kuti avumbulutse mabodza a amuna anzeru a ku Babulo."—The Sanctified Life, p. 34.

**c. Posatengera kuti ankati amalumikirizana ndi dziko la mizimu komanso moyo wa patsogolo pa imfa, kodi n'chiyani chimene amuna anzeru a ku Babulowa anavomereza? Danieli 2:8–11.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

"Podzala ndi mantha chifukwa cha zotsatira za kulephera kwawo, amatsenga anayesa kusonyeza mfumu kuti pempho lake linali lopanda nzeru komanso mayeso ake anali oposa omwe munthu aliyense angafunsidwe."—Prophets and Kings, p. 492.

**a. Kodi mfumu inachita chiyani pamene amatsenga aja analephera kuulula ndi kumasulira loto lake, ndipo ndimotani mmene Danieli anakhudzidwira muchochitikacho? Danieli 2:12–16.**

---

"Pakati pa anthu amene ankafunidwa ndi nthumwi za mfumu omwe anali kukonzekera kukwaniritsa zomwe lamulo la mfumu linanena, panali Danieli ndi anzake. Atauzidwa kuti malinga ndi lamulolo, iwonso ayenera kufa, 'ndi uphungu ndi nzeru' Danieli anafunsa Arioki, kapitawo wa alonda a mfumu, 'Chifukwa chiyani lamuloli latuluka mwachangu chonchi kuchokera kwa mfumu?' Arioki anamuuza nkhani ya kusautsika kwa mfumu chifukwa cha loto lake lodabwitsa, komanso kulephera kwake kupeza thandizo kwa anthu omwe anali kuwadalira kwambiri. Atamva izi, Danieli, atatenga moyo wake m'manja mwake, anapita kwa mfumu ndikupempha kuti amupatse nthawi, kuti apemphe Mulungu wake kuti amuululire lotoli ndi tanthauzo lake.

"Ku pempho limeneli mfumu inavomereza. 'Pamenepo Danieli anapita kunyumba kwake, nadziwitsa nkhaniyi Hananiya, Misaeli, ndi Azariya anzake aja.' Onse pamodzi anafunafuna nzeru kuchokera ku Gwero la kuunika ndi chidziwitso. Chikhulupiriro chawo chinali cholimba podziwa kuti Mulungu anawaika pamalo omwe anali, kuti anali kuchita ntchito Yake ndikukwaniritsa zofunikira za udindo wawo."—Prophets and Kings, p. 493.

**b. Ndi chiyani chomwe tingaphunzirepo kuchokera ku momwe Danieli ndi anzake anapempherera pa nthawi iyi? Danieli 2:17–23.**

---

---

"Mu nthawi zovuta ndi zoopsa [Danieli ndi anzake] ankatembenukira kwa [Mulungu] kuti awatsogolere ndi kuwateteza, ndipo Iye anatsimikizira kukhala thandizo lopezekeratu nthawi zonse. Tsopano ndi mtima wolapa anadziperekanso mwatsopano kwa Woweruza wa dziko lapansi, kumupempha kuti awapulumutse mu nthawi yawo ya chosowa chachikulu. Ndipo sanapemphe kwa chabe. Mulungu amene anamulemekeza, tsopano anawalemekeza iwo. Mzimu wa Ambuye unakhala pa iwo, ndipo kwa Danieli, 'm'masomphenya a usiku,' linavumbulutsidwa loto la mfumu ndi tanthauzo lake ."—Ibid, pp. 493, 494.

"[Ahebri anayi aja] sanapemphe chifundo cha Mulungu kwa chabe. Ndipo Danieli anayitana anzake aja, nayamika Mulungu kuti mapemphero awo anamvedwa ndi kuyankhidwa, ndipo anapereka kwa Mulungu nsembe yotamanda ndi yoyamikira, yomwe inali yovomerezeka kwathunthu kwa Wolamulira wa chilengedwe chonse. [kuchokera pa Danieli 2:20–22]. Danieli ndi anzake anali ndi msonkhano woyamika, ndipo chilengedwe chonse chakumwamba chinagwirizana nawo poyamika."— The Youth's Instructor, November 22, 1894.

**a. Kodi Danieli anafotokozera motani Nebukadinezara za kubvumbulutsidwa kwa loto lake? Danieli 2:24–30.**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

“Taonani kapolo wa chi Yudayu, odekha komanso odzigwira, pamaso pa mfumu ya ufumu wamphamvu kwambiri padziko lonse lapansi. M’mawu ake oyamba, anakana ulemu wakwa iye mwini ndipo anakweza Mulungu monga gwero la nzeru zonse. Pofunsa mfumu modabwa, ‘Kodi ungathe kundidziwitsa loto limene ndinalota, ndi tanthauzo lake?’ Iye anayankha kuti: ‘Chinsinsi chimene mfumu ikufuna kumva anzeru, openduza, amatsenga, alauli sangathe kuululira mfumu, koma kuli Mulungu kumwamba amene amavumbulutsa zinsinsi, nadziwitsa mfumu Nebukadinezara zimene zidzachitika m’masiku otsiriza.’ ”—Prophets and Kings, pp. 494–497.

“Kapolo wa Chiyuda anaima pamaso pa mfumu ya ufumu wamphamvu kwambiri womwe dzuwa linawalirapo. Posawelengera chuma ndi ulemerero, Nebukadinezara anali ndi nkhawa kwambiri, koma kapolo wachinyamatayo anali wodekha komanso wosangalala mwa Mulungu wake. Ndiye, ngati kunali kotheka, unali mwayi wakuti Danieli adzikweze—kuti aonetse ubwino wake ndi nzeru zake zapamwamba. Koma kuyesayesa kwake koyamba kunali kudzichotsera ulemu wonse, ndi kutamanda Mulungu monga Gwero la nzeru.”—The Youth's Instructor, September 1, 1903.

**b. Fotokozani fano limene mfumu inaliwona m'maloto ake. Danieli 2:31–33.**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

“Atamvetsera mosamala pamene chilichonse chinkabwerezedwanso, mfumu inazindikira kuti ili ndi loto limene linamuvutitsa kwambiri; ndipo anali wokonzeka kulandira ndi chikondwelero kumasulira kwake.”—Ibid.

“Mfumu ya mafumu inali pafupi kupereka choonadi chachikulu kwa mfumu ya ku Babulo. Mulungu adzabvumbulutsa kuti ali ndi mphamvu pa maufumu a dziko lapansi, mphamvu zolonga ufumu ndi kuchotsa mafumu. Malingaliro a Nebukadinezara anali oti adzuke, ngati n’kotheka, kuti azindikire udindo wake ku Kumwamba. Zochitika zamtsogolo, zofikira kumapeto kwa nthawi, zinali zoti zibvumbulitsidwe pamaso pake .”—Prophets and Kings, p. 498.

**c. Kodi chinachitika ndi chiyani pamene mfumu inali kuyang’ana fano limeneli? Danieli 2:34, 35.**

______________________________________________

______________________________________________

**a. Kodi tanthauzo la mutu wopangidwa ndi golide linali chiyani? Danieli 2:36–38.**

---

“Pansi pa Mfumu Nebukadinezara, Babulo unali ufumu wolemera komanso wamphamvu kwambiri padziko lonse lapansi. Chuma chake ndi ulemerero wake zafotokozedwa pang'ono ndi Kuuziridwa.”— The Youth's Instructor, September 29, 1903.

**b. Ndi maufumu ati omwe amaimiridwa ndi zitsulo zotsatirazi? Danieli 2:39, 40.**

---

“Ulosi wafotokozera kuuka ndi kupita patsogolo kwa maufumu akuluakulu a dziko lapansi—Babulo, Mediya ndi Perisiya, Ufumu wa a Helene, ndi Roma.”—Prophets and Kings, p. 535.

“Danieli… analengeza kwa Nebukadinezara kuti ufumu wake uyenera kuponderezedwa. Ukulu wake ndi mphamvu zake m’dziko la Mulungu zidzatha, ndipo ufumu wachiwiri udzabuka, womwenso udzakhala ndi nthawi yake yoyesedwa ngati ungakweze Wolamulira mmodzi, Mulungu woona yekha. Popanda kuchita izi, ulemerero wake udzatha, ndipo ufumu wachitatu udzalowa m’malo mwake. Potsimikiziridwa ndi kumvera kapena kusamvera, uwu nawonso udzatha; ndipo wachinayi, wolimba ngati chitsulo, udzagonjetsa mitundu ya dziko lapansi. Maulosi awa a Wosathayo, olembedwa patsamba la ulosi ndipo akupezeka m’masamba a mbiri yakale, anaperekedwa kuti asonyeze kuti Mulungu ndiye mphamvu yolamulira muzochitika za dziko lino. Amasintha nthawi ndi nyengo, Amachotsa mafumu ndi kuyika mafumu, kuti akwaniritse cholinga Chake.”—The Youth’s Instructor, September 29, 1903

“Babulo anapita chifukwa mu ulemerero wake anaiwala Mulungu, ndipo anaonetsera kuti ulemerero wake unalipo chifukwa cha zipambano za umunthu.”

“Ufumu wa Mediya ndi Peresiya unakumana ndi mkwiyo wakumwamba chifukwa mu ufumu uwu lamulo la Mulungu linaponderezedwa. Kuopa Yehova sikunapezeke m’mitima ya anthu. Chikoka chomwe chinakula kwambiri mu ufumu wa Mediya ndi Peresiya unali kuipa, kunyoza Mulungu, ndi ziphuphu.”

“Maufumu omwe anatsatira anali oipa kwambiri komanso obvunda. Anayamba kuipiraipira chifukwa anasiya kumvera Mulungu. Pamene anamuiwala Iye, iwo anatsika kwambiri natsika kwambiri pamlingo wa makhalidwe abwino.”—Ibid., September 22, 1903.

**c. Kodi maufumu omwe ankaimiridwa ndi mapazi ndi zala anali osiyana ndi ena aja motani? Danieli 2:41–43**

“Malo athu m’chifaniziro cha Nebukadinezara akuimiridwa ndi zala za mapazi, mu khalidwe logawanika, komanso la chinthu chosweka, chomwe sichingagwirizane.”—Testimonies for the Church, vol. 1, p. 361.

## 5. UFUMU WA MULUNGU UDZAKHALA KWA MUYAYA — Lachisanu, Epulo 16

**a. Ndi ufumu uti umene udzathetsa dongosolo lonse la ulamuliro wa dziko lapansi? Danieli 2:44, 45.**

___

"Loto la fano laliikulu, linatsegura kwa Nebukadinezara zochitika zofikira kumapeto kwa nthawi, linaperekedwa kuti amvetse gawo lomwe iye ayenera kuchita mumbiri ya dziko lapansi, komanso ubale womwe ufumu wake uyenera kuchirikiza ndi ufumu wakumwamba. Pomasulira malotowo, iye adalangizidwa momveka bwino za kukhazikitsidwa kwa ufumu wosatha wa Mulungu."—Prophets and Kings, p. 503

**b. Kodi ulamuliro wa ufumu wa Mulungu mu ulemerero udzayamba liti? Yohane 18:36; Mateyu 25:31–34; 26:64; Chivumbulutso 6:15–17.**

___

"Ufumu wathu suli wa dziko lino lapansi. Tikuyembekezera Ambuye wathu kuchokera kumwamba kubwera padziko lapansi kudzachotsa ulamuliro wonse ndi mphamvu zonse, ndikukhazikitsa ufumu Wake wosatha. . . . Ulosi umatisonyeza kuti tsiku lalikulu la Mulungu layandikira. Ukufulumira kwambiri."—Testimonies for the Church, vol. 1, pp. 360, 361.

**c. Kodi mfumu inachita chiyani pamene Danieliaanakwanitsa kubvumbulutsa maloto ake? Danieli 2:46–49.**

___

___

"Kufotokozera kwa Danieli maloto amenewa kunamupangitsa kuti mfumu imupatse ulemu ndi udindo iye ndi anzake. . . . Anzake atatu a Danieli anapangidwa kukhala aphungu, oweruza, ndi olamulira m'dzikolo. Amuna awa sanadzitukumule ndi kudzikuza, koma anaona ndi kusangalala kuti Mulungu anazindikirika pamwamba pa mafumu onse a padziko lapansi, ndi kuti ufumu wake unakwezedwa kuposa maufumu onse a padziko lapansi."—The Youth's Instructor, September 8, 1903.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu nchimodzi, Epulo 17

1. Kodi Mfumu Nebukadinezara anapeza chiyani chokhudza anthu ake anzeru odalirika?
2. Kodi ndichifukwa chiyani zikuwonetsedwa kuti pemphero loyamika la Danieli lalembedwa, pomwe pemphero lake lopempha silinalembedwe?
3. Ngakhale kuti Danieli anali munthu wanzeru kwambiri mu Babulo, kodi anali ndi khalidwe lotani?
4. Fotokozani makhalidwe a maufumu omwe akuimiridwa ndi kusintha sintha kwa zipangizo zopangira gawo la fanoli.
5. Kodi gawo la maloto lokhudza mwala lidzakwaniritsidwa liti?

# Masomphenya Oyamba a Danieli

**VESI LOLOWEZA:** “Ndinapenya, ndipo nyanga yomweyi inachita nkhondo ndi opatulikawo, niwalaka; mpaka inadza Nkhalamba ya kale lomwe; ndi mlandu unakomera opatulika a Wam’mwambamwamba; nifika nthawi yakuti ufumu unali wawo wa opatulikawo” (Danieli 7:21, 22).

**Zowerenga Zowonjezera:** The Great Controversy, masamba 479–491; Early Writings, masamba 54–56.

“Pamene tikuyandikira kutha Kwa mbiri ya dziko lino, maulosi olembedwa ndi Danieli akufunika chidwi chathu chapadera, chifukwa akunena za nthawi yomwe tikukhalamo.”—Prophets and Kings, tsamba 547.

## 1. MPHEPO ZINAYI, ZILOMBO ZINAYI — Loyamba, Apulo 19

a. **Ndi liti lomwe Danieli adalandira masomphenya ake oyamba aulosi, ndipo adachita nawo chiyani? Danieli 7:1, 15, 16 (gawo loyamba).**

“Kutatsala nthawi yochepa kuti Babulo agwe, pamene Danieli ankalingalira za maulosiwa ndi kufunafuna Mulungu kuti amuthandizire kumvetsetsa kwa nthawizo, masomphenya otsatizana anaperekedwa kwa iye okhudza kuuka ndi kugwa kwa maufumu. Ndi masomphenya oyamba, monga momwe adalembedwera m’mutu wachisanu ndi chiwiri wa buku la Danieli, kutanthauzira kunaperekedwa; komabe si zonse zimene zinaululidwa momveka kwa mneneriyo.”—Prophets and Kings, tsamba 553.

b. **Kodi zinthu zachilengedwe zomwe zinaoneka zidali kuyimira chiyani? Danieli 7:2; Chivumbulutso 17:15; Yeremiya 25:31–33.**

c. **Kodi mngelo adalongosola bwanji tanthauzo la zilombo zazikulu zinayi zomwe zinatuluka? Danieli 7:3, 16 (gawo lomaliza), 17.**

“Maufumu aakulu omwe alamulira dziko lapansi anaonetsedwa kwa mneneri Danieli monga zilombo zolusa.”—The Great Controversy, masamba 439, 440.

**a. Kodi chilombo choyamba mwa zilombo zinayizi chidali chiyani, ndipo chidali kuyimira ufumu uti? Danieli 7:4; Yeremiya 50:17; Habakuku 1:6–8.**

____________________________________________

____________________________________________

"[Babulo] sanakwaniritse cholinga cha Mulungu; ndipo nthawi Yake itafika, ufumu wonyada ndi wamphamvu uwu, wolamulidwa ndi amuna anzeru zapamwamba, unasweka, n'kugubuduzika, popanda thandizo. Khristu adalengeza kuti, 'Popanda Ine simungathe kuchita kanthu.' Atsogoleri otchuka a ku Babulo sanadzione ngati odalira Mulungu. Amaganiza kuti adapanga ulemerero ndi ukulu wawo wonse pamaso pawo. Koma pamene Mulungu adalankhula, adali ngati udzu umene umafota, ndipo ngati maluwa a mu udzu amene amafota. Mawu ndi chifuniro cha Mulungu zokha ndizo zidzakhalapo mpaka kalekale."—The Youth's Instructor, September 29, 1903.

**b. Kodi chilombo chachiwiri chidafotokozedwa bwanji, ndipo chidayimira ufumu uti? Danieli 7:5.**

____________________________________________

____________________________________________

"Mtundu uliwonse umene waonekera pa dziko lapansi waloledwa kukhala ndi malo ake pa dziko lapansi, kuti kuoneke ngati udzakwaniritsa cholinga cha 'Woyang'anira ndi Woyera.' Ulosi watsatira kuuka ndi kugwa kwa maufumu aakulu a dziko lapansi—Babulo, Medo-Persia, Greece, ndi Roma. Pa uliwonse wa maufumuwa, monga mwa mitundu ya mphamvu zochepa, mbiri idadzibwereza yokha. Uliwonse unakhala ndi nthawi yake yoyesedwa, uliwonse unalephera, ulemerero wake unazima, mphamvu yake inachoka, ndipo malo ake anatengedwa ndi wina. "Pamene mitundu inakana mfundo za Mulungu, ndipo m'kukana kumeneku inadzipangira chiwonongeko chake, chidali choonekera kuti cholinga chaumulungu chodutsamo chidali kugwira ntchito m'mayendedwe awo onse."—Education, masamba 176, 177.

**c. Kodi ndi zinthu ziti zachilendo zomwe zidakhala mwa chilombo chachitatu, choimira ufumu wa chi Herene? Danieli 7:6.**

____________________________________________

____________________________________________

"Ngati maufumu osiyanasiyana awa akadakhala ndi mantha a Yehova pamaso pawo nthawi zonse, akadagawiridwa nzeru ndi mphamvu, zomwe zikadawamanga pamodzi ndikuwasunga kukhala amphamvu. Koma olamulira a maufumu a dziko lapansi sadapange Mulungu kukhala mphamvu yawo pokhapokha atazunzidwa ndi kusokonezeka... Adakakamizika kupempha kwa iwo omwe malingaliro awo adawunikiridwa ndi kuwala kwa kumwamba, kuti awafotokozere zinsinsi zomwe sakanatha kuzimvetsa."—The Youth's Instructor, September 29, 1903.

**a. N’chiyani chinapangitsa chilombo chachinayi kukhala chovuta kuchifotokoza m’zinthu zachilengedwe? Danieli 7:7.**

“Mzimu Woyera akuimira maufumu a dziko lapansi pansi pa chizindikiro cha zilombo zolusa; koma Khristu ndiye ‘Mwana wankhosa wa Mulungu, amene achotsa chimo la dziko lapansi.’ Yohane 1:29. Mu dongosolo la ulamuliro wake mulibemo kuikamo mphamvu za ukali kuti zisokoneze ungwiro”—Christ’s Object Lessons, tsamba 77.

“Mtanda unalumikizidwa ndi mphamvu ya Roma. Chidali chida cha mtundu wa imfa yankhanza kwambiri komanso yochititsa manyazi. Zigawenga zotsika kwambiri zimayenera kunyamula mtanda kupita nawo kumalo ophedwerako; ndipo nthawi zambiri pamene unatsala pang’ono kuikidwa pa mapewa awo, ankatsutsa ndi chiwawa chachikulu, mpaka atagonjetsedwa, ndipo chida chozunziracho chinamangidwa pa iwo.”—The Desire of Ages, masamba 416, 417.

**b. Kodi n’chiyani chinaoneka pakati pa nyanga za chilombo chachinayi? Danieli 7:8.**

---

“M’zaka za m’ma 500 (6th century), upapa unali utakhazikika ndithu. Mpando wake wa ulamuliro wake unakhazikitsidwa mu mzinda wa ufumu, ndipo bishopu wa ku Roma analengezedwa kukhala mtsogoleri wa mpingo wonse. Chikunja chidapatsa malo ku upapa. Chinjoka chidapatsa chilombocho ‘mphamvu yake, ndi mpando wake, ndi ulamuliro waukulu.’ Chivumbulutso 13:2. Ndipo tsopano panayamba zaka 1260 za kuponderezedwa ndi upapa zomwe zinanenedweratu m’maulosi a Danieli ndi Chivumbulutso. Danieli 7:25; Chivumbulutso 13:5–7. Akhristu adakakamizika kusankha mwina kusiya chikhulupiriro chawo ndikulandira miyambo ya upapa ndi kulambira, kapena kuononga moyo wawo m’mayenje kapena kuphedwa pa rack, fagot, kapena nkhwangwa ya mphedzi. Pamenepo adakwaniritsidwa mawu a Yesu: ‘Mudzaperekedwa ngakhale ndi akukubalani, ndi abale, ndi apfuko lanu, ndi abwenzi anu; ndipo ena a inu adzakuphani. Ndipo anthu onse adzadana ndi inu chifukwa cha dzina langa.’ Luka 21:16, 17. Chizunzo chinatsegulidwa pa okhulupirika ndi mkwiyo waukulu kuposa kale lonse, ndipo dziko lapansi linakhala ngati malo ankhondo aakulu. Kwa zaka mazana ambiri mpingo wa Khristu unapeza pothawira m’malo obisika komanso osadziwika. Motero ananena mneneri: ‘Ndipo mkazi anathawira kuchipululu, kumene ali nayo mbuto yokonzedweratu ndi Mulungu, kuti kumeneko akamdyetse masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri, mphambu makumi asanu ndi limodzi.’ Chivumbulutso 12:6.”—The Great Controversy, masamba 54, 55.

**c. Kodi Danieli anafuna kudziwa chiyani ataona masomphenyawo? Danieli 7:19, 20.**

---

**a. Kodi mngelo adalongosola chiyani za chilombo chachinayi choopsa chosonyeza Ufumu wa Roma? Danieli 7:23.**

---

**b. Kodi n’chiyani chinaululidwa za nyanga yaing’ono? Danieli 7:24.**

---

“Ufumu waukulu wa Roma unagubuduzika kukhala zidutswa, ndipo kuchokera m’mabwinja ake munauka ulamuliro wamphamvu uja, Mpingo wa Katolika wa ku Roma. Mpingo uwu umadzitama chifukwa cha kusalephera kwake komanso chipembedzo chake cha chibadwa. Koma chipembedzo chimenechi ndi chowopsa kwa onse amene akudziwa zinsinsi za chinsinsi cha kusayeruzika. Ansembe a mpingowu amasunga ulamuliro wawo mu kusunga anthu kukhala osadziwa chifuniro cha Mulungu, monga momwe chaululidwira m’Malemba.”—The Youth’s Instructor, September 22, 1903.

**c. Kodi mkwiyo wa nyanga yaing’ono udzakhala kwa ndani? Danieli 7:21, 25.**

“Kukwera kwa Mpingo wa Roma ku mphamvu kunaonetsa chiyambi cha Nthawi Yamdima (Dark Ages). Pamene mphamvu yake inkawonjezeka, mdima unakula. Chikhulupiriro chinasamutsidwa kuchoka kwa Khristu, maziko owona, kupita kwa papa wa ku Roma. M’malo mokhulupirira Mwana wa Mulungu kuti akhululukidwe machimo ndi chipulumutso chamuyaya, anthu anayang’ana kwa papa, komanso kwa ansembe ndi akuluakulu a mpingo amene anawapatsa ulamuliro. Anaphunzitsidwa kuti papa ndiye mkhala pakati wawo wa padziko lapansi ndipo palibe amene angafike kwa Mulungu kupatula kudzera mwa iye; komanso, kuti iye anaimira Mulungu kwa iwo ndipo anafunika kumumvera kotheratu. Kupatuka pa mfundo zimenezi chinali chifukwa chokwanira chopatsira chilango chowopsa pa matupi ndi miyoyo ya olakwawo. Motero malingaliro a anthu anachotsedwa kwa Mulungu kupita kwa anthu oipa, olakwa, komanso ankhanza, ngakhale kuposera pamenepo, kwa kalonga wa mdima iye mwini, amene anagwiritsa ntchito mphamvu yake kudzera mwa iwo. Tchimo linabisidwa mu mwinjiro wa chiyero. Pamene Malemba aletsedwa, ndipo munthu adziona ngati wapamwamba, timayenera kuyembekezera chinyengo ndi choipa chachikulu. Kudzera mu kukwezedwa kwa malamulo ndi miyambo ya anthu, kunaonekera tchimo lomwe nthawi zonse limabwera chifukwa chotaya chilamulo cha Mulungu.

“Awa adali masiku owopsa kwa mpingo wa Khristu. Onyamula mbendera okhulupirika adali ochepa ndithu. Ngakhale choonadi sichinasiyidwe popanda mboni, koma nthawi zina zinkaoneka ngati kulakwa ndi kukhulupirira zamatsenga zidzapambana kotheratu, ndipo chipembedzo chowona chidzapirikitsidwa padziko lapansi. Uthenga wabwino unayiwalika, koma mitundu ya zipembedzo inachuluka, ndipo anthu analemedwa ndi zikakamizo zowopsa.”—The Great Controversy, tsamba 55.

## 5. CHIWERUZIRO — Lachisanu, Apulo 23

**a. Kodi chikanachitika n'chiyani kuti mphamvu ya nyanga yaing'ono ithetsedwe? Danieli 7:26.**

______________________________________________________________

"Miyezi makumi anayi ndi iwiri [ya pa Chivumbulutso 13:5] ndi yofanana ndi 'nthawi, ndi nthawi zina, ndi nthawi ya nusu,' zaka zitatu ndi theka, kapena masiku 1260 a pa Danieli 7—nthawi imene mphamvu ya upapa idzapondereza anthu a Mulungu. Nthawi imeneyi... idayamba ndi ulemu kwa upapa mu 538 A.D., ndipo inatha mu 1798. Pa nthawi imeneyo, papa anatengedwa ukapolo ndi asilikali a ku France, ulamuliro wa upapa unalandira bala la ku imfa, ndipo ulosi unakwaniritsidwa wakuti, 'Iye amene atsogolera ku ukapolo adzapita ku ukapolo.'"—The Great Controversy, tsamba 439.

**b. Kodi kuchitika kwa chiweruzo kwafotokozedwa motani? Danieli 7:9, 10, 13.**

______________________________________________________________

"Kubwera kwa Khristu komwe kukufotokozedwa pano si kubwera Kwake kwachiwiri padziko lapansi. Akubwera kwa Nkhalamba ya Kale lomwe kumwamba kuti alandire ulamuliro ndi ulemerero ndi ufumu, zomwe adzapatsidwa pa kutha kwa ntchito Yake monga mkhala pakati."—… tsamba 480.

**c. Kodi zotsatira za chiweruzo zidzakhala chiyani? Danieli 7:11, 14, 18, 22, 26, 27.**

______________________________________________________________

"Dongosolo lalikulu la chiombolo limapangitsa kuti dziko libwerere modzadza ku chisomo cha Mulungu. Zonse zimene zinatayika chifukwa cha uchimo zimabwezeretsedwa. Osati munthu yekha, komanso dziko lapansi limaomboledwa, kuti likhale malo okhalamo amuyaya a iwo omumvera. Kwa zaka zikwi zisanu ndi chimodzi Satana wakhala akulimbana kuti atenge dziko lapansi. Tsopano cholinga cha pachiyambi cha Mulungu m'chilengedwe chake chakwaniritsidwa. 'Koma opatulika a Wam'mwambamwamba adzalandira ufumuwo, ndi kukhala nawo ufumu kosatha ku nthawi zonka muyaya.' Danieli 7:18."—Patriarchs and Prophets, tsamba 342.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Epulo 24

1. Fotokozani zilombo zinayi zomwe Danieli adaziona zikutuluka m'nyanja.
2. Tchulani maufumu omwe zilombozo zidaimira, komanso momwe makhalidwe awo adakwaniritsidwira.
3. N'chiyani chomwe chinapangitsa ulamuliro wa nyanga yaing'ono kukhala wosiyana ndi ma ulamuliro ena omwe anaonetsedwa?
4. Kodi mawu "aakulu" a ulamuliro wa nyanga yaing'ono adali chiyani?
5. Kodi chiweruzo chidzapereka ulamuliro wa dziko lapansi kwa ndani, ndipo ndi liti?

# CHOPEREKA CHA SABATA YOYAMBA

**May 2, 2026**

**Za Umishonale wa Dziko Lonse**



Pa Msonkhano wa 24 wa ku likulu, ma mishoni atsopano ambiri omwe angotsegulidwa kumene adaimiridwa. Tikukondwera kwambiri ndi kupita patsogolo kumeneku m'ntchito ya choonadi cha nthawi ino, ndipo tikuyembekezera kutsegula madera ena ambiri, pamene dziko lonse liyenera kuwunikilidwa ndi ulemerero wa Mulungu.

Pali njira zoposa imodzi zothandizira pa ntchito yodabwitsa imeneyi yopulumutsa miyoyo m'madera atsopano. "Pakuti aliyense amene adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka. Ndipo iwo adzaitana bwanji pa Iye amene sanamkhulupirira? Ndipo adzakhulupirira bwanji Iye amene sanamva za Iye? Ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? Ndipo adzalalikira bwanji ngati satumidwa?" (Aroma 10:13–15, gawo loyamba). Onse awiri, ogwira ntchito m'munda komanso amene amapereka chuma chothandizira ntchitoyi, amakana wokha m'njira zosiyanasiyana kuti apulumutse nkhosa zotayika.

"Mukanadziwa nonse m'magulu athu mmene zinalili zovuta m'zaka zam'mbuyo kukhazikitsa ntchito m'madera omwe masiku ano akhala malo ofunika kwambiri, mukanazindikira kuti pamafunika kulimba mtima kulimbana ndi mikhalidwe yovuta ndikulengeza, kwinaku manja ali m'mwamba kupita kumwamba kuti: 'Sitikulefuka kapena kutaya mtima.' Iwo omwe asanaphule nawo kanthu m'madera atsopano komanso ovuta sazindikira zovuta za ntchito ya upainiya. Ngati akanatha kumvetsa kagwiridwe ka ntchito ka Mulungu, sakanangosangalala chifukwa cha zomwe zachitika, koma akanaona chifukwa chosangalalira m'tsogolo mwa ntchitoyi.

"Abale anga, palibe chifukwa chotayira mtima. Mbewu yabwino ikufesedwa. Mulungu adzaiyang'anira, ndipo adzaipangitsa kuti imere ndi kubala zokolola zambiri. Kumbukirani kuti ntchito yambiri yopulumutsa miyoyo, kuyambira pachiyambi, yakhala ikupitabe chitsogolo pakati pa zovuta zazikulu."—Testimonies for the Church, vol. 7, tsamba 242.

Ndalama iliyonse yomwe tili nayo ndi ya Ambuye. M'malo mowononga chuma pa zinthu zosafunikira, tiyenera kuchigwiritsa ntchito poyankha maitanidwe a ntchito ya utumiki. "Pamene madera atsopano akutsegulidwa, maitanidwe a chuma akuchuluka kosalekeza."—Historical Sketches, tsamba 293.

Choncho, chopereka cha Sabata Yoyamba cha lero chisonkhanitsidwa kuti chigwire ntchito ku ma mishoni a dziko Lonse, chuma chofunikira kwambiri chomwe chikusowekera zedi tsopano lino. Ambuye adalitse wopereka aliyense kuti apereke mwachimwemwe, modzikana, komanso mwachikhulupiriro—ndipo apereke mphoto kwa aliyense payekhapayekha.

Ndife abale anu ochokera ku General Conference.

LASABATA, MEYI 2, 2026

PHUNZIRO 5

# Mndandanda wa Maufumu

**VESI LOLOWEZA:** "Ndipo masomphenya a madzulo ndi mamawa adanenawo ndi oona; koma iwe ubise masomphenyawo; popeza adzachitika atapita masiku ambiri" (Danieli 8:26).

**Zowerenga Zowonjezera:** The Great Controversy, masamba 423–432.

"Mtundu uliwonse... wakhala ndi nthawi yake yoyesedwa; uliwonse walephera, ulemerero wake wazilala, ndipo mphamvu yake yachoka."—Prophets and Kings, p. 535.

## 1. NKHOSAYO IKHALA YAMPHAMVU — Loyamba, Epulo 26

**a. Chakumapeto kwa ulamuliro wa Babulo, kodi Danieli anaona chiyani? Danieli 8:1, 2.**

______________________________________________________________________

**b. Fotokozani khalidwe la chilombo choyamba chomwe chinaonekera n'kukhala champhamvu. Danieli 8:3, 4.**

______________________________________________________________________

**c. Kodi mngelo adatanthauzira bwanji nkhosa yamphongo imene Danieli adaiona? Danieli 8:19, 20.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"M'masomphenya a mneneri [Mulungu] akuoneka akugwetsa wolamulira wamphamvu mmodzi, ndipo akukhazikitsa wina. Akuululidwa kukhala mfumu ya chilengedwe chonse, yomwe yatsala pang'ono kukhazikitsa ufumu Wake wosatha—Nkhalamba ya kale lomwe, Mulungu wamoyo, Gwero la nzeru zonse, Wolamulira wa nthawi ya lero, ndi Woulula zam'tsogolo."—The SDA Bible Commentary [E. G. White Comments], vol. 4, tsamba 1166.

"Kuchokera pa kuuka ndi kugwa kwa mitundu monga momwe kwafotokozedwera momveka m'mabuku a Danieli ndi Chivumbulutso, tifunika kuphunzira mmene ulemerero wakunja ndi wa dziko lino ulili wopanda pake. Babulo, ndi mphamvu zake zonse ndi ukulu wake, zomwe dziko lathu silinaoneponso chotero—mphamvu ndi ukulu zomwe kwa anthu a nthawi imeneyo zinkaoneka ngati zokhazikika ndi zokhalitsa—mmene zinathera psiti! Monga 'maluwa a udzu,' iwo wawonongeka. Chotero ufumu wa Medo-Persia unatha, komanso maufumu a Chigiriki ndi Roma. Ndipo chidzathanso choncho chilichonse chomwe chilibe Mulungu monga maziko ake."—Prophets and Kings, tsamba 548.

**a. Kodi ndi mphamvu iti yatsopano yomwe inadza kudzatsutsa Medo-Persia? Danieli 8:5, 21.**

**b. Fotokozani mphamvu yogonjetsa ya mfumu ya mu ufumu watsopanowu. Danieli 8:6, 7.**

---

"Mphamvu imene wolamulira aliyense pa dziko lapansi amagwiritsa ntchito imaperekedwa kuchokera kumwamba; ndipo pa kagwiritsidwe ntchito kake ka mphamvu yomwe wapatsidwayo, kupambana kwake kumadalira pamenepo. Kwa aliyense mawu a Woyang'anira waumulungu ali akuti, 'Ndidzakumanga m'chuuno, ngakhale sunandidziwa.' Yesaya 45:5. Ndipo kwa aliyense mawu olankhulidwa kwa Nebukadinezara wakale ndi phunziro la moyo: 'Dulani machimo anu ndi kuchita chilungamo, ndi mphulupulu zanu mwa kuchitira a umphawi chifundo; kuti kapena nthawi ya mtendere wanu italike.' Danieli 4:27. "Kumvetsa zinthu izi—kumvetsa kuti 'chilungamo chikuza mtundu wa anthu;' kuti 'pakuti mpando wawo wakhazikika ndi chilungamo' ndipo 'chisungika ndi chifundo' (Miyambo 14:34; 16:12; 20:28); kuzindikira kugwira ntchito kwa mfundo izi m'kuonetsedwa kwa mphamvu Yake amene 'achotsa mafumu, nalonga mafumu' (Danieli 2:21)—uku ndiko kumvetsa nzeru za mbiri ya dziko.

"M'mawu a Mulungu mokha ndimo izi zafotokozedwa momveka bwino. Pano zikuonetsedwa kuti mphamvu ya mitundu, monga ya munthu aliyense payekha, siipezeka m'mwayi kapena zinthu zomwe zikuoneka kuti zimawapangitsa kukhala osagonjetseka; siipezeka m'kudzikuza kwa ukulu wawo. Imayezedwa ndi kukhulupirika kumene amakwaniritsa nako cholinga cha Mulungu."—Education, masamba 174, 175.

**c. Kodi n'chiyani chinachitikira ufumu wa Chigiriki pamene unakhala wamphamvu kwambiri pa nthawi ya ulamuliro wa Alexander Wamkulu? Danieli 8:8, 22.**

"Iye amene ali wochedwa kukwiya,' akuti munthu wanzeru, 'aposa wamphamvu; ndipo wolamulira mzimu wake aposa wolanda mzinda.' Mwamuna kapena mkazi amene amasunga kulinganiza kwa maganizo pamene ayesedwa kuchita zofuna za mtima amakhala pamwamba pamaso pa Mulungu ndi angelo akumwamba kuposa mkulu wa asilikali wotchuka kwambiri amene anatsogolerako asilikali kunkhondo ndi kupambana. Mfumu ina yotchuka kwambiri inati ili pakama wa imfa, 'Mwa kugonjetsa kwanga konse, pali kumodzi kokha kumene kukundipatsa chitonthozo tsopano, ndipo kumeneko ndi kugonjetsa kumene ndapeza pa mkwiyo wanga wosalamulirika.' Alexander ndi Caesar anapeza kukhala kophweka kugonjetsa dziko kuposa kudzigonjetsa okha. Atatha kugonjetsa mtundu ndi mtundu, iwo anagwa—mmodzi wa iwo 'ngati wozunzidwa ndi kuledzera, wina ndi kudzikuza kopenga nako."—Child Guidance, masamba 95, 96.

**a. Kodi ndi mphamvu iti yatsopano imene ikufotokozedwa kuti inatenga ulamuliro wa ufumu wa Chigiriki utagawikana? Danieli 8:9, 23.**

**b. Fotokozani zochita za ufumu wa Roma—wa chikunja ndi wa upapa—zomwe Danieli anaona m’masomphenya. Danieli 8:10–12, 24.**

“Upapa unali utakhala wolamulira wankhanza wa dziko lonse. Mafumu aang’ono ndi aakulu omwe anagwadira malamulo a Papa wa Roma. Tsogolo la anthu, la nthawi ino komanso la muyaya, linkaoneka kukhala pansi pa ulamuliro wake... Koma ‘usana wa upapa unali pakati pa usiku wa dziko lapansi...’ Kwa zaka mazana ambiri ku Ulaya sikunapite patsogolo m’maphunziro, luso la zamanja, kapena chitukuko. Kupuwala kwa makhalidwe ndi nzeru kunali kutagwera Dziko la Chikhristu.”—The Great Controversy, tsamba 60.

“Monga momwe zinanenedweratu ndi ulosi, mphamvu ya upapa inagwetseratu choonadi pansi. Chilamulo cha Mulungu chinaponderezedwa m’fumbi, pamene zikhalidwe ndi miyambo ya anthu zinakwezedwa. Mipingo yomwe inali pansi pa ulamuliro wa upapa inakakamizidwa mofulumira kulemekeza Lamlungu kukhala tsiku loyera. Pakati pa kulakwa ndi kukhulupirira zamatsenga komwe kunalipo, ambiri, ngakhale anthu owona a Mulungu, anasokonezeka kwambiri moti pamene ankasunga Sabata, ankalekanso kugwira ntchito pa Lamlungu. Koma izi sizinakhutilitse atsogoleri a upapa. Iwo anafuna kuti osati Lamlungu lokha likhale loyera, koma kuti Sabata liyipitsidwe; ndipo anadzudzula m’mawu amphamvu kwambiri iwo amene anayesa kulilemekeza. Inali njira yothawira ku mphamvu ya Roma kokha imene aliyense akanatha kumvera chilamulo cha Mulungu mu mtendere.”—tsamba 65.

**c. Ngakhale njira zake zinali zachinyengo, kodi ulamuliro umenewu ukanatha bwanji? Danieli 8:25.**

---

“Pakati pa mdima umene unakhazikika padziko lapansi m’nthawi yayitali ya kukweza upapa, kuwala kwa choonadi sikukanatha kuzimitsidwa kotheratu. Mu m’badwo uliwonse panali mboni za Mulungu—amuna amene anasunga chikhulupiriro mwa Khristu monga mkhala pakati yekhayo wa Mulungu ndi munthu, amene anasunga Baibulo monga lamulo lokhalo la moyo, ndi amene anayeretsa Sabata lowona. Kukula kwa ngongole imene dziko lino lili nayo kwa amuna awa, m’badwo wa m’tsogolo sudzadziwa n’komwe. Iwo anatchedwa ampatuko, zolinga zawo zinayesedwa kukhala zoipa, makhalidwe awo ananyozedwa, zolemba zawo zinaletsedwa, kupotozedwa, kapena kuonongedwa. Komabe iwo anayima nji, ndipo m’badwo ndi m’badwo unasunga chikhulupiriro chawo m’kuyera kwake, monga cholowa chopatulika cha mibadwo imene ikubwera.”— tsamba 61.

1. **Kodi Danieli anamva kukambirana kotani kokhudzana ndi nthawi yomwe zinthu za m'masomphenyawo zidzatenge, ndipo n'chiyani chidzachitika kumapeto kwa nthawi imeneyo? Danieli 8:13, 14.**

2. **Kodi ndi chochitika chiti chomwe chidasonyezedwa ndi kuyeretsedwa kwa malo opatulika, monga momwe kusonyezedwera m'chilamulo cha miyambo, ndi kunenedweratu m'masomphenya a Danieli? Levitiko 23:27–32; 16:33, 34.**

"M'dongosolo la zophiphilitsa, lomwe linali mthunzi wa nsembe ndi unsembe wa Khristu, kuyeretsedwa kwa malo opatulika unali utumiki womaliza wochitidwa ndi mkulu wa ansembe m'chaka chonse cha utumiki. Inali ntchito ya kutseka kwa chitetezero—kuchotsa kapena kutaya machimo mwa Israyeli. Inali chithunzi cha ntchito yomaliza mu utumiki wa Mkulu wa nsembe wathu kumwamba, m'kuchotsa kapena kufafaniza machimo a anthu Ake, omwe alembedwa m'mabuku a kumwamba."—The Great Controversy, tsamba 352.

"Monga kale machimo a anthu mwa chikhulupiriro ankaikidwa pa nsembe yauchimo ndipo kudzera m'mwazi wake ankasamutsidwa, m'chithunzi, kupita m'mkachisi wa padziko lapansi, chotero m'pangano latsopano machimo a olapa mwa chikhulupiriro amaikidwa pa Khristu ndipo amasamutsidwa, m'zenizeni, kupita m'kachisi wa kumwamba. Ndipo monga kuyeretsedwa kwa chithunzi kwa kachisi wa padziko lapansi kunakwaniritsidwa mwa kuchotsa machimo amene anadetsedwa nawo, chotero kuyeretsedwa kwenikweni kwa kachisi wa kumwamba kuyenera kukwaniritsidwa mwa kuchotsa, kapena kufafaniza, machimo amene alembedwa kumeneko. Koma izi zisanachitike, payenera kukhala kufufuza kwa mabuku a zolembedwa kuti kudziwike amene, kudzera m'kulapa machimo ndi chikhulupiriro mwa Khristu, ali ndi mwayi wopindula ndi chitetezero Chake. Kuyeretsedwa kwa malo opatulika chotero kukuphatikiza ntchito yofufuza—ntchito ya chiweruziro. Ntchitoyi iyenera kuchitika Khristu asanadze kudzawombola anthu Ake; pakuti akadzadza, mphotho Yake Ali nayo yakupatsa munthu aliyense monga mwa ntchito zake. Chivumbulutso 22:12."—masamba 421, 422.

3. **Kodi mngelo anati chiyani za ulosi wa masiku 2300? Danieli 8:26 (yerekezerani ndi vesi 14).**

## 5. MASOMPHENYA OMWE SANAMVETSETSEKE BWINOBWINO — Lachisanu

**a. Kodi mngelo Gabriyeli anatumidwa kuti amuchitire chiyani Danieli? Danieli 8:15–18.**

“Anali Gabriyeli, mngelo wotsatira pa udindo pambuyo pa Mwana wa Mulungu, amene anabwera ndi uthenga waumulungu kwa Danieli. Anali Gabriyeli, ‘mngelo Wake,’ amene Khristu anamutuma kuti adzatsegule zam’tsogolo kwa Yohane wokondedwa; ndipo mdalitso watchulidwa pa iwo amene amawerenga ndi kumva mawu a ulosi, ndi kusunga zinthu zolembedwamo. Chivumbulutso 1:3.”—The Desire of Ages, tsamba 234.

**b. Ngakhale anapatsidwa malongosoledwe amene adali omveka bwino, kodi Danieli anachita chiyani atamva za ulosi wa nthawi ya masiku 2300? Danieli 8:27.**

---

“Kudzera m’masomphenya ena kuwala kwina kunaperekedwa pa zochitika zam’tsogolo; ndipo chidali chakumapeto kwa masomphenya awa pamene Danieli anamva ‘woyera mmodzi akulankhula, ndipo woyera wina anati kwa woyera uja amene ankalankhula, Masomphenya adzakhala mpaka liti?’ Danieli 8:13. Yankho lomwe linaperekedwa, ‘mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku; pamenepo malo opatulika adzayesedwa wolungama’ (vesi 14), linamudzadza ndi kusokonezeka. Mofunitsitsa anafunafuna tanthauzo la masomphenyawo. Sakanatha kumvetsa m’gwirizano womwe ulipo pakati pa zaka makumi asanu ndi awiri (70) za ukapolo, monga momwe kunanenedweratu kudzera mwa Yeremiya, ndi zaka zikwi ziwiri ndi mazana atatu (2300) zomwe m’masomphenya anamva mlendo wakumwamba akulengeza kuti zidzadutsa malo opatulika a Mulungu asanayeretsedwe. Mngelo Gabriyeli anamupatsa kumasulira kwa pang’ono; komabe pamene mneneriyo anamva mawu akuti, ‘Masomphenya... adzakhala a masiku ambiri,’ anakomoka. ‘Ine Danieli ndinakomoka,’ iye alemba zimene zinachitika, ‘ndipo ndinadwala masiku ena; pambuyo pake ndinadzuka, ndipo ndinagwira ntchito ya mfumu; ndipo ndinadabwa ndi masomphenyawo, koma panalibe wakuwazindikilitsa.’ Vesi 26, 27.”—Prophets and Kings, tsamba 554.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n’chimodzi, Meyi 1

1. Kodi ndi zolinga ziti zomwe nthawi zambiri zimapangitsa maufumu a dziko lapansi kufuna kulanda malo a ena?
2. Kodi ndi vuto liti la khalidwe lomwe silinakonzedwe lomwe linapangitsa nyanga yaikulu ya tonde kuthyoka?
3. Kodi gawo la Roma wachikunja ndi Roma waupapa linafana bwanji?
4. Kodi n’chiyani chidzachitika kumapeto kwa masiku 2,300?
5. Ndi gawo liti la masomphenya lomwe linali chinsinsi kwa Danieli pamene adakomoka?

# Masomphenya Afotokozedwa

**VESI LOLOWEZA:** “Dziwani tsono, nimuzindikire, kuti kuyambira kutuluka kwa lamulo lakukonzanso, ndi kummanga Yerusalemu, kufikira wodzodzedwayo, ndiye kalonga, kudzakhala masabata asanu ndi awiri; ndi masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri, makwalala ndi chemba zidzamangidwanso, koma mu nthawi ya mavuto” (Danieli 9:25).

**Zowerenga Zoonjezera:** *The Great Controversy,* pp. 409–422.

“Mngelo anatumizidwa kwa Danieli ndi cholinga chakuti amufotokozere mfundo imene iye analephera kumvetsetsa m’masomphenya a chapta chachisanu ndi chitatu, mawu onena za nthawi.” — *The Great Controversy, p. 326.*

## 1. KUWERENGA KUTI UMVETSE

**Loyamba, Meyi 3**

**a. Pa nthawi imene Amedi ndi Aperisi anagonjetsa Babulo, Kodi Danieli ankaphunzira chiyani? Danieli 9:1, 2.**

___

___

___

“Pamene iwo amene anakhalabe okhulupirika kwa Mulungu pakati pa Babulo anali kufunafuna Yehova ndi kuphunzira maulosi oneneratu za kupulumutsidwa kwawo, Mulungu anali kukonzetsera mitima ya mafumu kuti Iye asonyeze chisomo kwa anthu Ake olapa.”—The *SDA Bible Commentary* [EG White Comments], vol. 4, p. 1172

**b. Fotokozani kufunikira kwa ulosi umene Danieli anali kuwerenga. Yeremiya 25:8–14.**

___

___

___

**c. Kodi ulosi wa Yeremiya unalimbikitsa anthu a Mulungu kuchita chiyani? Yeremiya 29:10–14**

___

___

“Zolemba za Yeremiya zopezekeratu ndi [anthu ogwidwa ukapolo], ndipo m’zimenezi munalembedwa momveka bwino nthawi imene iyenera kudutsa Israyeli asanabwerere ku Babulo. . . . Chiyanjo chidzaperekedwa kwa otsala a Yuda, poyankha pemphero lochokera pansi pa mtima.”— Prophets *and Kings,* p. 552.

**a. Kodi Danieli anachita chiyani poyankha zomwe anawerenga? Danieli 9:3.**

---

"Ndi chikhulupiriro chozikidwa pa mawu otsimikizika a ulosi, Danieli anapempha Ambuye kuti malonjezo awa akwaniritsidwe mwachangu. Iye anapempha kuti ulemu wa Mulungu ukasungidwe. M'pemphero lake iye anadzizindikiritsa kwathunthu ndi iwo amene analephera kukwaniritsa cholinga cha Mulungu, naulula machimo awo ngati ake."—*Prophets and Kings, pp. 554, 555*

**b. Pakutha kuwerenga pemphero la Danieli, kodi munganene chiyani za momwe iye anadzichepetsera ndikupembedzera kwa Mulungu? Danieli 9:4–19.**

---

"Ngakhale kuti Danieli wakhala mu utumiki wa Mulungu kwa nthawi yaitali, ndipo kumwamba kunamutchula kuti 'wokondedwa kwambiri,' komabe tsopano anaonekera pamaso pa Mulungu monga wochimwa, akupembedzera chosowa chachikulu cha athu omwe iye amawakonda." — Ibid., p. 555.

**c. Kodi Danieli ankadera nkhawa kwambiri za chiyani? Danieli 9:16, 17.**

---

---

"Kwa zaka pafupifupi makumi asanu ndi awiri, Israyeli anali mu ukapolo. Dziko limene Mulungu anasankha kukhala lake linaperekedwa m'manja mwa amitundu. Mzinda wokondedwa, wolandira kuwala kwa kumwamba, womwe kale unali chisangalalo cha dziko lonse lapansi, tsopano unanyozedwa ndi kupeputsidwa. Kachisi amene anali ndi likasa la pangano la Mulungu ndi akerubi aulemerero omwe anali kuphimba mpando wachifundo, anali atawonongeka. Malo ake omwe anaipitsidwa ndi mapazi odetsedwa. Amuna okhulupirika omwe ankadziwa za ulemerero wakale anadzazidwa ndi chisoni chifukwa cha kuwonongedwa kwa nyumba yopatulika yomwe inasiyanitsa Israyeli monga anthu osankhidwa ndi Mulungu. Amuna awa anali mboni za kudzudzula kwa Mulungu chifukwa cha machimo a anthu Ake. Iwo anali mboni za kukwaniritsidwa kwa mawu awa. Iwo analinso mboni za malonjezo a chisomo Chake ngati Israyeli angabwerere kwa Mulungu, ndikuyenda mosamala pamaso Pake. Oyendayenda okalamba, aimvi analikupita ku Yerusalemu kukapemphera pakati pa mabwinja ake. Iwo anapsompsona miyala yake, nainyowetsa ndi misozi yawo, pamene ankapempha Ambuye kuti achitire chifundo Ziyoni, ndi kumuphimba ndi ulemerero wa chilungamo Chake. Danieli ankadziwa kuti nthawi yoikika ya ukapolo wa Israyeli inali pafupi kutha; koma sanachimve kuti chifukwa Mulungu analonjeza kuwapulumutsa iwo, iwo analibe gawo lochitapo kanthu. Ndi kusala kudya ndi kulapa, anafunafuna Ambuye, kuulula machimo ake ndi machimo a anthuwo."—The *SDA Bible Commentary* [EG White Comments], vol. 4, p. 1172.

**a. Kodi pemphero la Danieli linasokonezedwa bwanji? Danieli 9:20, 21**

“Kumwamba kunali kuwerama kuti kumve pemphero lochokera pansi pa mtima la mneneri. Ingakhale iye asanamalize pempho lake la cikhululukiro ndi kubwezeretsa, Gabrieli wamphamvuyo anaonekeranso kwa *iye.”—Prophets and Kings,* p. 556

“Anali Gabrieli, mngelo wotsatira pa udindo wa Mwana wa Mulungu, amene anabwera ndi uthenga wa Mulungu kwa Danieli. . . . Mulungu watipatsa zinthu izi, ndipo madalitso Ake adzabwera chifukwa cha kuphunzira malemba aulosi mwaulemu komanso mwapemphero.”— *The Desire of Ages,* p. 234.

**b. Kodi cholinga cha kuyendera kwa Gabrieli kunali chiyani, ndipo kukugwirizana bwanji ndi masomphenya omwe ali mu Chaputala 8? Danieli 9:22, 23.**

“[Gabrieli] anaitanitsa chidwi chake ku masomphenya amene anaona Babulo asanagwe komanso imfa ya Belisazara isanachitke.”— Prophets *and Kings,* p. 556

“Mulungu analamula mthenga wake kuti: ‘Mpange munthu uyu kumvetsetsa masomphenyawa.’ Ntchito imeneyi iyenera kukwaniritsidwa. Pomvera izi, mngeloyo, patapita nthawi, anabwerera kwa Danieli, nati: ‘Ndabwera tsopano kuti ndikupatse luntha ndi chidziwitso;’ ‘chifukwa chake mvetsetsa nkhaniyi, ndipo lingalira masomphenyawa.’ Danieli 8:27, 16; 9:22, 23, 25–27. Panali mfundo imodzi yofunika kwambiri m’masomphenya a chaputala 8 yomwe sinafotokozedwe, ndiyo yokhudzana ndi nthawi—nthawi ya masiku 2300; chifukwa chake mngeloyo, poyambiranso kufotokoza kwake, anakhazikika kwambiri pa nkhani yokhudza nthawi.”—The *Great Controversy,* p. 325

**c. Kodi ndi nthawi ya iti yomwe inapatulidwira mtundu wa Chiyuda, ndipo n’chiyani chomwe chimayenera kukwaniritsidwa panthawiyo? Danieli 9:24.**

“Uthenga wa ulaliki wa Khristu unali wakuti, ‘Nthawi yakwaniritsidwa, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; lapani, ndipo khulupirirani uthenga wabwino.’ Motero uthenga wabwino, monga momwe unaperekedwera ndi Mpulumutsi Mwiniwake, unachokera pa maulosi. ‘Nthawi’ imene Iye analengeza kuti yakwaniritsidwa inali nthawi imene mngelo Gabrieli anadziwitsa Danieli. . . . Mu ulosi tsiku limodzi limayimira chaka chimodzi. Onani Numeri 14:34; Ezekieli 4:6. Masabata makumi asanu ndi awiri, kapena masiku mazana anayi mphambu makumi asanu ndi anayi, akuyimira zaka mazana anayi mphambu makumi asanu ndi anayi.”—The *Desire of Ages,* p. 233

**a. Kodi ndi lamulo lofunika liti la mfumu lomwe linkasonyeza kuyamba kwa masabata makumi asanu ndi awiri? Danieli 9:25.**

---

"Lamulo lokonzanso ndi kumanga Yerusalemu, monga momwe linamalizidwira ndi lamulo la Artaxerxes Longimanus (onani Ezara 6:14; 7:1, 9, margin), linayamba kugwira ntchito m'dzinja la chaka cha 457 B.C. Kuyambira nthawi imeneyi zaka mazana anayi mphambu makumi asanu ndi atatu ndi zitatu zinafikira m'dzinja la chaka cha 27 A.D." — The *Desire of Ages,* p. 233.

**b. Fotokozani zinthu zomwe zinaperekedwa mu lamulo lomwe linakwaniritsa ulosiwu. Ezara 7:11–13, 21–27.**

---

---

"Ambuye… anakhudza mtima wa mfumu, kotero kuti Ezara anakomeredwa mtima ndi iye. Mfumu inamupatsa njira zambiri zomangiranso kachisi, ndipo iinapanga zotheka kuti Ayuda abwerere kwawo."—The *SDA Bible Commentary* [EG White Comments], vol. 3, p. 1134.

c. **Kodi ulosiwo unaneneratunso chiyani za utumiki wa Mesiya? Danieli 9:26**

---

"Malinga ndi ulosi, nthawi imeneyi inali yoti ifike kwa Mesiya, Wodzozedwayo. Mu A.D 27, Yesu pa ubatizo wake analandira kudzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo posakhalitsa anayamba utumiki wake. Kenako uthenga unalengezedwa. 'Nthawi yakwana.'

"Kenako, anatero mngelo, 'Iye adzatsimikizira pangano ndi ambiri kwa sabata imodzi [zaka zisanu ndi ziwiri].' Kwa zaka zisanu ndi ziwiri Mpulumutsi atayamba utumiki wake, uthenga wabwino unayenera kulalikidwa makamaka kwa Ayuda; kwa zaka zitatu ndi theka ndi Khristu Mwiniwake; ndipo patsogolo pake ndi atumwi. 'Pakati pa sabata Iye adzaletsa nsembe yphera ndi msembe ya ufa.' Danieli 9:27. M'chaka cha AD 31, Khristu nsembe yeniyeni inaperekedwa pa Kavale. Kenako chophimba cha kachisi chinang'ambika pakati, kusonyeza kuti kupatulika ndi kufunika kwa utumiki wopereka nsembe kunatha. Nthawi inali itafika yoti nsembe yophera ndi msembe ya ufa ya padziko lapansi zithe.

Sabata imodzi—zaka zisanu ndi ziwiri—inatha mu chaka cha 34 AD. Kenako mwa kuponya miyala Stefano, Ayuda anatsimikizira kukana kwawo uthenga wabwino; ophunzira omwe anabalalika chifukwa cha chizunzo 'anapita kulikonse akulalikira mawu' (Machitidwe 8:4)." — The *Desire of Ages,* p. 233.

## 5. MASABATA MAKUMI ASANU NDI AWIRI ATSIRIZIDWA — Lachinayi, Meyi 7

**a. Ndi tsoka lotani lomwe lidachitika zaka 490 zitatha? Danieli 9:26 (gawo lomaliza), 27 (gawo lomaliza); Luka 21:20.**

---

"Kuleza mtima kwa Mulungu pa Yerusalemu kunangotsimikizira Ayuda mukusalapa mtima kwawo. . . . Mu khungu komanso kudzikuza kwawo [atsogoleri awo] analengeza poyera kuti sankaopa kuti Yerusalemu adzawonongedwa, chifukwa unali mzinda wa Mulungu mwiniwake. Kuti akhazikitse mphamvu zawo mwamphamvu, anapereka ziphuphu kwa aneneri onyenga kuti alengeze, ingakhale pamene magulu ankhondo achiroma anali kuzungulira kachisi, kuti anthu ayenera kuyembekezera chipulumutso kuchokera kwa Mulungu. Kumapeto kwake, anthu ambiri anakhulupirira kuti Wam'mwambamwamba adzalowererapo kuti adani awo agonjetsedwe. Koma Israyeli anakana chitetezo cha Mulungu, ndipo tsopano analibe tchinjirizo. Yerusalemu wosasangalala! wong'ambika ndi mikangano yamkati, mwazi wa ana ake akuphedwa ndi manja a wina ndi mnzake akuwala m'misewu yake, pamene magulu ankhondo achilendo akugwetsa malinga ake ndi kupha amuna ake ankhondo!"— The *Great Controversy,* pp. 28, 29.

**b. Popeza tamvetsa gawo loyamba la masiku awa, kodi tingazindikire chiyani tsopano? Danieli 8:14; 9:24.**

---

"Kufikira pamenepa, zonse zomwe zafotokozedwa mu maulosi zakwaniritsidwa modabwitsa, ndipo chiyambi cha masabata makumi asanu ndi awiri chakhazikitsidwa mopanda kukayikira pa 457 BC, ndikutha kwawo mu AD 34. Kuchokera pa chidziwitso ichi palibe chovuta mu kupeza mathero a masiku 2300. Masabata makumi asanu ndi awiri—masiku 490—atachotsedwa pa 2300, panali masiku 1810 otsala. Patsogolo pa kutha kwa masiku 490, masiku 1810 anali oti akwaniritsidwe. Kuyambira AD 34, zaka 1810 zinafika mu 1844. Chifukwa chake masiku 2300 a Danieli 8:14 amatha mu 1844. Pakutha kwa nthawi yayikulu yaulosi iyi, motsatira umboni wa mngelo wa Mulungu, 'malo opatulika adzayeretsedwa.' Kotero nthawi yoyeretsa malo opatulika . . . inafotokozedwa momveka bwino ."—Ibid., p. 328.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Meyi 8

1. Ngakhale kuti Danieli mwini anali mneneri, kodi anali wofunitsitsa kumvetsa chiyani?
2. N'chifukwa chani Danieli anadziphatikiza m'mapemphero olapa machimo a Israyeli?
3. Kodi tikudziwa bwanji kuti Danieli 9 akufotokozera momveka bwino chinsinsi cha Danieli 8?
4. Fotokozani chochitika chomwe chinalozera kuyamba kwa ulosi wa zaka 490.
5. Fotokozani kuwonongedwa kwa Yerusalemu, monga momwe Danieli ndi Yesu ananeneratu.

# Buku Losindikizidwa Litsegulidwanso

**VESI LOLOWEZA:** “Ndipo ndinamuka kwa mngelo, ndikunena naye, Ndipatse kabukuko. Ndipo ananena ndi ine, Dzatenge, nudye; ndipo kadzawawitsa m’mimba mwako, komatu m’kamwa mwako kadzazuna ngati uchi.” (Chivumbulutso 10:9).

**Zowerenga Zoonjezera:** *The Great Controversy, pp. 391–408.*

“Mngelo wamphamvu amene analangiza Yohane sanali munthu wocheperapo kuposa Yesu Khristu.”—The *SDA Bible Commentary* [EG White Comments], vol. 7, p. 971

## 1. ANZERU ADZAWARA — Loyamba, Meyi 10

**a. Fotokozani mayesero ndi chipambano chomwe chinaonekera kumapeto kwa masomphenya omaliza a Danieli. Danieli 12:1, 2.**

______________________________________________________________

______________________________________________________________

**b. Kodi anzeru adzaoneka bwanji mosiyana ndi oipa m'tsiku limenelo? Danieli 12:3; Mateyu 13:41–43.**

______________________________________________________________

“Moyo wotembenuka umakhala mwa Khristu. Mdima wake umachoka, ndipo kuwala kwatsopano ndi kwakumwamba kumawala mu moyo wake. ‘Iye amene amapindula miyoyo ndiye wanzeru.’ ‘Ndipo anzeru adzawala ngati kuwala kwa thambo; ndipo iwo amene atembenuza ambiri ku chilungamo adzakhala ngati nyenyezi kwamuyaya.’ Chomwe chimachitika kudzera mu mgwirizano wa anthu ndi Mulungu ndi ntchito yomwe sidzawonongeka, koma idzapitirira mpaka nthawi zosatha. Iye amene amapanga Mulungu kukhala nzeru yake, amene amakula kufikira pa msinkhu wathunthu wa munthu mwa Khristu Yesu, adzaima pamaso pa mafumu, pamaso pa anthu otchedwa akuluakulu a dziko lapansi, ndi kuwonetsa matamando a Iye amene adamuyitana kuti achoke mumdima kupita kuunika kwake kodabwitsa. Sayansi ndi mabuku sizingabweretse mumtima mwa anthu kuwala komwe uthenga wabwino wa Mwana wa Mulungu ungabweretse. Mwana wa Mulungu yekha ndiye amene angachite ntchito yayikulu yowunikira moyo. Nzosadabwitsa kuti Paulo akunena kuti, ‘Pakuti sindichita manyazi ndi uthenga wabwino wa Khristu; pakuti ndi mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa aliyense wokhulupirira.’ Uthenga Wabwino wa Khristu umakhala khalidwe mwa iwo okhulupirira, ndipo umawapanga kukhala makalata amoyo, odziwika ndi owerengedwa ndi *anthu onse.”—Fundamentals of Christian Education,* pp. 199, 200

**a. Kodi Danieli anauzidwa kuchita chiyani tsopano? Danieli 12:4 (gawo loyamba), 8, 9 (gawo loyamba)**

“Atalemekezedwa ndi anthu omwe anali ndi maudindo aboma komanso zinsinsi za maufumu zomwe zinali ndi ulamuliro padziko lonse lapansi, Danieli analemekezedwa ndi Mulungu monga kazembe Wake, ndipo anapatsidwa mavumbulutso ambiri a zinsinsi za mibadwo yamtsogolo. Maulosi ake odabwitsa, monga momwe adalembedwera ndi iye m'mchaputa 7 mpaka 12 a buku lotchedwa dzina lake, sanamvetsetsedwe mokwanira ngakhale ndi mneneri mwiniwake; koma ntchito zake za moyo zisanathe, iye anapatsidwa chitsimikizo chodala chakuti ‘pamapeto a masiku’—m’nthawi yomaliza ya mbiri ya dziko lino—iye adzaloledwanso kuyima pamalo ake. Sikunapatsidwe kwa iye kuti amvetse zonse zomwe Mulungu adavumbulutsa za cholinga chaumulungu. . . .

“Pamene tikuyandikira mapeto a mbiri ya dziko lino, maulosi olembedwa ndi Danieli amafuna chidwi chathu chapadera, chifukwa akukhudzana ndi nthawi yeniyeni imene tikukhalamo. Pamodzi ndi iwo payenera kulumikizidwa ziphunzitso za buku lomaliza la Malemba a Chipangano Chatsopano.”—Prophets *and Kings,* p. 547.

**b. N’chiyani chikusonyeza kuti mawu a mngelo analozera ku chinsinsi cha masiku 2300, ndipo chinsinsi chimenecho chidzabvumbulutsidwa liti? Danieli 8:17; 12:4, 9 (gawo lomaliza).**

---

“Maulosi akupereka zochitika zosiyanasiyana zomwe zikutsogolera ku chiyambi cha chiweruzo. Izi ndi zoona makamaka m’buku la Danieli. Koma gawo la ulosi wake lomwe linali lokhudza masiku otsiriza, Danieli anauzidwa kuti alitseke ndi kulisindikiza ‘mpaka nthawi ya chimaliziro.’ Mpaka titafika nthawi imeneyi, mpamene uthenga wokhudza chiweruzo udzalengezedwe, kutengera kukwaniritsidwa kwa maulosi amenewa. Koma pa nthawi ya chimaliziro, akutero mneneriyo, ‘ambiri adzathamangira uku ndi uku, ndipo chidziwitso chidzawonjezeka.’ Danieli 12:4. . . .

"Kuyambira mu 1798, buku la Danieli chisindikizo chake chinachotsedwa, chidziwitso cha maulosi chawonjezeka, ndipo ambiri analengeza uthenga wofunika kwambiri wa chiweruzo choyandikira."

“Monga momwe zinthu zinalili pa nthawi ya kukonzanso kwakukulu kwa m’zaka za m’ma 1600, gulu la anthu odikira kubwer kachiwir kwa Khristu linaonekera m’maiko osiyanasiyana achikhristu mu nthawi imodzi. Ku Ulaya ndi ku America amuna a chikhulupiriro ndi opemphera anatsogoleredwa kuti aphunzire maulosi, ndipo, pofufuza zolemba zouziridwa, iwo anaona umboni wokhutiritsa wakuti mapeto a zinthu zonse anali pafupi. M’mayiko osiyanasiyana munali magulu a Akristu omwe, mwa kuphunzira Malemba okha, anafika pa chikhulupiriro chakuti kubwera kwa Mpulumutsi kunali pafupi.”—The *Great Controversy,* pp. 356, 357.

**a. Pamene Danieli ankayang'anitsitsa ndi kumvetsera, kodi ndi lamulo lotani lofunika kwambiri lomwe linazindikiritsa nthawi yotsogolera nthawi ya chimaliziro? Danieli 12:5-7.**

---

**b. Kudzera mu kufananiza malemba, zindikirani nthawi ya ulosi uwu Danieli 7:25; Chivumbulutso 11:2, 3; 12:6, 14; 13:5.**

---

“Mtumwi Paulo anachenjeza mpingo kuti usayembekezere kubwera kwa Khristu m’nthawi yake. ‘Tsiku limenelo silidzafika,’ iye anatero, ‘koma pokhapokha patadza chipanduko choyamba, ndipo munthu wa uchimo kudzabvumbulutsidwa.’ 2 Atesalonika 2:3. Kufikira chipanduko chachikulu chitachitika, komanso nthawi yaitali ya ‘Munthu wa uchimo,’ mpamene tingayang’anire kubwera kwa Ambuye wathu. ‘Munthu wa Uchimo’ amene amatchedwanso ‘chinsinsi cha kusayeruzika,’ ‘mwana wa chiwonongeko,’ ndi ‘woipa uja,’ akuyimira upapa, womwe, monga momwe unanenedweratu mu ulosi, uyenera kukhalabe ndi ulamuliro wake kwa zaka 1260. Nthawi imeneyi inatha mu 1798. Kubwera kwa Khristu sikukanatha kuchitika nthawi imeneyo isadutse. Paulo akufotokozera ndi chenjezo lake nthawi ya mbiri yachikhistu mpaka chaka cha 1798. Ndi mbali iyi ya nthawi imeneyo pamene uthenga wa kubwera kwachiwiri kwa Khristu uyenera kulengezedwa.”—The *Great Controversy,* p. 356.

**c. Kodi nthawi ya zaka 1260 inafotokozedwa motani ndi mngeloyo? Danieli 12:10 (gawo loyamba).**

---

---

“M’zaka za m’ma 1300, injini yoopsa kwambiri ya apapa inakhazikika—Kafukufuku. Kalonga wa mdima ankagwira ntchito limodzi ndi atsogoleri a ulamuliro wa papa. M’maupo awo achinsinsi Satana ndi angelo ake ankalamulira maganizo a anthu oipa, pomwe pakati pawo panali mngelo wa Mulungu, akutenga mbiri yoopsa ya malamulo awo oipa ndikulemba mbiri ya zochita zoopsa kwambiri kuti anthu azione. ‘Babulo Wamkulu’ anali ‘ataledzera ndi magazi a oyera mtima.’ Mitundu yophwanyika ya anthu mamiliyoni ambiri omwe anaphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo inafuulira kwa Mulungu kuti alange mphamvu yampatuko imeneyo. . . .

“Mkhalidwe wa dziko lapansi pansi pa ulamuliro wa Aroma unapereka kukwaniritsidwa koopsa komanso kodabwitsa kwa mawu a mneneri Hoseya. . . . ‘Palibe choonadi, kapena chifundo, kapena kudziwa Mulungu m’dzikomo. Mwa kulumbira, ndi kunama, ndi kupha, ndi kuba, ndi kuchita chigololo, amapatuka, ndipo mwazi umakhudza mwazi.’ Hoseya 4:6, 1, 2. Izi zinali zotsatira za kuchotsa mawu a Mulungu.”—Ibid., pp. 59, 60

## 4. BUKU LITSEGULIDWA

**a. Poona kufanana ndi Danieli 12:7, kodi mneneri Yohane anaona bwanji kutsegulidwa kwa masomphenya osindikizidwa a Danieli? Chivumbulutso 10:1, 2, 5, 6.**

“Mngelo wamphamvu amene analangiza Yohane sanali wocheperapo kuposa Yesu Khristu. Kuika phazi lake lamanja panyanja, ndi lamanzere lake pamtunda wouma, kumasonyeza gawo limene Iye akuchita m’zochitika zomaliza za mkangano waukulu ndi Satana. Udindo umenewu ukusonyeza mphamvu zake zazikulu ndi ulamuliro wake padziko lonse lapansi. . . .

“Yohane akuona kabuku kakang’ono kakutsegulidwa. Kotero maulosi a Danieli ali ndi malo ake oyenera mu mauthenga a angelo oyamba, achiwiri, ndi achitatu omwe ayenera kuperekedwa kudziko lapansi. Kutsegulidwa kwa kabuku kakang’ono kunali uthenga wokhudzana ndi nthawi. . . .

"Nthawi iyi, yomwe mngelo akulengeza ndi lumbiro lalikulu, si mapeto a mbiri ya dziko lino, kapena kutsekedwa kwa chitetezero, koma kwa nthawi yaulosi, yomwe ili pa mbuyo pa kubwera kwa Ambuye wathu. Ndiko kuti, anthu sadzakhala ndi uthenga wina wokhudza nthawi yeniyeni. Patsogolo pa nthawi imeneyi, kufika mu . 1844, sipangakhale kutsata kotsimikizika kwa nthawi yaulosi. Chiwerengero cha nthawi yayitali kwambiri chikufika mu nthawi yophukira ya 1844."

“Kuima kwa mngelo, phazi limodzi panyanja, lina pamtunda, akusonyeza kukula kwa kulengeza kwa uthengawo. Udzawoloka madzi ambiri ndipo udzalengezedwa m’maiko ena, ngakhale padziko lonse lapansi.” —*The SDA Bible Commentary* [EG White Comments], vol. 7, p. 971.

**b. Fotokozani momwe zomwe Yohane adakumana nazo m'masomphenya akudya kabuku kakang'ono zinali zofanana ndi zomwe zinachitika mu gulu lomwe la Advent Movement la m'ma 1840. Chivumbulutso 10:9–11.**

“Kumvetsetsa choonadi, kulandira uthenga mosangalala, kumaimiridwa mu kudya buku laling’ono. Chowonadi chokhudza nthawi ya kubwera kwa Ambuye wathu chinali uthenga wamtengo wapatali ku miyoyo yathu.” —Ibid.

"Nthawi yoyembekezera inapita, ndipo Khristu sanawonekere kuti apulumutse anthu Ake. Iwo amene ndi chikhulupiriro chenicheni ndi chikondi anali kufunafuna Mpulumutsi wawo, nakumana ndi kukhumudwa kowawa. Komabe zolinga za Mulungu chinali chikwaniritsidwa; Iye anali kuyesa mitima ya iwo amene ankati akuyembekezera kuwonekera Kwake. . . .

“Koma Yesu ndi khamu lonse lakumwamba linayang’ana mwachikondi ndi chifundo anthu oyesedwa komanso okhulupirika koma okhumudwa. Chophimba cholekanitsa dziko looneka ndi losaoneka chikanachotsedwa, angelo akanawoneka akuyandikira miyoyo yolimbayi ndikuiteteza ku njira za Satana.”—The *Great Controversy,* p. 374

## 5. Pakati pa Anzeru — Lachisanu, Meyi 14

**a. Kodi Danieli anafotokozedwa bwanji ndi Ezekieli, mmodzi wa anthu a m'nthawi yake? Ezekieli 14:14.**

---

**b. Kodi tingakhale bwanji pakati pa anzeru monga momwe Danieli analili? Danieli 12:10 (gawo lomaliza); Miyambo 9:10; Mateyu 7:24, 25**

---

---

“Nthawi ya mavuto, yomwe sinachitikepo,’ ikubwera posachedwa; ndipo tidzafunika mbiri ya zodutsamo yomwe tilibe tsopano ndipo ambiri ndi aulesi kwambiri kuti aipeze. Nthawi zambiri mavuto amakhala aakulu pamene akuyembekezedwa kuposa m’zenizeni; koma izi sizili choncho pamavuto omwe ali patsogolo pathu. Kufotokozera bwino chithunzi thunzi cha zimenezi sikungafikire kukula kwa vuto ili. Mu nthawi imeneyo ya mayesero, munthu aliyense ayenera kuyimirira yekha pamaso pa Mulungu. ‘Ngakhale Nowa, Danieli, ndi Yobu’ anali m’dzikolo, ‘Pali Ine, akutero Ambuye Mulungu, sadzapulumutsa mwana wamwamuna kapena wamkazi; adzapulumutsa miyoyo yawo yokha ndi chilungamo chawo.’ Ezekieli 14:20

“Tsopano, pamene Mkulu wa Ansembe wathu wamkulu akupembedzera machimo athu, tiyenera kuyesetsa kukhala angwiro mwa Khristu. Ngakhale ndi lingaliro, Mpulumutsi wathu sanagonjetsedwe ndi mphamvu ya mayesero. Satana amapeza m’mitima ya anthu malo ena kumene angapeze malo; chilakolako china cha uchimo chimasungidwa, mwa njira imene mayesero ake amasonyezera mphamvu zawo. Koma Khristu analengeza za Iye mwini kuti: ‘Kalonga wa dziko lino lapansi akubwera, ndipo alibe kanthu mwa Ine.’ Yohane 14:30. Satana sakanapeza kalikonse mwa Mwana wa Mulungu komwe kakanamuthandiza kupambana. Iye anasunga malamulo a Atate wake, ndipo panalibe tchimo mwa Iye limene Satana akanatha kugwiritsa ntchito ku chipindulo chake. Umu ndi momwe anthu omwe adzayime nthawi ya mavuto ayenera kukhalira.”— The *Great Controversy,* pp. 622, 623.

**c. Kodi mngelo potsiriza anasiyana naye Danieli motani? Danieli 12:13.**

---

---

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachasanu n’chimodzi 15

1. Kodi kuuka kwa akufa a mu Danieli 12:2 kudzachitika liti?
2. N’chiyani chinachitika kuti ulosi wa Danieli utsegulidwe?
3. Ndi chochitika chiti chomwe chinasonyeza kuyamba kwa nthawi ya ku mapeto?
4. Ndi ulosi uti umene unavumbulutsa chiyambi cha buku la Danieli?
5. Kodi ndingatsimikize bwanji kuti ndili pakati pa anzeru?

LASABATA, MAY 23, 2026

PHUNZIRO 8

# Mneneri Wa Ku Patimosi

**VESI LOLOWEZA:** *‘Koma m’modzi wa akuphunzira ake, amene Yesu anamkonda, anali kutsamira pa chifuwa cha Yesu’* [Yohane 13;23].

**Zowelenga Zoonjezera:** *The Acts of the Apostles,* pp.539-556.

“Pambuyo pa kukwera kwa Yesu kupita kumwamba, Yohane anaima ngati mtumiki okhulupirika, ogwira ntchito molimbika kwa Ambuye.” –*The Acts of the Apostles,* p.546.

## 1. OPHUNZIRA YEMWE YESU ANAMKONDA — Loyamba, May 17

**a. Ndizitsanzo ziti zomwe zimasonyeza kuti mtumwi Yohane anali pafupi ndi Yesu? Mateyu 17:1; Maliko14:33; Luka 8:51.**

______________________________________________

______________________________________________

“[Yohane] anaoneka kukhala osangalala kwambiri ndi ubwenzi wa Khristu, ndipo analandira umboni wammbiri wachidaliro ndi chikondi cha mpulumutsi. Iye anali mmodzi wa atatu aja omwe analoledwa kuchitira umboni za ulemelero wa Khristu pa phiri la kusandulika kwake mu Getsemane, ndipo chinali chifukwa chimenechi kuti Ambuye wathu anapereka amayi ake kuchisamaliro chake mu maola otsiriza a zowawa pa mtanda.”- *The Acts of Apostles,* p.539.

**b. Ndimotani m’mene Yohane amazindikirika pakati pa ophunzira aja? Yohane 13:23; 21:20 [mbali yoyamba], 24.**

______________________________________________

“Yohane ndi Yakobo, Andreya ndi Petro, limodzi ndi Filipo, Natanayeli, ndi Mateyu, anali ogwirizana kwambiri ndi Iye kuposa ena onse, ndipo anaona zozizwitsa Zake zambiri. Petro, Yakobo, ndi Yohane anaima paubale wapafupi ndi Iye. Iwo anali pafupi ndi Iye nthawi zonse, kuchitira umboni zozizwitsa Zake, ndi kumva mawu Ake. Yohane anakhala woyandikana kwambiri ndi Yesu, ndipo ndichifukwa chake akudziwika monga munthu amene Yesu anamkonda. Mpulumutsi anawakonda onse, koma mzimu wa Yohane unali womvera kwambiri. Iye anali wamng’ono kuposa enawo, ndipo ndi chikhulupiriro chochuluka chonga cha mwana anapereka mtima wake kwa Yesu. Chotero iye anafika mu chifundo chachikulu ndi Khristu, ndipo kupyolera mwa iye chiphunzitso chakuya chauzimu cha Mpulumutsi chinaperekedwa kwa anthu Ake.”-*The Desire of Ages,* p..22.

**a. Kodi dzina limene Yesu anapatsa Yohane ndi m'bale wake Yakobo limatanthauza chiyani? Maliko3:17.**

________________________________________________________________

"Yohane mwachibadwa analibe khalidwe labwino lomwe linadzabvumbuluka mtsogolo mwake. Mwachibadwa anali ndi zilema zazikulu. Iye sanali wonyada, wodzikuza, ndi wofuna ulemu kokha ayi, komanso anali wopupuluma, ndi waukali povulazidwa. Iye ndi mbale wake ankatchedwa 'ana a bingu.' Kupsa mtima koipa, chikhumbo cha kubwezera, mzimu wokonda kudzudzula, zonse zinali mwa wophunzira wokondedwayo. Koma pansi pa zonsezi Mphunzitsi waumulunguyo anazindikira mtima wachangu, wowona, ndi wachikondi. Yesu anadzudzula kudzikonda kwake, kukhumudwitsa zokhumba zake, kuyesa chikhulupiriro chake. Koma Iye anamuululira chimene moyo wake unkalakalaka—kukongola kwa chiyero, mphamvu yosintha ya chikondi."-*The Acts of Apostles,* p. 540.

**b. Ndimotani mmene Yohane anaphunzirira njira yatsopano yolumikizanirana ndi ena? Yohane 13:34;1 Yohane 4:7,8.**

________________________________________________________________

"Maphunziro a Khristu, kuwonetsera kufatsa, kudzichepetsa ndi chikondi ngati zinthu zofunikira kwambiri pa kukula m'chisomo ndi kukhala oyenera kugwira ntchito yake, zinali zamtengo wapatali kwambiri kwa Yohane. Anatenga phunziro lililonse kukhala lapamwamba ndipo nthawi zonse ankaganiza zobweresa moyo wake muchiyanjano ndi kumwamba. Yohane anayamba kuzindikira mwa nzeru za ulemerelo wa Khristu, osati ngati olamulira wa dziko ndi mphamvu monga anakhala akuphunzitsiridwa ndikuyembekezera, koma monga Mwana obadwa yekha wa Atate odzala ndi chifundo ndi choonadi.' Yohane1:14." -Ibid, p.544.

**c. Fotokozani zotsatira za mtima odzala ndi chikondi cha pa abale. 1 Yohane 3:10,11; Yohane 13:35.**

"Kuzama ndi kulimba kwa chikondi chimene Yohane anali nacho kwa Mbuye wake, sizomwe zinapangitsa kuti Khristu amukonde iye, koma chotsatira cha chikondicho. Yohane anafuna kukhala monga Yesu, ndipo pakusitha kokudza kamba kachikondi cha Khristu, anakhala ofatsa ndi odekha. Undekha unabisika mwa Khristu. Koposa anzake onse, Yohane anadzipereka yekha ku mphamvu ya moyo opambanawo…. Yohane anamudziwa mombolo kudzera mukukhala naye pafupi. Maphunziro a Mbuye wake anakhazikika mu moyo wake. Pamene anachitira umboni za chisomo cha Mpulumutsi, mawu ake anali okhulupirika komanso omveka bwino ndi chikondi chotumphukira mu mzimu wake." -Ibid, pp. 544,545.

## 3. APONYEDWA KU PATIMO

Lachitatu, May 19

**a. Atalephera kuchotsa moyo wa Yohane, kodi ndikuti komwe anamutumiza? Chibvumbulutso 1:9.**

"Yohane …... anaitanidwa ku Rome kuti akayesedwe pa chikhulupiriro chake. Kumeneku pamaso pa olamulira, chiphunzitso cha mtumwiyu chinali kupototozedwa. Mboni zabodza zinamuneneza mlandu wakuti ankaphunzitsa ziphunzitso zopotoka zotsutsana ndi boma. Kudzera muzomuneneza zimenezi adani ake adayembekezera kuti zikhoza kupangitsa kuti wophunzirayu aphedwe.

"Yohane anayakha mwa yekha mu njira yomveka bwino ndi yokopa, yophweka ndi yoona mtima kotero kuti mawu ake anali ndi zotsatira za mphamvu. Omumvera ake anadabwa ndi nzeru yake ndikuyankhula kwake kwapamwamba. Koma pamene umboni wake umakhala opatsa chidwi, mkwiyo ndi chidani cha omutsutsa ake zinali kukulirakulirabe.

"Yohane anaponyedwa mu mphika wamafuta owira; koma Mulungu anasamalira moyo wa kapolo wake okhulupirikayu monga mmene anatetezera Aheberi atatu aja mng'anjo yamoto. Monga mmene mawu anayankhulidwa, (Yesu khristu wa ku nazareti), kuti akaononge onse okhulupirira onyengayu, Yohane anafotokoza kuti, Mbuye wanga moleza mtima anavomereza zonse zomwe satana ndi angelo ake anakonza kuti mukandizuze ndikunditonza. Anapereka moyo wake kuti akapulumutse dziko. Ndalemekezeka polola kuvutika muchifuniro chake….

"Mawu awa anali ndi chikoka champhanvu. Yohane anatulutsidwa mu mphika uja ndi amuna omwe anamulowetsamo aja. Muulamuliro wa mfumu, Yohane anathamangitsidwira pa chilumba cha Patimo…. Adani ake ankaganiza kuti chikoka chake sichidzamvedwanso ndipo ayenera kufa ndi chisautso ndi mavuto."–*The Acts of the Apostle,* pp. 569,570.

**b. Kodi kuthamangitsidwa kwake kunabwereretsa mwayi waukulu wotani? Chibvumbulutso 1:1-3,10,11.**

Patimo, chilumba chamiyala ndi chopanda kanthu m'nyanja ya Aegean, Anasankhidwa ndi ulamulirro wa chiRoma monga malo othamangitsirako anthu olakwa; koma malo okhala a mdima ndi achisoniwa anakhala khomo la kumwamba la kapolo waMulungu. Pano, atatsekeredwa kutali ndi zotangwanitsa za moyo komanso ntchito zomwe ankagwira mu zaka zapitazo, iye anakhala akulumikizana ndi Mulungu, ndi Khristu komanso angelo akumwamba, ndipo mwa iwowa iye analandira malagizo a mipingo yonse yanthawi yamtsogolo. Zochitika zomwe zikuyenera kukwaniridwa kumapeto kwa mbiri ya dziko lapansi lino zinayalidwa mowoneka bwino pamaso pake; ndipo kumeneko iye analemba masophenya omwe anawonetsedwa ndi Mulungu."-*Ibid,* pp.570,571.

**a. Ndimotani momwe Yesu anawonekera kwa Yohane mmasophenya pa Patimo? Chibvumbulutso 1:12-16.**

---

[Wophunzira wokondedwayo] anawona Mbuye wake m'Getsemane, nkhope Yake yodzala ndi madontho a mwazi wa zowawa, 'nkhope yake . . . yoonongeka koposa munthu aliyense, ndi maonekedwe ake koposa ana a anthu.' Yesaya 52:14 . Anamuona m'manja mwa asilikali achiroma, atavala mwinjiro wakale wa chibakuwa, ndi korona waminga. Anamuwona Iye atapachikidwa pa mtanda wa Kalvare, chinthu chonyozedwa ndi nkhanza. Tsopano Yohane waloledwanso kuona Ambuye wake. Koma mawonekedwe Ake asintha bwanji! Salinso Munthu wachisoni, wonyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu. Wabvekedwa chobvala chonyezimira chakumwamba. . . . Patmo akuwala ndi ulemerero wa Ambuye woukitsidwayo."-*The Acts of the Apostles,* p.582.

**b. Kodi Yohane anachita bwanji, nanga ndi ntchito yanji yomwe Yesu anamupatsa iye? Chibvumbulutso 1:17-19.**

"Yohane analimbikitsika kukhala pamaso pa Ambuye wake olemekezeka. Pambuyo pa masophenya ake odabwitsa ulemelero wammwamba unatseguka. Analoledwa kuona mpando wachifumu wa Ambuye, ndipo poyang'ana mopitilira nkhondo za dziko lapansi, anaona gulu lalikulu la owomboledwa atabvala zobvala zoyera. Anamva nyimbo za angelo akumwamba ndi nyimbo zogonjetsa za iwo amene anagonjetsa ndi mwazi wa Mwana wa Nkhosa ndi mawu aumboni wawo. Mu vumbulutso lopatsidwa kwa iye munali chochitika chofutukuka pambuyo pa chochitika chochititsa chidwi mu zochitika za anthu a Mulungu, ndi mbiri ya mpingo inanenedweratu mpaka kumapeto kwenikweni kwa nthawi. M'mafanizo ndi zophiphiritsa, nkhani zofunika kwambiri zinaperekedwa kwa Yohane, zimene anayenera kulemba, kuti anthu a Mulungu okhala m'nthaŵi yake ndi m'mibadwo yam'tsogolo akazindikire mwanzeru mavuto ndi mikangano imene inali patsogolo pawo."- *Ibid,* p.582-583.

**c. Ndimotani mmene buku la Chivumbulutso liliri uthenga kwa ife patokha? Chibvumbulutso 1:4-6; 3:22.**

"Vumbulutso limeneli linaperekedwa kaamba ka chitsogozo ndi chitonthozo cha mpingo m'nyengo yonse ya Chikristu." Komabe aphunzitsi achipembedzo alengeza kuti ilo ndi bukhu lomatidwa ndipo zinsinsi zake sizingafotokozedwe. Chotero ambiri apatuka pa cholembedwa chaulosi, kukana kuthera nthaŵi ndi kuphunzira ku zinsinsi zake. Koma Mulungu sakufuna anthu ake adziliona chotero bukhuli."- *Ibid,* p.583.

## 5. KUPEZEKA KWA KHRISTU KUTSIMIKIZIDWA — Lachisanu, May 21

**a. Kodi masomphenya a Khristu ali pakati pazoikapo nyali zisanu ndi ziwiri za golide amatanthawuza chiani? Chivumbulutso 1:20.**

"Khristu akunenedwa kuti akuyenda pakati pa zoyikapo nyali zagolide. Izi zikuyimira ubale wake ndi mipingo. Iye amalumikizana ndi anthu ake. Amadziwa chenicheni chimene iwo ali. Amaona dongosolo lawo, kupembedza kwawo, ndi kudzipereka kwawo. Ngakhale kuti Iye ali Mkulu wa Ansembe ndi Mkhalapakati m'kachisi wakumwamba, akuyimiridwabe ngati akuyenda pakati pa mipingo yake padziko lapansi. Ndi maso osatopa ndi chenjezo losalekeza, amawunika kuona ngati kuwala kwa alonda ake kuli kufooka kapena kuli pafupi kuzima. Ngati zoyikapo nyali zikanasiyidwa m'manja mwa anthu okha, lawi lofewa likanachepa ndi kuzima; koma Iye ndi mlonda woona m'nyumba ya Yehova, woyang'anira woona wa bwalo la kachisi. Kusamalira kwake kosalekeza ndi chisomo chake chothandiza ndizo gwero la moyo ndi kuwala."— *The Acts of the Apostles,* p. 586.

**b. Fotokozani cholinga cha mauthenga a Mulungu ku mpingo wonse, womwe ukuimiridwa ndi mipingo isanu ndi iwiri mu Chibvumbulutso 2 ndi 3.**

"Mayina a mipingo isanu ndi iwiri ndi chizindikiro cha mpingo m'nthawi zosiyanasiyana za nthawi ya Chikhristu. Nambala 7 ikusonyeza kukwanira, ndipo ndi chizindikiro chakuti mauthengawa akufikira mpaka kumapeto kwa nthawi, pamene zizindikiro zomwe zagwiritsidwa ntchito zikuwonetsa khalidwe la mpingo m'nthawi zosiyanasiyana za mbiri ya dziko lapansi."— *Ibid,* p.585.

"Mpingo unali ndi zolakwa ndipo unafunikira kudzudzulidwa mwamphamvu ndi kulangidwa, ndipo Yohane analimbikitsidwa kulemba mauthenga a chenjezo, kudzudzula, ndi kupempha kwa iwo amene, posiya kuona pa mfundo zofunika za uthenga wabwino, ankayika pa ngozi chiyembekezo chawo cha chipulumutso. Koma nthawi zonse mawu a kudzudzula amene Mulungu amaona kuti ndi ofunika kutumiza amalankhulidwa ndi chikondi chofatsa komanso ndi lonjezo la mtendere kwa wokhulupirira aliyense wolapa."— *Ibid,* p.587.

## MAFUNSO OBWEREZA PA WEKHA — Lachisanu n'chimodzi, May 22

1. Ngakhale Yesu analibe okondedwa ake apadera, n'chifukwa chani Yohane ankatchedwa ophunzira wokondedwaa?
2. Kodi ndi chani chinabweretsa kusintha mu khalidwe ndi moyo wa Yohane?
3. Kodi Mulungu anasokoneza bwanji zolinga za anthu oipa omwe anayesa kuthana ndi Yohane?
4. Ngakhale nthawi zambiri buku la Chibvumbulutso limatchedwa lotsekedwa, kodi limatanthauza chani kwa ife?
5. Fotokozani cholinga cha Mulungu potumiza uthenga odzudzula mpingo wake.

LASABATA, MEYI 30,2026

PHUNZIRO 9

# Chinjoka, Nkazi, ndi Otsala

**Vesi Loloweza:** "Ndipo chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nichinachoka kunka kukachita nkhondo ndi otsala a mbeu yake, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nawo umboni wa Yesu ." (Chivumbulutso 12:17).

**Zowerenga Zoonjezera:** The Great Controversy, pp. 582–592.

"Ufulu wa chikumbumtima, umene unalipiridwa ndi nsembe yaikulu kwambiri, sudzalemekezedwanso. Mu mkangano womwe ukubwera posachedwa, tidzaona kukwaniritsidwa kwa mawu a mneneri." — The Great Controversy, pp. 592.

## 1. MPINGO UULULIDWA

**Loyamba, Meyi 24**

**a. Kodi chikuwoneka ndi chiyani pa chiyambi pa masomphenya achinayi a Yohane? Chivumbulutso 12:1.**

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

**b. Mu chizindikiro cha m'Baibulo, kodi mkazi amaimira chiyani? 2 Akorinto 11:2; Ezekieli 23:2–4; Chivumbulutso 17:3–6.**

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

"Mu Chivumbulutso 17, Babulo amaimiridwa ngati mkazi—chithunzi chomwe chimagwiritsidwa ntchito m'Baibulo kuimira mpingo. Mkazi wangwiro amaimira mpingo woyera, ndipo mkazi woipa amaimira mpingo wakugwa.

"M'Baibulo, khalidwe lopatulika komanso lokhalitsa la ngwirizano umene ulipo pakati pa Khristu ndi mpingo wake umaimiridwa ndi mgwirizano wa ukwati. Ambuye walumikiza anthu Ake kwa Iye mwa pangano lokhazikika; Iye analonjeza kukhala Mulungu wawo, ndipo iwo analonjeza kukhala Ake, Ake okha. Iye akunena kuti: 'Ndipo ndizakutomera kuti ukhale wanga kosatha; inde, ndidzakutomera ukhale wanga m'chilungamo, ndi m'chiweruzo, ndi m'ukoma mtima, ndi m'chifundo.' (Hoseya 2:19). Ndiponso: 'Ine ndizakutengerani inu kuziyoni.' (Yeremiya 3:14). Ndipo Paulo amagwiritsa ntchito chithunzi chomwechi mu Chipangano Chatsopano pamene akunena kuti: 'Ndakupalitsani ubwenzi kwa mwamuna mmodzi, kuti ndikalangize inu ngati namwali woyera mtima kwa Khristu.' 2 Akorinto 11:2." — The Great Controversy,p. 381.

**a. Kodi mpingo unadutsa mu masautso otani poyembekezera kubadwa kwa Mesiya? Chivumbulutso 12:2; Yesaya 9:6; Luka 2:25–32.**

---

---

“Mawu omaliza a Yakobo atatsala pang’ono kufa amadzaza [okhulupirika pakati pa Ayuda] ndi chiyembekezo: ‘Ndodo yaufumu sidzachoka mwa Yuda, kapena wolamulira pakati pa mapazi ake, kufikira Silo adzabwera.’ (Genesis 49:10). Kusika pansi kwa mphanvu za Israeli zimasonyeza kuti kubwera kwa Mesiya kunali pafupi. Ulosi wa Danieli unasonyeza ulemerero wa ufumu wake pa ufumu umene udzagonjetsa maufumu onse a padziko lapansi; ndipo mneneriyo anati, ‘Udzakhazikika kosatha.’ (Danieli 2:44). Ngakhale ochepa anamvetsa chikhalidwe cha utumiki wa Khristu, panali kuyembekezera kwakukulu kwa kalonga wamphamvu amene adzakhazikitse ufumu wake mu Israeli, ndipo adzabwera monga Mpulumuts i wa mitundu.”

“Mapeto a nthawi afika. Mtundu wa anthu, womwe waipisisa chifukwa cha uchimo wa mibadomibado, ukuitanitsa ku kubweranso kwa mombolo.” — The Desire of Ages, p.34.

**b. Kodi ndi mphamvu yanji ya boma imene ikuimiridwa ndi chinjoka chachikulu chofiira? Chivumbulutso 12:3.**

---

---

“Pansi pa zizindikiro za chinjoka chachikulu chofiira, chilombo chonga nyalugwe, ndi chilombo chokhala ndi nyanga ngati za mwanawankhosa, maboma a padziko lapansi amene makamaka azasogerera mukuphwanya malamulo a Mulungu ndi kuzunza anthu ake anaonetsedwa kwa Yohane.” — SDA Bible Commentary [E. G. White comments], vol 7, p. 972.

**c. Chifukwa cha mphamvu yonga ya chinjokayi, ndi chiwopsezo chotani chimene mpingo ndi Mesiya anakumana nacho? Chivumbulutso 12:4.**

---

---

“Satana wakhala akugwira ntchito kuti apange pompho kukhala lakuya komanso losatheka kuwoloka pakati pa dziko lapansi ndi kumwamba. Kudzera mu mabodza ake analimbikitsa anthu mu uchimo. Cholinga chake chinali kuchotsa kuleza mtima kwa Mulungu, ndi kuzimitsa chikondi chake kwa anthu, kuti Iye asiye dziko lapansi, pansi pa ulamuliro wa Satana.” — The Desire of Ages, p. 34, 35.

“Satana kumwamba amamuda Khristu chifukwa cha udindo wake m’mabwalo a Mulungu. Anadana naye kwambiri pamene iye mwini anachotsedwa pa udindo wake. Anamuda Iye amene analonjeza kuwombola mtundu wa ochimwa. Komabe m’dziko limene Satana amati ndi lake, Mulungu analola mwana wake kubwera, ngati khanda losowa thandizo, logonjera kufooka kwa umunthu. Anamulola kuti akumane ndi zoopsa za moyo monga munthu aliyense, kumenya nkhondo monga mwana aliyense wa munthu ayenera kulimbana nayo, pachiopyezo cholephera ndi kutayika kwamuyaya.” — **Ibid., p. 49.**

**a. Kodi ndi chidziwitso chotani cha m'mbuyomo chimene chinaululidwa kwa Yohane, ndipo chimatanthauza chiyani? Chivumbulutso 12:7–9.**

---

"Kutsutsa lamulo la Mulungu kunayambira m'mabwalo a kumwamba, ndi Lusifala, kerubi wophimba. Satana anatsimikiza kukhala woyamba m'maulangizi a kumwamba, ndi kukhala wofanana ndi Mulungu. Iye anayamba ntchito ya chipanduko ndi angelo amene anali pansi pa ulamuliro wake, kufalitsa mzimu wosakhutitsidwa pakati pawo. Ndipo anagwira ntchito mwachinyengo kwambiri kotero kuti angelo ambiri anakhala kumbali yake asanadziwe bwinobwino zolinga zake. Ngakhale angelo okhulupirika sanamvetse mokwanira khalidwe lake kapena kuona kumene ntchito yake inkapita. Pamene Satana anapambana kukopa angelo ambiri kumbali yake, anaitengera nhani yake kwa Mulungu, kunena kuti linali khumbo la angelo kuti iye atenge malo amene Khristu anali nawo.

"Zoipazo zinapitiriza kugwira ntchito mpaka mzimu wosakhutira unakhwima n'kukhala chipanduko chowonekera. Kenako panali nkhondo kumwamba, ndipo Satana, limodzi ndi onse amene anamumvera, anathamangitsidwa." — SDA Bible Commentary [E. G. WhiteComments], vol. 7, pp. 972, 973.

**b. Kodi chilengezo cha pa Chivumbulutso 12:10, 11 chikuwonetsa bwanji kukwaniritsidwa kwa kuthamangitsidwa kwa Satana pa nthawi ya utumiki wa Yesu?**

---

"Ndi maso aulosi, Khristu anaona zochitika zimene zidzachitike mu nkhondo yake yayikulu yomaliza. Iye ankadziwa kuti akadzafuula kuti, 'Kwatha,' kumwamba konse kudzapambana. Khutu lake linamva kale nyimbo zakutali ndi kufuula kwa chigonjetso m'mabwalo a kumwamba. Iye ankadziwa kuti belu lolira la mapeto a ufumu wa Satana lidzamenyedwa, ndipo dzina la Khristu lidzalengezedwa kuchokera ku dziko lina kupita ku lina m'chilengedwe chonse." — The Desire of Ages, p. 679.

"Dongosolo la chiwombolo linali ndi cholinga chachikulu komanso chakuya kuposa kupulumutsa munthu. Sikuti chifukwa chimenechi chokha Khristu anabwera padziko lapansi; osati kungoti okhala m'dziko laling'ono lino alemekeze lamulo la Mulungu monga liyenera kulemekezedwera; koma kunali kutsimikizira khalidwe la Mulungu pamaso pa chilengedwe chonse. … Ntchito ya Khristu yakufa kuti apulumutse munthu sinali kungotsegulira anthu mwayi wopita kumwamba, koma pamaso pa chilengedwe chonse inali yolungamitsa Mulungu ndi mwana wake pa mmene anachitira ndi chipanduko cha Satana. Inakhazikitsa kuti lamulo la Mulungu ndi losatha, ndipo inawulula chikhalidwe ndi zotsatira za uchimo." — Patriarchs and Prophets, pp. 68, 694.

**a. Ndi chiwopsezo chowonjezereka chotani chimene tsopano chikuperekedwa ku mpingo? Chivumbulutso 12:12, 13.**

“Satana, podziwa kuti ufumu umene analanda pamapeto pake udzachotsedwa kwa iye, anatsimikiza kuti sadzalekerera, koma adzayesetsa kuwononga onse omwe Mulungu analenga m’chifanizo chake. Anada munthu chifukwa Khristu anasonyeza chikondi chachikulu chomukhululukira ndi kumuchitira chifundo; ndipo tsopano iye anakonzekera kugwiritsa ntchito mitundu yonse ya chinyengo kuti kudzera muzinyengo zimenezi iwo akataike. Iye analimbikira machitidwe ake ndi mphamvu zambiri chifukwa cha kusowa kwake chiyembekezo.” — SDA Bible Commentary [ E. G. White Comments], vol. 7, pp. 973, 974.

“Mkangano waukulu pakati pa chabwino ndi choipa udzawonjezereka mphamvu kumapeto kwa nthawi. M’mibadwo yonse, mkwiyo wa Satana wakhala ukuonekera motsutsana ndi mpingo wa Khristu; ndipo Mulungu wapereka chisomo chake ndi Mzimu wake kwa anthu ake kuti awalimbikitse kuyima motsutsana ndi mphamvu ya woipayo. Pamene atumwi a Khristu ankayenera kunyamula Uthenga Wabwino wake kupita ku dziko lapansi ndi kuwulemba kuti mibadwo yonse idzawerenge, anapatsidwa kuunika kwapadera kwa Mzimu. Koma pamene mpingo ukuyandikira kuchiombolo chake chomaliza, Satana adzagwira ntchito ndi mphamvu yowonjezereka. … Ndipo luso lonse la Satana, chinyengo chake chonse, ndi nkhanza zonse zimene zinakuzika, m’nkhondo za mibadwo, zidzagwiritsidwa ntchito motsutsana ndi anthu a Mulungu mu mkangano womaliza. Ndipo pa nthawi ya chiwopsezochi, otsatira a Khristu ayenera kupereka chenjezo la kubwera kwachiwiri kwa Ambuye ku dziko lapansi; ndipo anthu ayenera kukonzekeretsedwa kuti adzayime pamaso Pake pa kubwera Kwake, ‘opanda chilema, ndi opanda banga.’ (2 Petro 3:14). Pa nthawi imeneyi mphatso yapadera ya chisomo chaumulungu ndi mphamvu ikufunika kwambiri kuposa mmene zinalili m’nthawi ya atumwi.” — The Great Controversy, pp. ix, x.

**b. Fotokozani zimene mpingo unakumana nazo m’nthawi ya zaka chikwi, mazana awiri, mphambu zisanu ndi chimodzi( 1,260) za kuponderezedwa ndi kuzunzidwa. Chivumbulutso 12:6, 14.**

**c. Ndi chithandizo chotani chimene chinabwera kuti chilepheretse chiwembu cha zida za anthu zimene chinjoka chinkafuna kugwiritsa ntchito motsutsana ndi okhulupirika? Chivumbulutso 12:15, 16.**

“Pamene uthenga unafalikira m’mayiko a ku Ulaya wokhudza dziko limene munthu aliyense akanatha kusangalala ndi zipatso za ntchito yake ndi kutsatira zimene chikumbumtima chake chikumuuza, anthu zikwi ndi zikwi anafika m’mphepete mwa dziko latsopano .” —Ibid,p.296.

## 5. OTSALA — Lachisanu, Meyi 28

**a. Pamene mkwiyo wa chinjoka ukufika pachimake, okhulupirika akufotokozedwa bwanji? Chivumbulutso 12:17.**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

“Wolemba wa Chivumbulutso, poyang’ana m’masiku a mtsogolo kufikira kumapeto kwa nthawi, analengeza kuti, ‘Ndipo Chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nicinachoka kukachita nkhondo ndi otsala a mbeu yake, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nawo umboni wa Yesu.’ (Chivumbulutso 12:17). Ena mwa amene akukhala padziko lapansi lero adzaona mawu awa akukwaniritsidwa. Mzimu womwewo umene mu m’nthawi zakale unatsogolera anthu kuzunza mpingo weniweni, m’tsogolo udzatsogolera mukuchitidwa kwa zinthu zoipa zofanana kwa iwo amene akupitiriza kukhala okhulupirika kwa Mulungu. Ngakhale tsopano kukonzekera kwa mkangano womaliza waukulu kukuchitika.” — Prophets and Kings, p. 605.

**b. Kodi ndi motani mmene makhalidwe a otsala akufotokoza mpingo mu masiku otsiriza? Chivumbulutso 14:12; 19:10.**

______________________________________________

______________________________________________

“Mpingo otsala udzavomereza Mulungu mu lamulo lake ndipo udzakhala ndi mphatso ya uneneri. Kumvera lamulo la Mulungu, ndi mzimu wa uneneri, nthawi zonse zakhala zizindikiro zosiyanitsa anthu enieni a Mulungu, ndipo yeso kawirikawiri likuonetseredwa mu zochitika zoonekera za zinthu panopa.” — Loma Linda Messages, p.33.

“Mpingo otsala udzabweretsedwa mu yeso lalikulu ndi chisautso. Iwo amene amasunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu adzamva mkwiyo wa chinjoka ndi khamu la ankhondo ake. Satana amawerengera dziko lapansi ngati lake; walanda ulamuliro pa mipingo yopanduka; koma pano pali kagulu kakang’ono komwe kakukaniza ulamuliro wake.” — Testimonies for the Church, vol. 9, p. 231.

“Kukana kumvera malamulo a Mulungu, ndi kusimikizika kusunga chidani motsutsana ndi amene amalalikira malamulo amenewa, kumatsogolera nkhondo yolimba kwambiri kuchokera kwa chinjoka, chimene chimagwiritsa ntchito mphamvu zake zonse motsutsana ndi anthu a Mulungu osunga malamulo.” — Ibid.,vol.8,p.117.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n’chimodzi, Meyi 29

1. Kodi ndi chifukwa chiyani mpingo ukuimiridwa m’Baibulo ngati mkazi?
2. Fotokozani chiopsezo chimene Mwana wa Mulungu anatenga pobwera padziko lapansi ngati munthu.
3. Kodi ndi liti limene kuthamangitsidwa kwa Satana kumwamba kunakwaniritsidwa mokwanira?
4. Fotokozani chifukwa cha mkwiyo wa chinjoka motsutsana ndi mpingo.
5. Ndi makhalidwe ati amene timayang’ana pozindikira otsala ?

## Zopereka zoyamba zapasabata

**Juni 6, 2026**

**Nyumba Yopempherera ku Prague, Boma la Czech**



Boma la Czech ndi mzinda umene uli mkati mwa Europe, mphepete mwa Germany, piland, Austria ndi Slovakia. Mkati mwa dzikoli muli Bohemia, chigwa china chadela ndi zithuzi za midzi, zochitika zapamwamba ndi zikhalidwe za chuma ndi cholowa cha uzimu kumene John Huss mu (1369-1415) anakhazikitsa kukonzanso kwakukulu. Lero ndi mzinda wokongola wokhala ndi chiwelengelo pafupifupi 10.9 million cha anthu mwa amene 1.4 million amakhala mu mzinda waukulu, wa Prague.

Plague silangokhala dela la mbiri ndizikhalidwe zokha komanso malo amene anthu zigwi akusoweka uzimu, mwa ambiri amasaka tanthauzo la moyo, chiyembekezo, ndi mtendere mmitima yawo. Pakati pa okhala 47.8% ndi osapembeza,11.7% ndi achikhristu pamene 9.3% amazicha akatolika ndi 2.3% ongozinena Akhristu ndi 10.8% ndi azipembezo zina.

Ntchito ya SDA Reform Movement mumzindawu inayamba mu Meyi 2014, pamene anthu atatu okha anasonkhana pa mkumano woyamba. Kenako, mu ogasiti 2020, M,busa ndi banja lake anatumizidwa kumeneku kukalalikira uthenga wachoonadi ku miyoyo yotaika.

Lero, ku mpingo wakuPrague kuli miyoyo 30ya ku mpingo, ndi pamodzi ndi miyoyo yachidwi ndi okozonseledwa ku ubatizo, aliko pamozi anthu 70. Utumiki wopembeza umachitikira kumalo olipira, koma gululi moona mtima limapemphera kuti azachite mwayi wogula kapena kumanga nyumba yawo yopempherera- malo amene anthu aMulunguha kumasonkhana, ndikulimbikitsana mchikhulupiliro, ndikugawirana kuunika pamodzi ndi iwo owazungulira iwo.

“Nyumba imene mulungu amapembezedwa iyenela kukhala monga mwa khalidwe lake ndi ufumu wake.”-Testimonies for the church, vol.5,p.268.

Okondedwa abale ndi alongo, lero tili ndi mwayi wamdalitso mukutenga mbali mu ntchito yaikulu ya Mulungu. Zopereka zanu ndi chosungitsa cha umuyaya, mukupulumutsa miyoyo, ndi mukuilmbikitsa mpingo kumabwalo amu Europe. Choonde pempherani chitsogozo cha Mulungu, mwachifundo thandizani ntchito imeneyi, ndikugawilana ndi chosowa cha ena. Ambuye adalitse winaaliyense wotenga nawo gawo muntchitoyi!

“Tiyamika mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu nonse, ndi ndikumbukila inu m’mapemphero atu.”(1Atesalonika1:2).

Abale anu ndi Alongo ku Prague

# Chilombo ndi Chizindikilo

**VESI LOLOWEZA:** "Ndipo chichita kuti onse , ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo, alandile chilembo pa dzanja lao ndi pamphumi pawo;" (Chibvumbulutso13:16)

**Zowelenga Zoonjezera:** The Great Controversy, pp. 439-450.

"Nyanga yonga ngati mwanawankhosa ndi mawu achilombo zikuonetsa kusiyana pakati pa mayankhulidwe ndi machitachita a dziko lomwe chilombochi chikuimira."—The Great Controversy, p 442.

## 1. CHILOMBO CHONGOFANIZILA — Loyamba, Meyi 31

**a. kodi Yohane anaona chiyani mu chibvumbulutso 13:1 (mbali yoyamba) nanga ndimotani tingazindikilire ichi mu kuunika kochokela mukuwelenga kwathu mu Daniel7:3?**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

**b. Kodi tingaphunzireko chiyani kuchokera mu ena mwamaonekedwe akunja a chilombo mofanizira ndi zirombo zinayi zimene taziphunzira? Chibvumbulutso13:2; Danieli7:4-6.**

____________________________________________________________

____________________________________________________________

"Pa mutu 13 (Vesi 1-10) pakufotokozedwa chilombo china `chooneka ngati nyalugwe' chimene chilombo anachipatsa mphanvu zake, ndi mpando wake, ndi ulamuliro waukulu, ichi chikuimilira, mipingo yotsutsa imene inakhulupilira, yoimilira Papa, imene inapamba mumphanvu ndi chimpando ndi ulamuliro pamene umasogoleledwa ndi ulamuliro wa chiroma kwa ofanana ndi nyalugwe kunalengezetsedwa: "Kunapasidwa kwa iye pakamwa polankhula zinthu zazikulu ndi zamwano…. Ndipo iye anatsegula pakamwa pake mwa mwano kuchitila Mulungu kutukwana zina lake, ndi kachisi wake, ndi iwo okhala kumwamba. Ndipo kunapatsidwa kwa iye kuchita nkhondo ndi oyera mtima , ndi kuwagonjetsa iwo; ndipo mphanvu zinapatsidwa kwa iye kwa mitundu yonse ndi manenedwe onse ndi maiko onse, ulosi uwu, umene uli chifupi mofanana ndi zofotokozera za nyanga yaing'ono mu Danieli 7, mopanda mafunso ukulozera kwa Papa."—The Great Controversy p,439.

"M'maiko ambiri aku Europe mphanvu zimene zimalamulira mumpingo ndi mmadera kwa zaka zakhala zikutsogoleredwa ndi Satana kudzera munjira ya papa."—Ibid., pp.268, 269.

**a. Ndimotani chizindikiro cha chirombo chinasimikiziridwa molingana ndi nthawi ya ulamuliro wake? Chibvumbulutso13:5; Danieli7:25.**

“Mphanvu zinapatsidwa kwa iye mukupitilira kwa miyezi 40 ndi iwiri; Ndipo anatelo mneneri, ndinaona umodzi wa mutu wake unalasidwa kufikila ku imfa,” Ndipo kachiwilinso, `iye amene anatsogolera kuukapolo azapita kuukapolo; Iye amene akupha ndi lupanga azaphedwa ndi lupanga. Kwanthawi yokwana miyezi 40 ndi iwiri ndi ofanana ndi nthawi ndi yogawidwa pakati kwa zaka zitatu ndi theka, kapena matsiku 1260, amu danieli 7- nthawi imene mkatikati mwa mphanvu za papa ndi kupondereza anthu a Mulungu. Nthawi imeneyi inayamba ndi ulamuliro wa papa, mu a.d 538, ndi kuthetsedwa mu 1798. Munthawi imeneyo Papa anaikidwa mndende ndi asilikali achifrenchi, mphanvu za papa analandira bala la kuimfa ndipo bala lakuimfa ndipo ulosi unakwanilitsidwa `Iye amene alinga kundende, kundendeko, adzapita.’”—*The Great Controversy,* p. 439

**b. Ndimotani ulamuliro wa nyalugwe monga chilombo zinachepesedwera? Chibvumbulutso 13:3 (mbali yoyamba), 10,**

**c. Ndi machitachita anji omwe chilombo chinachita? Chibvumbulutso13:6-8.**

“Chikoka cha katolika mumaiko chimene mwakamodzi chinazindikiridwa ulamuliro wake udakali chitsogolo kuti uwonongedwe. Ndipo ulosi unafotokozeledweratu za kubwezeretsedwa kwa mphanvu zake. `ndinaona umodzi wa mutu wake monga unavulazidwa kufikira ku imfa, ndipo bala lake la kuimfa linapola, ndipo dziko lonse linazizwa ndi chilombochi; Vesi3, kubvutika kwa bala lake lakuimfa kumalodzera zakugwa kwa papa mu 1798, zitatha izi, anatelo mneneri, bala lake lakuimfa linapola; ndipo dziko lonse linadabwa ndi chilombochi; Paulo anafotokozera momveka kuti ndi munthu wa uchimo azapitilira kufikira kubwera kwachiwiri kwa Khristu. 2Atesalonika2:3-8. Kumapeto anthawi iye azapititsa chitsogolo ntchito ya chinyengo. Ndipo mbvumbulutsi anafotokoza molozeranso kwa papa. “Onse okhala pa dziko lonse lapansi azachipembezo ichi, amene maina awo sanalembedwe m’buku lamoyo; chibvumbulutso 13:8. Mofanana monse mudziko lakale ndi latsopano, Papa azalandira ulemu kuchokera kuulemu wopelekedwa ku kukhazikitsidwa kwa Sunday (Tsiku loyamba), kupuma kumeneku kunapelekedwa pa ulamuliro wa mpingo wakatolika.”—Ibid.,p579

## 3. CHILOMBO CHONGA NGATI MWANAWANKHOSA — Lachitatu, Juni 2

**a. Ndimphanvu zanji zatsopano za ndale zimene zinaonedwa zikufika mosakhalitsa monga ngati mphanvu za papa zimene zinalandira mabala lakuimfa? Chibvumbuluitso13:11**

“Chilombo chokhala ndi nyanga zonga mwanawankhosa chinaoneka chikutuluka m’dziko.’ Dzikoli likudzuka ku malo lopanda anthu ndi ku kukula pang'onopang'ono mwamtendere malo mochita nkhondo kugonjetsa maiko ena amphamvu kuti icho chikhazikike. sizikanatheka kuti lidzuke pakati pa unyinji wa anthu olimbilana mphamvu mdzika lomwe linalipo kale- p apanyanja aanthuakati pa unyinji, ndi mizinda, ndi manenedwe ambiri.’ Liyenera kukhala dziko la kumpoto.

“Ndi dziko lanji mu dziko latsopano muchaka cha 1798 linadzuka kukhala lamphamvu, ndikupereka lonjezo la mphanvu ndi lalikulu ndi kukopa chidwi cha dziko lonse? Choyimilirachi chinavomelezedwa opandapo mafunso. Dziko limodzi lokha ndilomwe likukwaniritsa zizindikiro zonse zomwe zatchulidwa mu ulosiwu, mwachindunji ulosiwu umalodzera mopanda cholakwitsa ku dziko la (USA) United Statse of America. Mobwelezabweleza malingaliro, pafupifupi mawu enieni, aolemba weniweni wakhala mopanda kuzindikira kugwiritsidwa ntchito ndi katswiri wolankhula ndinso wosunga mbiri mukufotokoza za kudzuka ndi kukula kwa dzikoli. Chilombo chinaonedwa `chikutuluka padziko.’ Ndipo, molingana ndi womasulira, mawu apa anabweletsa poyera `kutuluka’ akuyimilira kukula kapena kumasula monga ngati zomela.’ Ndipo monga taonela , maiko akuyenela kudzuka mudera lakale losakhalidwa…

“`Ndipo chinali ndi nyanga ziwiri zonga ngati zamwanawankhosa zikuimilira achinyamata., achilungamo, ndipo oima njii, Amphanvu akuimilira khalidwe la mdziko la (US, united states) pamene limaonetsedwa muulosi monga lotuluka mu 1798. Pakati pa akhristu omangidwa koyambilira amene anapita ku amerika ndi kukapeza chithandizo kuchoka kukuphinjika kwakukulu ndi kusagwirizana kwa amsembe kunali mwa ambiri amene amafuna kukhazikitsa boma pa madziko amalamulo ndi ufulu wachipembezo. Kawonedwe kawo anapeza malo mu chigamulo choima paokha, chimene chinabweretsanso choonadi chachikulu chonena kuti `Anthu onse analengedwa mofanana’ ndikupereka pamodzi ndi kuunika kokhazikika, `moyo, ufulu, ndi chimwemwe chenicheni’ ndipo malamulo analimbikitsa kwa anthu ufulu wozilamulira okha, kuthandiza kuti oyimilira osankhidwa ndi mavoti oyenera atha kugwira ntchito ndi kuyang’anira malamulo. Ufulu wa chipembezo chachikhulupiliro chinalimbikitsidwanso, munthu wina aliyense amaloledwa kupembeza Mulungu molingana ndi momwe chikumbumtima chake chikuyankhulira. Zipembezo zosankhidwa ndi anthu, ina you Kira, zinakhala madziko amfundo za dziko. Mfundo zimenezi ndi zinsinsi za mphanvu zake ndi chipambano chake. Odzudzidwa ndi oponderezedwa pakati pa akhristu onse amabwela ku malo amenewa pamodzi, ndi chidwi ndi chiyembekezo. Zikwizikwi anaoloka Nyanja yake ndipo United States anazuka kukhala dziko lamphamvu kwambiri pa dziko.”—The Great Controversy, pp. 440,441.

## 4. KUYANKHULA NGATI CHINJOKA

Lachinayi, Juni 3

**a. Ndichochitika chanji choopsa chimene chikuyenera chichitike chokakamizidwa ndi chilombo chonga ngati mwanawankhosa? Chibvumbulutso 13:12, 16.**

“Nyanga yonga mwanawankhosa ndi mawu achinjoka akuimilira akuonetsa kutsutsana pakati pa okhala nawo chiziwitso ndi ochita amdziko monga aoneseledwa. `Kuyankhula’ kwa dziko ndi machitachita a chilamulo chopangidwa ndi cha Boma, ndi machitidwe amenewo adzapereke bodza kwa iwo oukira ndi mfundo za mtendere zimene zizaperekanso monga madziko amalamulo ake. Ulosi umene uzalankhule `monga chinjoka’ ndi kuchita ` ndimphanvu zonse za chilombo choyamba’ monveka bwino umafotokozera kukula kwa uzimu wosagwirizana ndi wokupha zimene zidzachitidwe ndi dziko loimililidwa ndi chinjoka ndi chilombo chonga nyalugwe. Ndipo mawu omwe chilombo chanyanga ziwiri azayankhule ` azayambitsa dziko ndi iwo okhalamo kupembeza chilombo choyamba kuonetsera kuti ulamuliro wadziko limeneli ukuyenera kuchitidwa mukukakamiza ena mukusunga zimene zizaonetsere kupeleka ulemu kwa papa’

“Mchitidwe umenewu uzakhala mwachindunji kutsutsana ndi mfundo za boma ili, mwa ukadaulo mwa malamulo ake aufulu, mwachindunji ndi kulimbika kwachifundo kwa chigamulo choima paokha ndi molingana ndi malamulo aboma. Woyang’anira wa dziko mwanzeru azaganiza zoyang’anira motsutsana ndi ntchito zamphanvu zapaderadera kumbali ya mpingo, ndi zotsatira zawo zokhazikika- chisokonezo ndi kuzunza. Malamulo amabweletsa kuti gululi lisapange malamulo mukulemekeza chipembezo chokhazikitsidwa kapena kulesa kuchita zinthu mwa ufulu, ndiko kuti tsopano palibe chipembezo choyesedwa chimene chingafunikire monga ngati choyenereza ku maudindo alionse odalilika poyela pansi pa United states.’ Ndipokhapokha mukuphwanya zofunikira za chitetezo cha kayendesedwe ka dziko mwa ufulu, ndipomwe kusunga kwa chipembezo chilichonse chingakakamizizdwe ndi malamulo adziko.”-The Great Controvesy,p.442.

**b. Ndimotani mmene kukakamiza kwa chizindikiro cha chilombo kungazagwesere dziko la United States? Miyambo 14:34; Masalimo 119:126.**

“Kwa nthawi zilizonse za kuononga chuma kwakhala kukuwelengeseledwa mwa mkwiyo molimbana ndi tsiku la mkwiyo, ndipo pamene nthawi izafike ndikuti zoipa zadzadza, tsopano mulungu azachita ntchito yake yachilendo chizapezeka chinthu choopsa kuchotsa kupilira kwa umulungu; chifukwa mkwiyo wa mulungu uzagwera mwa chizindikiro ndi mwamphanvu kuti unaonetsedwa monga wosasanganizidwa ndi chifundo; ndipo dziko lonse lizakhala lopanda kanthu. Izakhala nthawi ya kuukila kwa maiko, pamene muzachitika pa ulamuliro wa Satana wolamulira wa dziko azaziphatika okha kumbali ya munthu wauchimo- ndipomwe tsopano muyeso wa uchimo uzazaze; kuukira kwa dziko ndi chizindikiro cha ulamuliro wa dziko.”—Selected Messages, bk 3 p. 373.

## 5. CHIZINDIKIRO CHA CHILOMBO — Lachisanu, Juni 4

**a. Kodi chizindikiro cha ulamuliro wa katolika ndi chanji? Daniel 7:25.**

"Monga chizindikiro cha ulamuliro wa mpingo wakatolika, wolembera papa mchitidwe wosintha sabata kukhala Sunday, limene woukira anabvomereza; …chifukwa pa kusunga Sunday iwo azazindikilitsa mphanvu za mpingo muku lemekeza mphwando, ndinso mukulamula iwo pansi pa uchimo; Henry Tuberville, An abridgment of the Christina Doctrine, page 58, Ndimotani tsopano mukusintha kwa Sabata koma chizindikiro, cha ulamuliro wa mpingo wa katolika- chizindikiro cha chilombo?..

"Pamene kusunga kwa tsiku loyamba Sunday kuzakakamizidwe mulamulo, ndipo dziko lizaunikilidwa molingana kukwanilitsa kwa kusunga koona kwa Sabata, tsopano aliyense angaphwanye kulamula kwa Mulungu, mukumvera malamulo amene Sali apamwamba kuposera iwo akatolika, adzakhala tsopano akulemekeza moyenera pamwamba pa Mulungu."—The Great Controversy, pp. 448,449

**b. Chulani pachimake pa kuyendabe kofanana- chimodzi mukuunikira miyoyo pazokhuza choonadi ndi china mukukakamiza chizindikiro cha chilombo. Chibvumbulutso 13:13-15;16:13, 14, Mateyu 24;14, 24.**

---

"Mpingo ukupempha mkokomo wamphanvu zamalamulo aboma, ndipo muntchito imeneyi, Atsogoleri apapa ndi mipingo yotsutsa izalumikizana. Monga woyendabe kukukakamiza kwa Sunday kuzakhala kwa mphanvu ndi kokhazikika, lamulo lizalimbikitsidwa motsutsana ndi osunga malamulo. Iwo azaopsezedwa ndi chindaputsa ndi kusekeledwa mnende, ndipo ena azapatsidwa maudindo abwino, ndi ena kupatsidwa mphoto ndi zabwinozabwino, monga zowalowela kukulengezetsanso chikhulupiliro chawo. Koma mwa change chawo azayankha kuti; `Tioneseleni ife kuchokera mmawu amulungu cholakwa chathu.'-Pempho lofanana ndi lomwe linachitika ndi luther pansi pa zochitika zofanana. Iwo amene azazengedwa mlandu pa maso pa mabwalo amilandu azapanga chizindikilitso champhanvu cha choonadi ndipo ena amene azawamve azatsogoleredwa kukuima njii mukusunga malamulo a Mulungu. Chifukwa kuunika kuzabweletsedwa pamatso pa zikwizikwi amene mwa njira ina sakanazindikira kanthu ku choonadi ichi."—Ibid., p. 607.

## MAFUNSO OBWELEZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Juni 5

1. Ndimotani ena mwa maonekedwe a chilombo chamu Daniel 7 chinabweletsedwela mu katolika?
2. Bwelezani njira zina za zaka 1260 za ulamuliro wa papa unaonesedwela.
3. Chifukwa chiyani mabala akuimfa sizinali zotsatira za muimfa ya chilombo?
4. Kodi tsogolo lenileni la united states linaonetsedwera ndi nyanga za mwana wankhosa?
5. Kodi anthu opembeza Sunday lero kodi adakali ndi chizindikiro cha chilombo?

LASABATA, JUNI 13, 2026

PHINZIRO 11

# Angelo Atatu

**VESI LOLOWEZA:** “Pano pali chipiliro cha oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a mulungu, ndi chikhulupiliro cha Yesu.” (Chibvumbulutso14:12)

**Zowelenga Zoonjezera:** Early Writings pp. 232-261.

“Ndinaonetsedwa makwelero atatu-uthenga wa angelo woyamba, wachiwiri, ndi wachitatu. Anatero mngelo wondipelekeza, `tsoka kwa iye amene adzayike chochinga kapena kuika chosokoneza kuuthenga umenewu. Kuzindikira koona kwa uthenga umenewu ndi wofunikira kwambiri.”—Early writings, p.258.

## 1. MNGELO WA MCHIBVUMBULUTSO — Loyamba, Juni 7

**a. Fananitsani ndi kusiyanitsa pakati mitundu ya uthenga womwe unapelekedwa ndi angelo. Chibvumbulutso1:20; 10:1,5; 11:1; 22:8.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**b. Ndimotani mmene Mulungu amatumizira uthenga kwa aliyense pa dziko? Aroma10:13-15**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

“Monga omuimilirako ake pakati pa anthu, Mulungu samasankha angelo amene sanagwepo, koma anthu olengedwa, amuna azikhumbitso zofanana pamodzi ndi iwo ofuna kupulumutsa… Ndipo kwa abambo ndi amayi amene azipereka ku chidaliro chopatulika kuti adziwe `chuma chobisika cha Khristu.’Aefeso3:8.”—The Acts of the Apostles,p. 134.

“Tikuyenera kukhala ogwira ntchito limodzi pamodzi ndi angelo akumwamba mukupereka Yesu kudziko lapansi… kwa munthu akuyenela kukhala njira mukulumikizana ndi anthu. Ndipo pamene tikuzipereka kwa Khristu ndi mitima yonse mozipereka, angelo amasangalala kuti atha kumalankjula kudzera mmawu athu kubvumbulutsa chikondi cha Mulungu.”—The Desir of Ages, p. 297.

Ndi ndani anaimililidwa ndi mngelo wamuchibvumbulutso 14:6-12 ndi utumiki wawo? Mateyu28:19,20; Machitidwe1:8.

“Angelo anaonetsedwa akuuluka pakatikati pa mlengalenga, kulengezetsa kudziko uthenga wa chenjezo… Panalibe amene amanva mawu a mngelo ameneyi, popeza iwo ndi oimilira anthu a Mulungu amene akugwira ntchito muchiyanjano ndi kumwamba konse.”—Selected Messages, bk. 2, p. 387.

**a. Ndikwayani kumene mngelo woyamba anatenga uthenga wake? Chibvumbulutso14:6.**

---

“Chipembezo chachikulu chinadzuka pansi pa kulalikira za kubwera posachedwa kwa khristu zinalembedweratu mu ulosi wa uthenga wa mngelo woyamba muchibvumbulutso 14… Mngelo anauluka ‘pakatikati pa mlengalenga,’ `Uthenga waukulu’ umene chenjezo lake linalalikidwa, ndi kulengezetsedwa kwa onse `Okhala padziko lapansi’- `Kumaiko onse, ndi mitundu yonse, ndi manenedwe onse, ndi anthu’-kupeleka umboni wakuchulukandi dziko lonse unayendayenda mochuluka.”—The Great Controversy, p.355.

**b. Ndimotani uthenda wa mnelo woyamba umaitanira chidwi kwa Mulungu monga Mlengi wathu? Chibvumbulutso14:7; Genesisi1:1; Aefeso3:9.**

---

Onetserani ndimotani momwe okhulupirira kubwela kwakhristu anauyeneleza uthenga wa mngelo woyamba ndi chiweludziro kukulalikira kwawo mukubwera posachedwa kwa Khristu. Daniel 7:26,27; 8:14; Machitidwe Atumwi 17:30,31.

“Kwa William Miller ndi ogwira nawo ntchito anzake kunaperekedwa kulalikira chenjezo ku Amelika.Dziko limeneli linakhala phata la okhulupirira zakubwera kwa Khristu. Panali apa pamene ulosi wa uthenga wamngelo woyamba unakwanilitsidwa mwachindunji . Zolembera za Miller ndi amzake zinatengeledwa kumalao akutali. Kulikonse utumiki umaperekedwa kudziko lonse,umatumizidwa moyenela za kubwela kwa Khristu mwachangu.Patali ndi pozungulira lalikirani uthenga wabwino wosatha:`Opani Mulungu, ndipo mpaseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake.’

“Umboni wa ulosi umene umaonetsera kulozera za kubwela kwaKhristu mchaka cha 1844 unatengedwa mokhazikika mmalingaliro mwa anthu. Pamene uthenga umapita kudera ndi kudera, panali paliponse chidwi chofalikira chachikulu. Ambiri amakopedwa kuti zotsusana zochokera munyengo ya ulosiyi zinali zolondola,ndi kuchosa zikhumbitso zawo zonyada, iwo mwamsangala analandira choonadi. Azibusa ena anasiya pambali zowona zawo zamipatuko ndi zokhumba zawo, anasiya malipiro awo ndi mipingo yawo , ndikulumikizana mukulalikira zakubwera kwa Yesu. Pali kusiyanitsa pakati pa azibusa ochepa, komabe, amene angalandire uthengawu; chifukwa chake mochuluka amakhala ozipereka kwa amuna ozichepetsawa… Zikhalidwe za mipingo yopandamo umulungu ndi dziko lagonela muzoipa, kulemetsa miyoyo ya alonda oona, ndipo mofunitsa amapilira ntchito zolemetsa, umphawi, ndi kubvutika, kuti akaitanire anthu kukulapa kupita ku chipulumutso. Ngakhale motsutsana ndi Satana, ntchito imapitabe chitsogolo, ndipo choonadi cha kubwela kwa Khristu chinalandiridwa ndi zikwi zochuluka.”—Ibid.,p. 368.

**a. Kodi mngelo wachiwiri akufuna kulankhula chiyani zokhuzana ndi khalidwe la uzimu la uzichula mpingo wa Khristu? Chibvumbulutso14:8.**

---

"kodi vinyo ameneyo ndi wanji?-chipembezo chake chabodza. Iye anapereka kudziko sabata labodza mmalo mwa Sabata lapalamulo lachinayi, ndipo wakhala akubweleza mwabodza kuti Satana pachiyambi anauza Hava mu Edeni-khalidwe losafa la moyo. Mitundu yambiri yazolakwitsa wakhala akuimwadza patali ndi mmbalimbali, `ndi kuphunzitsa ziphuzitso ndi malamulo aanthu' (Mateyu15:9)."—Selected Messages, bk. 2, p. 118.

"Babylon wakhala akumwadza chiphuzitso choipa, vinyo woipa. Vinyo ameneyu wa zolakwa amapangidwa pa chiphuzitso chaboza, monga khalidwe losafa lamoyo, kubvutika kwamuyaya kwa oipa, kukana kwa kupezeka kwa khristu kwapachiyambi mukubadwa kwake kubetelehemu, ndi unkhala pakati wake ndi kukudza tsiku loyamba lapasabata pamwamba pa tsiku lopatulika ndiloyeletsdewa. Iyi ndi mitundu ina ya zolakwa imene inapelekedwa kudziko lapansi ndi mipingo yambiri, ndipo malembo anakwanilitsidwa onena kuti , `Maiko onse azamwako vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake.''—Testimonies to Ministers, pp. 61,62.

**b. Fotokozani ndimotani okhulupilira za kubwela kwa Khristu anamvetsetsera chokhumudwitsa chawo, kuzindikira mathero olondola amatsiku 2300, ndikuyitana kwawo kukukutuluka kuchoka kwa iwo amene anaukana uthenga. Habakuku 2:3; Mateyu 25:6.**

"Munyengo yodzizira mu 1844, pakatikati pa nthawi imene panali lingaliro loyamba kuti matsiku 2300 akutha, ndikuti mnengo yotentha ya chaka chofananachi, kumene mapeto ake kunazindikirika kuti akupitilira, uthenga unaperekedwa kuchokera mmalemba opatulika: `Onani mkwati adza!'

"Chimene chinatsogolera kupita chitsogolo ndi kuzindikilidwa kuti ukulu wa Atexaxis za kubwezeretsedwa kwa Yerusalemu, chimene chinapangidwa kuyambira munthawi ya matsiku okwana 2300, inaita ndi zotsatira munyengo yokolora amchaka cha 457b.c., ndipo osati pachiyambi pa chaka, ndipomwe panayamba kukhulupiliridwa. Kuchokela munyengo yotentha yamu 457, mzaka 2300unatha mu nyengo ya 1844.'—The Great Controvesy, pp 398,

"Monga mpingo unakana kulandira uthenga wa mngero woyamba, unakana kuunika kochokera kumwamaba ndi kutsika kuchokera kukondera kwa Mulungu. Iwo anadalira kumphanvu zaiwo eni, ndipo mukutsutsa uthenga woyamba anaziika okha pamene sangaonetso kuunika kwa uthenga wamngelo wachiwiri. Koma Mulungu wachikondi, amene anaponderezedwa,analandira uthenga, `wagwawagwa Babulo,'ndi kutuluka mumpingo."—Ealy Writings,p.237.

**a. Ndi chenjezo lanji lozizimutsa likubwera kuchokela kungelo wachitatu? Chibvumbulutso 14:9-11.**

---

“Choopsesetsa ndi chochititsa mantha chakhala chikulengezetsedwa kwa opanda muyaya ukupezeka kuuthenga wa mngelo wa chitatu. Limeneli likuyenela kukhala chimo loopsa limene likuitanitsa mkwiyo wamulungu wosasanganiza ndi chifundo. Anthu sakuyenera kusiidwa mu mdima zokhuzana ndi mfundo yofunikirayi. Chenjezo lotsutsana ndi chimoli likuyenera kupelekedwa kudziko pasanafike chiweludzo cha Mulungu, kuti onse akaziwe kuti chifukwa chiyani akuyenera kutsautsika, ndikukhala ndi mwayi wakupulumuka kuchimenechi… chinapelekedwa mu ulosi pamene umalalikidwa ndi mawu aakulu, kudzera mwa mngelo wouluka pakatikati pa mlengalenga; ndipo adzaitanitsa chidwi cha mdziko.”—The Great Controversy, pp. 449,450.

**b. Munthawi ya uthenga wa mngelo wachitatu, ndimotani oyeramtima azasiyanitsidwire? Chibvumbulutso 14:12.**

“Opembeza Mulungu mwapaderadera azasiyanitsidwa ndi iwo molingana ndi lamulo lachinayi, Pamene lamulo limeneli ndi chizindikiro cha mphanvu ya kulenga ya Mulungu ndi umboni wa kuzichula kwake pa ulemu ndi kulemekeza kwa munthu…Mu chochitika cholimbana ndi akhristu onse azagawidwa mu magulu awiri, iwo amene amasunga malamulo a Mulungu ndikukhala nawo chikhulupiriro mwa Yesu, ndiiwo amene amapembeza chilombo ndi fanolake, ndikulandirachizindikiro chake. Ngakhale mpingo ndi boma azalumikizana pamodzi ndimphanvu zawo mukukakamiza onse, Onse akulu ndi aang’ono, olemera ndi osauka, afulu ndi omangidwa, kukulandira chizindikiro cha chilombo, pamene anthu amulungu sazachilandira ichi. Chibvumbulutso13:16.”—Testimonies for the church, vol.9,pp.16,17.

**c. Ndimotani kudzuka kwa uthenga wa mngelo wachitatu kukufotokozeledwa? Chibvumbulutso7:2,3.**

“Pamkumano womwe unachitika mu Dorchesta, Mass., Novemba, 1848, Ndinaonetsedwa za kulalikira kwa uthenga wa kuikidwa chizindikiro, ndi ntchito ya abale mukupeleka kuunika kumene kukuwalira panjira pathu.

“Nditalandira masomphenyawa, ndinalankhula kwa mwamuna wanga.’ “Ndili ndi uthenga wa inu, mukuyenera kuyamba kutulutsa zipepala zochepa ndi kuzitumiza izi kwa anthu. Ziyenera kukhala zochepa koyambilira. Koma pamene anthu akuwelenga, iwo azapeleka njira imene mungasindikizire ndipo chizakhala chipambano kuchokela koyamba. Kuchokela kuchiyambi chochepachi ndinaonetsedwa kwa ine kukhala monga kasupe wa kuunika amene anayenda mwabwino kuzungulira dziko lonse.’”—Life Sketches, p, 125.

## 5. MUTU WA UTHENGA — Lachisanu, Juni 11

**a. Ndimotani mdalitso wolalikidwa uzakwanilisidwile posatengela iwo amene anafa mwachikhulupiliro mkati kati mwakulalikira kwa uthenga wamngelo wachitatu? Chibvumbulutso 14:13; Daniel 12:2.**

---

"Panali pakati pa utsiku pamene Mulungu anasankha kuombola anthu ake, pamene oipa amawatonza owazungulira, mwadzidzi dzuwa linaonekera kuwalira mu mphanvu zake, ndipo mwezi unaimanso. Oyipa anayang'ana pa chochitikachi modabwitsika, pamene oyera mtima anayang'ana ndi chimwemwe cha pamwamba kuyankhula za chiombolo chawo. Zizindikiro ndi zozizwa zinatsatirapo muchipambano cha change. Chilichonse chinaoneka mosandulika kuoneka muchilengedwe chenicheni, Misinje inasiya kuyenda, mtambo waukulu wokuda unasika ndikukhulana mwa iwo okha. Koma panali malo amodzi okha abwino okhazikika aulemelero, kunatuluka mawu a mulungu ngati madzi ochuluka, kugwedeza kumwamba ndi dziko lapansi. Kunali chibvomelezi champhanvu, manda anaseguka, ndipo onse omwalira mwachikhulupirilo pansi pa uthenga wangelo wachitatu, mukusunga Sabata, anatuluka kuchoka mufumbi, odzazidwa ndi ulemelero, kuzamva za pangano lamtendere umene Mulungu azapange ndi iwo amene amasunga malamulo ake."—Early Writings, p. 285.

**b. Ndi chiyani chizachitike kumathero a uthenga wa mngelo wachitatu? Chibvumbulutso14:14-16; Marko 4:26-29.**

---

---

"Ndinaona mngelo akuthamanga kuno ndi uko kumwamba. Mngelo ndi cholembela chake cha nyanga kumbali yake ina wochokela kudziko ndi kukapeleka mbiri kwa Khristu kuti ntchito yake wamaliza, ndipo oyera mtima anawelemgedwa ndi kuikidwa chizindikiro. Kenaka ndinaona Yesu, amene amatumikira pamaso pa likasa lokhala ndi malamulo khumi, anaponya pansi cholembela, iye anakweza manja ake, ndi mawu okweza anati, `Kwatha'".—Ibid.,p.279.

## Mafunso Obweleza Pawekha — Lachisanu n'chimodzi, Juni 12

1. Chifukwa chiyani Mulungu anapanga kuti kulalikira kwa uthenga wabwino kuzidalira anthu ngati zida zake?
2. Ndimotani uthenga wa mngelo woyamba anafikira kuzungulira dziko lonse?
3. Chulani cholinga choperekera uthenga wa mngelo wachiwiri.
4. Ndikusiyana kwanji kumene uthenga wa mngelo wachitatu unaonetsera?
5. Ndi chochitika chanji chizachitike utatha uthenga wa mngelo wachitatu ukazapelekedwa?

# Kuyitana Komaliza

**VESI LOLOWEZA:** “Ndipo zitatha izi ndinaona mngelo wina akutsika kumwamba wakukhala nao ulamuliro waukuru; ndipo dziko linaunikidwa ndi ulemerero wace (Chibvumbulutso 18:1)

**Zowerenga Zoonjezera:** Great Controversy, p. 603–612.

“Ntchito yayikulu ya uthenga wabwino sikutsekedwa ndi chionetsero chochepa kwa champhamvu za Mulungu kuposa momwe idayambira.”—The Great Controversy. 611.

## 1. Babulo Wamkulu — Loyamba, Juni 14

**a. Fotokozani mawonekedwe ochititsa chidwi omwe Yohane adawona a mpingo wotchedwa kuti Babulo Wamkulu. Chivumbulutso 17:1–6.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

“Mkazi (Babulo) wa pa Chivumbulutso 17 . . . akufotokozedwa anabvala chibakuwa, ndi mlangali, nakometsedwa ndi golidi, ndi miyala ya mtengo wace, ndi ngale; nakhala naco m'dzanja lace chikho chagolidi chodzala ndi zonyansa ndi zodetsa . . . ndipo pamphumi pace padalembedwa dzina, *CHINSINSI, BABULO WAMKURU AMAI WA ACIGOLOLO . . . .* ' Roma ndi ulamuliro womwe unalamulira mwa nkhanza kwa zaka mazana ambiri pa mafumu a Chikhristu. Chibakuwa, ndi mlangali, zokometsedwa ndi golidi, ndi miyala ya mtengo wace, ndi ngale zikuwonetsa bwino ulemerero ndi kudzikuza koposa kwa chifumu komwe kwakhudza ulamuliro wodzikuza wa chi Roma. Ndipo panalibe mphamvunso ina iliyonse yomwe inganenedwe moonadi kuti 'woledzera ndi mwazi wa oyera mtima' ngati mpingo umene wazunza mwankhanza otsatira a Khristu. Babulo akuyimbidwanso mlandu wochita mgwirizano wosaloledwa ndi 'mafumu a dziko lapansi.' Ndi kudzera mu kumusiya Mulungu, ndi kupanga mgwirizano ndi achikunja, komwe mpingo wa Ayuda unakhala wachigololo; ndipo Roma, podzidetsa mofanana motere, pofunafuna thandizo kuchokera ku maulamuliro a dziko lapansi, akulandira chigamulo chofanana.”—The Great Controversy, p. 382. [Kupendeka kwa Zolemba ndi kuchokera kwa Wolemba Bukulo.]

**b. Kodi mphamvu imeneyi idzafika bwanji kumapeto kwake? Chivumbulutso 17:15–18.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**a. Fotokozani za kubwera kwa mngelo amene akuwonekera mu Chivumbulutso 18:1.**

---

"Uthenga wa angelo atatu ukuyenera kuphatikizidwa, ndi kupereka kuwala kwawo kwa magawo atatu ku dziko lapansi. Mu buku la Chivumbulutso, Yohane akuti, 'Ndinaona mngelo wina akutsika m'Mwamba wakukhala nao ulamuliro waukuru; ndipo dziko linaunikidwa ndi ulemerero wace.' [Kuchokera pa Chivumbulutso 18:2–5.] Izi zikuyimira kupereka kwa uthenga womaliza wa magawo atatu wa chenjezo ku dziko lapansi."—The SDA Bible Commentary [E. G. White Comments], vol. 7 p. 985.

"Mpingo ndi malo osungiramo chuma cha chisomo cha Khristu; ndipo kudzera mu mpingo udzawonekera pamapeto pake, ingakhale ku 'ma ukulu ndi maulamuliro mu malo akumwamba,' chiwonetsero chomaliza komanso chodzadza cha chikondi cha Mulungu."—The Acts of Appostles, p. 9.

**b. Kodi ulemerero wa mngelo umatanthauza chani, ndipo umawonetsedwa motani? Masalmo 29:1, 2; Yohane 17:22, 23.**

"Ndi pamene kumanga khalidwe kwa nyalanyazidwa, pamene kukongola kwa moyo kwasowekera, pamene umulungu wophweka wanyozedwa, kunyada ndi chikondi chodzionetsera zomwe zimafunano makachisi okongoletseredwa komaso okometseredwa, ndi miyambo yokakamiza. Koma mu zonsezi Mulungu salemekezedwa. Iye amauwona mpingo wake kukhala wamtengo wapatali, osati chifukwa cha ubwino wake wakunja, koma chifukwa cha chipembedzo choona mumtima, chomwe chimawusiyanitsa ndi dziko lapansi. Iye amawuyeza molingana ndi kukula kwa ziwalo zake mu chidziwitso cha Khristu, molinganso ndi kupita patsogolo kwa zodutsamo za moyo wauzimu." — Prophets and Kings, pp. 565, 566.

**c. Kodi Mulungu anafotokoza bwanji za ulemerero wake, pamene Mose adapempha kuti awuone? Exodo 33:18, 19; 34:5–7.**

"Ulemerero wa makhalidwe a Mulungu umawonekera mu khalidwe lake. Tsamba lililonse la Malemba Opatulika limanyezimila ndi kuwala kwake. Chilungamo cha Khristu, monga ngale yamphumphu, yoyera, chilibe chilema, kapena banga. Palibe ntchito ya munthu yomwe ingakhonze kusintha mphatso yayikulu ya Mulungu komanso yamtengo wapatali. Iyo ilibe chilema." — Christ's Object Lessons, tsamba 115.

"Khalidwe ili linavumbulutsidwa mu moyo wa Khristu. Kuti kudzera mu chitsanzo Chake atsutse tchimo m'thupi, adadzitengera Iye mwini chifaniziro cha thupi lochimwa. Mopitirira ankayang'ana khalidwe la Mulungu; Iye mopitirira ankavunbulutsa khalidwe ili ku dziko lapansi.

"Khristu akufuna kuti omutsatira ake awonetsere khalidwe lomweli m'miyoyo yawo." — God's Amazing Grace, P.322.

**a. Kodi mngeloyo akulankhula bwanji ndi anthu okhala mu Babulo? Chivumbulutso 18:2.**

___

___

"Mphamvu ndi ulemerero waukulu zinaperekedwa kwa mngeloyo, ndipo pamene analikutsika, dziko lapansi linawalitsidwa ndi ulemerero wake. Kuwunika komwe kunabwera kwa mngeloyu kunafalikira kulikonse, pamene anafuula mwamphamvu, ndi mawu amphamvu. . . . Uthenga wa kugwa kwa Babulo, monga momwe unaperekedwera ndi mngelo wachiwiri, ukubwerezedwanso, ndi kuwonjezera zina mwa ziphuphu zomwe zakhala zikulowa m'mipingo kuyambira mu 1844."—Early Writings, p. 277.

**b. Kodi ndi chani chomwe chidakasintha mu Babulo kuyambira pamene uthenga wa mngelo woyamba unalarikidwa koyamba? Chivumbulutso 18:3.**

___

"Uthenga wa mngelo wachiwiri wa Chivumbulutso 14 unalalikidwa koyamba mu chilimwe cha 1844, ndipo mu nthawi imenei unali ndi phunziro lachindunji ku mipingo ya ku United States, komwe chenjezo la chiweruzo linalengezedwa kwambiri ndipo linakanidwa ndi ambiri, komwe kugwa kwa mipingo kunali kofulumira kwambiri. Koma uthenga wa mngelo wachiwiri sunakwaniritsidwe kwathunthu mu 1844. Mipingoyo inagwa mmakhalidwe, chifukwa cha kukana kwawo kuunika kwa uthenga wa kubweranso kwa Yesu khristu; koma kugwa kumeneko sikukwanire. Pamene anali kupitilizabe kukana choonadi chapadera cha nthawi imeneyi anagwa pang'ono pang'ono. Komabe, sikukananenedwa kuti Babulo wagwa, . . . ‘chifukwa wapangitsa mitundu yonse kumwa vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake.’ Iye sanapangitse mitundu yonse kuchita izi. Mzimu wotsatira dziko lapansi ndi kusalabadira choonadi choyesa cha nthawi yathu ulipo ndipo wakhala ukukulirakulira m'mipingo ya chikhulupiriro cha yotsutsa Chikatolika m'maiko onse a Chikhristu; ndipo mipingo iyi ikuphatikizidwa mu chidzudzulo chachikulu komanso choopsa cha mngelo wachiwiri. Koma ntchito ya kupanduka sinafike pachimake.

"Buku Lopatulika limanena kuti Ambuye asanabwere, Satana adzagwira ntchito 'ndi mphamvu yonse ndi zizindikiro zizizwa zonama, ndi chinyengo chonse cha chosalungamo;’ ndipo kwaiwo omwe 'sanalandire chikondi cha choonadi, kuti akapulumutsidwe iwo,' adzasiyidwa kuti alandire 'mchitidwe akusocheretsa, kuti akhulupirire bodza.' 2 Atesalonika 2:9–11. Mpaka makhalidwe amenewa atakwaniritsidwa, komanso mgwirizano wa mpingo ndi dziko lapansi utakwaniritsidwa mu dziko la chikhristu chonse, kugwa kwa Babulo kudzakhala kwathunthu. Kusintha uku ndi kopitilira, ndipo kukwaniritsidwa kwanthunthu kwa Chivumbulutso 14:8 kudzachitika mtsogolo.” — Great Controversy, pp. 389, 390. [Kupendeka kwa Zolemba ndi kuchokera kwa Wolemba Bukulo.]

**a. Kodi ndi kuitana kotani kofulumira komwe kukumveka ndi omwe akadali mu Babulo? Chivumbulutso 18:4.**

---

---

"Chivumbulutso 18 chikulozera ku nthawi yomwe, chifukwa chokana ma chenjezo atatu a Chivumbulutso 14:6-12, mpingo udzafika mokwanira pa khalidwe lomwe linanenedweratu ndi mngelo wachiwiri, ndipo anthu a Mulungu omwe akadali mu Babulo adzayitanidwa kuti asiyane ndi mgwirizano wake. Uthenga uwu ndi womaliza womwe udzaperekedwe ku dziko lapansi; ndipo udzakwaniritsa ntchito yake. Pamene iwo omwe 'sanakhulupirire choonadi, koma anakondwera ndi chosalungama' (2 Atesalonika 2:12), adzasiyidwa kuti alandire machitidwe akusocheretsa ndi kukhulupirira bodza, pamenepo kuwala kwa choonadi kudzawalira onse omwe mitima yawo yatseguka kuti achilandire, ndipo ana onse a Mulungu omwe atsala ku Babulo adzamvera kuitana: 'Turukani m'menemo, anthu anga' (Chivumbulutso 18:4).”—The Great Controversy, p. 390.

**b. Kodi ndi ndani amene amatchedwa kuti "Anthu anga," ndipo akulankhulidwa mu kuyitana koti achoke mu Babulo? Yohane 10:16.**

---

"Posawerengera m'dima wauzimu ndi kulekanitsidwa ndi Mulungu komwe kulipo m'mipingo yomwe yapanga Babulo, gulu lalikulu la otsatira owona a Khristu likupezekabe mu mgwirizano wawo. Pali ambiri mwa iwo omwe sanawonepo choonadi chapadera cha nthawi ino. Ambiri sakukhutira ndi momwe kalidwe lawo lilili ndipo akulakalaka kuwala kowoneka bwino. Akuyang'ana pachabe chifanizo cha Khristu m'mipingo yomwe alumikizidwa nawo. Pamene mipingo iyi ikutalikana talikana ndi choonadi, ndikugwirizana kwambiri ndi dziko lapansi, kusiyana pakati pa magulu awiriwa kudzakula, ndipo pamapeto pake kudzapangitsa kuti anthu alekane. Nthawi idzafika pamene iwo amene amamkonda Mulungu kotheraru sangadzathenso kukhala ogwirizana ndi anthu ‘okonda zozikondweretsa munthu osati kukonda Mulungu; akukhala nawo mawonekedwe a chipembedzo, koma mphamvu yake adaikana.’ " - Ibid., p. 390.

**c. Ndi chifukwa chani kuitana kotuluka mu Babulo kuli kofulumira kwambiri? Chivumbulutso 18:5–8.**

---

---

"Kuwala komwe kunaperekedwa pa odikirawo kunafikira paliponse, ndipo awo omwe anali m'mipingo yomwe inali nako kuunika kochepa, omwe sanamve ndi kukana mauthenga atatuwo, anamvera kuitanako ndipo anasiya mipingo yakugwa." - Early Writings, p. 278.

## 5. KUKONZEKA KUITANA — Lachisanu, Juni 18

**a. Fotokozani kufunika kwa uthenga womveka bwino komanso wotsimikizika wa chenjezo. Yesaya 58:1; 1 Akorinto 14:7, 8.**

"Chapta cha khumi mphambu zisanu ndi zitatu cha Chivumbulutso chikuvumbulutsa kufunika kopereka choonadi mopanda malire koma molimbika mtima ndi mwa mphamvu. ... Pakhala kuzungulira zungulira kwakukulu polalikira uthenga wa m'ngelo wachitatu." - Evangelism, p. 230.

"Mulungu anachikhazikitsa kuti alonda adzidzuka ndipo ndi mawu ogwirizana adzipereka uthenga womveka bwino, kulipatsa lipenga fuuu lapadera, kuti anthu onse adzakhala tsonga pa ntchito yawo ndi kuchita mbali yawo mu ntchiuto yayikuluyi. Kenako kuwala kwa mphamvu, konyezimila bwino kwa mngelo wina wa kutsika m'mwamba wakukhala nawo ulamiliro waukulu, akanawalira dziko lapansi ndi ulemerero wake. Tatsalira m'buyo kwa zaka zambiri; ndipo iwo amene anaima mwa khungu ndi kulepheretsa kupita patsogolo kwa uthenga womwe Mulungu anafuna kuti upite patsogolo kuchokera ku msonkhano wa Minneapolis ngati nyali yowala, anasowekera kudzichepetsa mitima yawo pamaso pa Mulungu ndikuona ndikumvetsetsa momwe ntchitoyi yalepheretsedwera ndi khungu lawo la maganizo ndi kuuma mtima kwawo." - The Ellen G. White 1888 Materials, p. 1070.

**b. Ndi pempho lotani la Yesu lomwe tonsefe tingalitengere ku mtima patokha? Yohane 12:35, 36.**

"Mngelo wina akugwirizanitsa mawu ake ndi mngelo wachitatu, ndipo dziko lapansi lawunikiridwa ndi ulemerero wake. Kuunikako kukukulirabe, ndipo kukuwalira mitundu yonse ya dziko lapansi. Kukuyenera kupita patsogolo monga nyali yomwe ikuyaka. Kudzatsoreredwa ndi mphamvu yayikulu, kufikira kuwala kwake kwagolide kudzafikire kwa mtundu uliwonse, ndi pfuko, ndi manenendwe, ndi anthu onse akukhala padziko lonse lapansi. Ndikufunseniko, kodi mukuchitapo chani kuti mukonzekere ntchito imeneyi? Kodi mukumanga kwa muyaya? Muyenera kukumbukira kuti mngelo uyu akuyimira anthu omwe ali ndi uthenga uwu woti awupereke ku dziko lapansi. Kodi muli pakati pa anthu amenewo?" — The Review and Herald, August 18, 1885.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA — Lachisanu n'chimodzi, Juni 19

1. Fotokozani momwe Roma ikugwirizanirana ndi kufotokozera kwa Babulo, mayi wa akazi achigololo.
2. Kodi ulemerero weniweni wa Mulungu ndi uti womwe udzavumbulutsidwa ndi mngelo wina?
3. N'chifukwa chani uthenga wa mngelo wachiwiri uyenera kubwerezedwa?
4. Kodi otsatira ambiri owona a Yesu ali kuti lero lino?
5. Kodi ndingakhale bwanji chikoka chabwino m'malo molepheretsa ntchito ya Mulungu masiku ano?

LASABATA, JUNI 27, 2026

PHINZIRO 13

# Chimaliziro Chanenedweratu

**Vesi Loloweza:** “Ndipo Iye wakukhala pa mpando wachifumu anati, Taonani, ndipanga zonse zatsopano. Ndipo ananena, Talemba; pakuti mawu awa ali okhulupirika ndi oona” (Chivumbulutso 21:5).

**Zowerenga Zoonjera:** Early Writings, pp. 279–295.

“Dziko lathu laling'ono, pansi pa themberero la uchimo, banga limodzi lakuda mu zolengedwa zake zaulemerero, lidzalemekezedwa kuposa maiko ena onse mu chilengedwe chonse cha Mulungu.”—The Desire of Ages, pp. 26.

## 1. MILIRI ISANU NDI IWIRI YOTSIRIZA — Loyamba, Juni 21

**a. Kodi ndi chiyani chomwe chavumbulutsidwa chokhudza ziweruzo za Mulungu zizatsanuliridwe padziko lapansi? Chivumbulutso 15:1; Chapta 16.**

“Ndinaona kuti miliri isanu ndi iwiri yomaliza inali pafupi kutsanuliridwa pa iwo amene analibe pothawira; koma dziko lapansi silinawaonenso monga momwe anagathe kuwonera madontho ambiri a madzi omwe anali pafupi kugwa. Kenako ndinapatsidwa mphamvu yotha kupirira  panthawi yoopsa ya miliri isanu ndi iwiri yomaliza, ya mkwiyo wa Mulungu. Ndinaona kuti Mkwiyo wake unali woopsa komanso wochititsa mantha, ndipo  Iye atangotambasula dzanja lake, kapena kulikweza mokwiya, okhala padziko lapansi adzakhala ngati sanakhaleponso, kapena adzavutika ndi zilonda zosachiritsika ndi miliri yowononga yomwe idzwagwera iwo, ndipo sadzapeza chipulumutso, koma adzawonongedwa ndi iyo.”—Early Writings, p.  64.

**b. Kodi chochitika chomwecho chikufotokozedwa bwanji m'njiranso yina yosiyana? Yeremiya 25:30–33; Chivumbulutso 19:17–21.**

“Oipa adutsa malire awo ochitiridwa chifundo; Mzimu wa Mulungu, womwe umakanidwa mosalekeza, mapeto ake wachotsedwa. Osaphimphidwanso ndi chisomo cha Mulungu, alibenso chitetezo chowatetezera kwa woipayo. Tsopano Satana adzatengalera okhala padziko lapansi muvuto lakulu, lomaliza. Pamene angelo a Mulungu adzasiya kugwira mphepo zochititsa mantha za chilakolako cha munthu, zinthu zonse zochititsa mikangano zidzamasulidwa. Dziko lonse lapansi lidzakhala mu chionongeko choopya kuposera chomwe chinachitika mu Yerusalemu wakale.”—The Great Controversy, p. 614.

a. Kodi buku la Chivumbulutso limafotokoza bwanji za kubweranso kwachiwiri kwa Khristu? Chibvumbulutso 1:7; 6:15–17.

"Posakhalitsa maso athu anakokeredwa kum'mawa, chifukwa chamtambo wakuda waung'ono omwe unaonekera, pafupifupi theka la kukula kwa chikhatho cha dzanja, omwe tonse tinkazindikila kuti chinali chizindikiro cha Mwana wa munthu. Tonsefe mopanda mantha tinayang'ana mtambowo pamene unkayandikira, ndipo unakhala wowala, waulemerero, komanso ulemerero opitilira, mpaka unakhala mtambo waukulu woyera . Pansi pake panaoneka ngati moto; utawaleza unali pamwamba pa mtambowo, pomwe mozungulirapo panali angelo zikwi khumi, akuimba nyimbo yokondedwa zedi; ndipo pamenepo panakhala Mwana wa munthu. Tsitsi lake linali loyera komanso lopota ndipo linafika pamapewa ake; ndipo pamutu pake panali akorona ambiri. Mapazi ake anali ngati moto; m'dzanja lake lamanja munali chikwakwa chakuthwa; kumanzere kwake, kunali lipenga la siliva. Maso ake anali ngati lawi la moto, lomwe linkafufuza ana ake monsemo. Kenako nkhope zonse zinayamba kuyera, ndipo iwo amene anakanidwa ndi Mulungu anasonkhana mu m'dima. Kenako tonse tinafuwula kuti, 'Ndani adzayime? Kodi mwinjiro wanga ndi wopanda banga?' Kenako angelo anasiya kuimba, ndipo panali nthawi ya chete odabwitsa, pamene Yesu analankhula nati:

'Iwo amene ali ndi manja oyera ndi mitima yoyera adzakhoza kuyimirira; Chisomo changa chikukwanirani.' Pamenepo nkhope zathu zinawala, ndipo chimwemwe chinadzaza mu mtima uliwonse. Ndipo angelo anakweza nyimbo, nayimbanso, pamene mtambo unali kuyandikira pafupi ndi dziko lapansi."—Early Writings, pp. 15, 16.

**b. Kodi angelo tsopano adzachita chiyani? Mateyu 24:31; 1 Atesalonika 4:16, 17.**

"Uchimo unawononga ndipo pafupifupi kuthetseratu chifaniziro cha Mulungu; koma Khristu anabwera kudzabwezeretsa izo zomwe zinatayika. Adzasintha matupi athu oipa ndikuwapanga kukhala ngati thupi lake laulemerero. Matupi akufa, ovundawa, osakongola, omwe anaipitsidwa ndi uchimo, adzakhala angwiro, okongola, komanso osafa. . . .

"Angelo 'anasonkhanitsa osankhidwa ake kuchokera ku mphepo zinayi, kuchokera kumalekezero a thambo mpaka kumalekezero ena.' Ana aang'ono ananyamulidwa ndi angelo oyera kaperekedwa m'manja mwa amayi awo. Abwenzi omwe analekanitsidwa ndi imfa kwa nthawi yayitali analukizanitsidwa, sadzalekanitsidwanso, ndipo ndi nyimbo zachisangalalo zinakwera pamodzi kupita ku Mzinda wa Mulungu."—The Great Controversy, p. 645.

**c. Kodi Satana adzaikidwa kuti? Chivumbulutso 20:1, 2.**

"Pa dziko pano padzakhala ku nyumba kwa Satana ndi angelo ake oipa kwa zaka chikwi. Popeza ali ndi malire ofikila ku dziko lapansi lokha, sadzakhala ndi mwayi wopita ku maiko ena kuti akayese ndi kukwiyitsa iwo omwe sanagwepo."—Ibid., p. 659.

**a. Kodi anthu oyera mtima azizachita chiyani mu zaka chikwi zimene Satana azamangidwe? Chibvumbulutso 20:4-6; 1 Akorinto 6:2, 3.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"Munthawi ya zaka chikwi kuchokera pa mzukiro oyamba kukafika pa wachiwiri chiweruzo cha oipa chidzachitika. Mtumwi Paulo akuloza ku chiweruzo chimenechi monga chochitika chomwe chizatsatire kubwera kwa Yesu kwachiwiri….Danieli akufotokoza kuti pamene Nkhalamba ya kale lomwe inabwera, 'Chiweruziro chinaperekedwa kwa opatulika a wamwambamwamba' Danieli 7:22. Munthawi imeneyi anthu olungama azalamulira monga mafumu ndi ansembe kwa Mulungu….Ndi munthawi imeneyi imene, monga analosera Paulo, 'oyera mtima azaweruza dziko lapansi.' 1 Akorinto 6:2. Pamodzi ndi Khristu iwo azaweruza anthu oyipa, kufananiza machitidwe awo ndi buku la malamulo, Baibulo, ndi kumagamula mulandu uliwonse molingana ndi nchito zomwe zinachitidwa muthupi. Kenako gawo lomwe munthu wochimwa akuyenera kusausika liziperekedwa, molingana ndi nchito zawo; ndipo zizilembedwa pa maina awo mbuku la imfa.

"Satananso ndi angelo oyipa akuweruzidwa ndi Khristu ndi anthu ake. Akunena Paulo: 'Kodi simudziwa kuti tidzaweruza angelo?' Vesi 3. Ndipo Yuda akufotokoza kuti 'Angelonso amene sanasunga cikhalidwe cao choyamba komatu anasiya pokhala pao pao adawasunga mdende zosatha pansi pa mdima, kufikira chiweruziro cha tsiku lalikuru.' Yuda 6." –The Great Controversy, pp. 660, 661.

**b. Kodi chizachitike ndi chiyani pa mapeto ake a zaka chikwi za chiweruziro? Chibvumbulutso 21:2; 20:7, 8.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"Pomalizira pa zaka chikwi mzukiro wachiwiri uzachitika. Panthawi imeneyi anthu ochimwa azaukisidwa kwa akufa ndi kuonekera ku mpando wachifumu wa Mulungu kuti 'alandire ziweruzo zimene zinalembedwa….' Yesaya akufotokoza, zokhuzana ndi oyipa kuti: 'Ndipo iwo azasonkhanitsidwa pamodzi, monga ndende zimasonkhanisidwa m'dzenje, ndi kutsekeredwa m'kaidi, ndipo atapita masiku ambiri adzawazonda.' Yesaya 24:22."- Ibid., p. 661.

**c. Kodi chimaliziro chenicheni cha anthu oyipa chizakhala chanji? Chibvumbulutso 20:9; Malaki 4:1.**

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

"Mu Malawi amoto oyeretsa anthu oyipa mapeto ake awonongedwa, muzu ndi mthambi-Satana muzu, omutsatira ake nthambi. Chilango chozaza cha lamulo chaperekedwa; zofuna za chilugamo zakwaniritsidwa;; ndipo kumwamba ndi dziko la pansi, poona zimenezi, akufotokoza chilungamo cha Yehova." –Ibid., p. 673.

**a. Fotokozani lonjezo la Mulungu lopanganso zinthu zonse mwatsopano. Chivumbulutso 21:1, 5; 22:1, 2; Yesaya 65:17.**

"Ntchito ya chiwombolo idzamalizidwa. M'malo omwe uchimo unachulukila, chisomo cha Mulungu chidzachuluka kwambiri. Dziko lapansi lomwe, malo womwe Satana amati ndi ake, siilidzangowomboledwa kokha komanso lidzakwezedwa. Dziko lathu laling'onoli, pansi pa temberero la uchimo, banga limodzi lakuda mu chilengedwe chake chaulemerero, lidzalemekezedwa pamwamba pa maiko ena onse mu chilengedwe cha Mulungu. Apa, pomwe Mwana wa Mulungu anakhala mwa anthu; komwe Mfumu ya ulemerero inakhala ndi kuvutika ndi kufa—apa, pamene Iye adzapanga zinthu zonse kukhala zatsopano, chihema cha Mulungu chidzakhala mwa anthu, 'ndipo Iye adzakhalitsa nawo, ndi iwo adzakhala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhala nawo, nadzakhala Mulungu wawo.' Ndipo kupyola m'mibadwo yosatha pamene owomboledwa adzayenda m'kuunika kwa Ambuye, adzamutamanda chifukwa cha Mphatso yake yosaneneka—Imanueli, 'Mulungu nafe.'"—The Desire of Ages, p. 26.

**b. Kodi chidzakhale chosiyana ndi chiyani mu dziko latsopano? Yesaya 65:21–25; Chivumbulutso 21:4.**

"Kupweteka sikungakhalepo mu moyo wakumwamba. Sipadzakhalanso misozi, sipadzakhalanso maliro, sipadzakhala misonkhano yolira. . . .

"Mu Mzinda wa Mulungu 'sikudzakhalanso usiku.' Palibe amene adzafunenso kapena kukhumbila kupumula. Sipadzakhalanso kutopa pochita chifuniro cha Mulungu ndi kupereka matamando kwa Iye ku dzina lake. Nthawi zonse tidzamva kuzizirira kwa m'mawa ndipo tidzakhala nako mopitirira. 'Ndipo sasowa kuunika kwa nyali, ndi kuunika kwa dzuwa; chifukwa Ambuye Mulungu adzwaunikira.' Chivumbulutso 22:5. Kuwala kwa dzuwa kudzachotsedwa ndipo m'malo mwake pazakhala kuwala konyezimira kumene sikumazapweteka pokuyan'gana, koma komwe kuzaposa kuwala kwa usana wathu." — The Great Controversy, p. 676.

"Mu Buku lopatulika cholowa cha opulumutsidwa chimatchedwa 'dziko.' Ahebrib 11:14-16. Kumeneko M'busa wakumwamba amatsogolera nkhosa zake ku akasupe a madzi amoyo. Mtengo wa moyo udzabala zipatso zake mwezi ndi mwezi, ndipo masamba a mtengowo ndiwo akuchiritsa nao amitundu. Kuli mitsinje yoyenda nthawi zonse, yoyera ngati krustalo, ndipo pambali pake mitengo yogwedezeka imaponya mithunzi yawo panjira yokonzedwera opulumutsidwa a Ambuye. Kumeneko zigwa zazikulu zizakuka mkukhala mapiri okongola, ndipo mapiri a Mulungu adzakwera kwambiri pamwamba. Pa zigwa zamtenderezo, mbali mwa mitsinje yamoyo, anthu a Mulungu, apaulendo ndi oyendayenda kwa nthawi yayitali, adzapeza nyumba zawo."—Ibid., p. 675.

## 5. KUYITANA NDI KUDALITSA

**Lachisanu, June 25**

**a. Kodi Yesu amafuna kulimbikitsa owerenga maulosi a Chivumbulutso ndi mawu otani? Chivumbulutso 22:7, 12-14.**

"Ambuye mwini anaulula kwa mtumiki wake zinsinsi zomwe zili m'bukuli, ndipo anakonza kuti zikhale zotseguka kuti onse aziphunzire. Choonadi chake chalembedwa kwa iwo okhala m'masiku otsiriza a mu mbiri ya dziko lapansi, komanso kwa iwo okhala m'masiku a Yohane. Zina mwa zochitika zomwe zafotokozedwa mu ulosiwu zinachitika kale, zina zikuchitika tsopano; zinaso zikuwonetsera kutha kwa mkangano waukulu pakati pa mphamvu za m'dima ndi Kalonga wa kumwamba, ndipo zina zimasonyeza kupambana ndi chisangalalo cha oomboledwa m'dziko lapansi lopangidwa latsopano."

"Wina asaganize kuti, chifukwa choti sangathe kufotokozera tanthauzo la chizindikiro chilichonse cha mu Chivumbulutso, kuti ndizopanda phindu kwa iwo kufufuza mu bukuli pofuna kudziwa tanthauzo la choonadi chomwe chilim'menemo. Iye amene anavumbulutsa zinsinsi izi kwa Yohane adzapatsa wofufuza mwakhama kulawa zinthu zakumwamba. Iwo amene mitima yawo ili yotseguka kuti alandire choonadi adzatha kumvetsetsa ziphunzitso zake, ndipo adzapatsidwa dalitso lolonjezedwa kwa iwo amene amva mawu a ulosiwu, ndi kusunga zinthu zonse zalembedwa mmenemo." - Acts of Apostles pp. 584, 585.

**b. Kodi Khristu amatiitana bwanji kuti tipeze moyo wosatha ndi mtendere kudzera mwa Iye? Chivumbulutso 22:17; Yesaya 55:1; Yohane 7:37, 38.**

"Kulira kwa Khristu kwa moyo wa ludzu kukupitirirabe, ndipo kukutidandaulira ife ndi mphamvu yayikulu ya kuposa iwo amene anayimva mu kachisi pa tsiku lomaliza la phwando. Kasupe watseguka kwa onse. Olema ndi othodwa apatsidwa mpweya wotsitsimutsa wa moyo wosatha. Yesu akuyitanabe, 'Ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine, namwe.'" - The Desire of Ages, p. 454.

## MAFUNSO OBWEREZA PAWEKHA

**Lachisanu n'chimodzi, Juni 26**

1. Kodi ndi motani mmene miliri ikubweretsera chimaliziro cha mbiri ya dziko lapansi?
2. Ndani adzayima pamene Khristu akadzabweranso?
3. Fotokozani cholinga cha chiweruzo mkati mwa zaka zikwi.
4. Kodi nyumba yomaliza ya oomboledwa idzakhala yotani?
5. Kodi ndikufuna ndi mtima wanga wonse kuzakhala gawo la ufumu wosatha wa Mulungu?

# Zopereka Za Sabata Loyamba



## Lasabata, Epulo 4, 2026

### Headquarters mu Filudi Ya ku Itale

Ndithawi yoti tikuze kufunikira kwa Likulu la chikoka mu Itale ku ulemerero wa Mulungu (Onani pa tsamba. 4)



## Lasabata, Meyi 2, 2026

### Zigawo Zofuna Thandizo Padzikolonse

Miyoyo ya mtengo wapatali ili mu mdima, yofunikira choonadi cha nthawi ino mwachangu kuti chipererkedwe kwa iyo lero—ndipo titha kuthandiza



## Lasabata, Juni 6, 2026

### Nyumba Yopempherera Ku Prague

Tiyeni tidzuke ndikumanTchalitchi ku ulemerero wa Mulungu mu mzinda wa mbiri yotchuka ya kukonzanso (Onani patsamba